


# MAFUNSO NDI MAYANKHO

 . . . ambiri amene ndikanawatenga, koma ine ndiri . . . Ine ndabweretsa konkodanse yanga. Ine ndikhoza kuipereka iyo kwa Leo pano, kapena winawake wakhala pafupi amene angandithandize ine ngati inu mukufuna kutero, ngati ife tingafike kwa iyo.

2 Tsopano, ngati dona uyu amene ali pamwamba apo, ngati pali . . . ngati iye anga . . . Ali kuti . . . Mwamuna wake ndi ndani? Eya. Chabwino, ngati mukufuna kuti mkazi wanu adzakhale ndi inu, iwo—iwo akhoza, palibe chimene chinanenedwa pakati pa abale koma chimene chinganenedwe kwa mlongo, nayenso. Ife basi . . . inu mukudziwa. Kodi izo—kodi izo ziri bwino? Tsopano, ndinu wolandiridwa kwambiri kukhala naye iye. Kodi—kodi iye wakhazikika kumeneko, Doc? Chabwino, izo ziri bwino, koma ndi zosungulumwa pang’ono kwa iye.

3 Ndipo palibe—palibe kanthu mkati muno . . . nthawizina chifukwa chimene ndimatchulira “mwamuna,” chifukwa ziripo nthawizina mwamuna akhoza kufunsa funso pakati pa amuna limene silingayankhidwe pamene pali akazi. Koma mulibe kalikonse mmenemo koma kamene kangayankhidwe konkuno mu mpingo wamba, chifukwa izo makamaka zikukhudza atumiki, ndi ena otero, ndi chimene kwawo—kutuma kwawo kuli ndi chimene iwo akuyenera kuchita.

4 Tsopano, ndikukhulupirira izi zikupita pa kujambula kwa tepi. Ngati . . . Sindiri wotsimikiza. M’bale Goad, ziri pati izo, kodi izo ziri pa kujambula kwa tepi tsopano? Chabwino. Chifukwa chimene ife timachitira izi ndi kuti tifufuze, abale, chimene chiri chenichenicho, chimene chiri—gawo, a . . . chimene chiri mmalingaliro a munthuyo, chiyani—zinthu zathu ndi chiyani.

5 Ife—ife tonse tikuyenera tiziyankhula chinthu chofanana. Tsopano, mwa chitsanzo, winawake abwera muno ndi, kudzati, mwinamwake iwo apita ku mpingo wa m’bale kuno, (dzina lanu loyamba ndi ndani, m’bale? Willard. M’bale . . . Tsopano, tiri ndi a Willard awiri pano, ndikuyenera ndikupatseni inu chinachakenso. Ngati ine . . . Dzina lanu lomaliza ndi ndani, tsopano? Crase) Mpingo wa M’bale Crase, ndipo M’bale Crase nkukanena chinthu chinachake. Ndiye iwo abwera kuchokera ku Sellersburg kupita kwa M’bale Ruddell, M’bale Ruddell nkukakhala zosiyana ndi zimenezo. Iwo nkupita kwa M’bale Junie, nkukakhala zosiyana, palimodzi. Kubwera kuno ku kachisi, ndipo zosiyanaabe. Mukuona? Izo zimawasokoneza anthu.

<sup>6</sup> Tsopano, monga winawake kudzati, “Oh, ine sindikukhulupirira kuti inu mungatero...inu mukuyenera kwenikweni kulandira Mzimu Woyera. Ine sindikuganiza kuti izo ndi zofunikira.” Kudzati, mwachitsanzo, M’bale Crase anganene zimenezo. Ndiyeno nkudzabwera uko kwa—kwa M’bale Ruddell, ndipo iye nkudzati, “Inde, izo ndizofunikira.” Ndipo kenako nkupita uko kwa Junie, ndi kukati, “Chabwino, izo sizimapanga kusiyana kwakukulu.” Mukuona? Ngati titakhala palimodzi ngakhale. . . Ine ndikanakonda tikanakhala ndi atumiki onse aku Jeffersonville (mu dera lino) titasonkhana pamodzi kuti ife tidzinena chinthu chofanana.

<sup>7</sup> Ndipo chotero, nthawi zambiri, madikoni ndi matrastii, iwo amayenera kuti apeze chimene ntchito yawo ili. Ndipo ine ndikuwona ife tiri ndi msungichuma wa tchalitchi ndi wosamalira pamalo pano usikuuno, kotero ife tipeza yomwe ntchito yawo ili. Koma mu zonsezi ndipo makamaka (kuno) ndi mafunso basi amene angafunsidwe kulikonse ndipo akhoza kuyankhidwa kulikonse. Ndi mafunso ophweka chabe, ndipo pokhala ngati ntchito za matrastii, ntchito za . . . Tsopano, ngati izo ziri ntchito zenizeni, ine ndikuganiza izo zinayikidwa pa bolodi komwe kuno tsopano, za ntchito za trastii ndi zimene amayenera kuti azichita. Koma ndinaganiza mwinamwake. . .

<sup>8</sup> Ndipo limodzi linabwera pamenepo, ndipo ndikuganiza kuti izo ziri bwino, ine ndiyankha ilo pakapita kanthawi, Ambuye akalola kuti ife tifiye kwa ilo, ndi:

**Mu vuto lina lake, kod dikoni akuyenera azichita chiyani? Iye ndi chiyani. . . Kodi ntchito yake yoti aziyichita ndi iti pamene vuto linalake lidzuka? Kodi iye azichita motani? Mukuona? Kapena trastii akuyenera azichita chiyani, kodi m’busa akuyenera azichita chiyani, chinachake chonga izo, pamene pabwera vuto? Ife timadziwa njira yachizolowezi, koma bwanji ngati chinachake chingachitike chimene chiri kunja kwa chizolowezi, mwaona, ndiye kodi iwo akuyenera kuti azichita chiyani?**

<sup>9</sup> Ndipo ife timangodziwa kumene tingagwere, izo ziri ngati kuphunzitsa asilikali, ndipo ife aliyense timadziwa malo athu. Tsopano, monga gulu ngati ili, ife tikhoza kukhala pano theka la usiku, ife tikudziwa zimenezo, koma ndi. . . ine sindikuganiza kuti izo ndi zofunikira. Ife tiyankha izo. Tsopano ndikufuna aliyense. . .

<sup>10</sup> Tsopano, palibepo maina, ena a iwo ali ndi maina, koma ine—ine sindingamatchule maina a anthu. Chifukwa basi—basi chirichonse chimene funsolo liri, ine ndizingowerenga funsolo. Pali pafupifupi awiri a iwo mmenemo amene ali ndi maina pa iwo. Ndipo, dikirani, ine mwina ndipeza lina. Ine ndikudziwa, ndi Dokotala Ingleman wokalamba, ine ndimayenera kuti ndimuyimbire iye uko ku—south wing, ku 4—426 south wing.

Ndi pamene dokotala wakale kumusi kuno kumene ife tinali lero, uko ku Georgetown, anachiritsidwa, kapena anabwera atakomoka kwa nthawi yayitali, ndi—ndi zina zotero. Tsopano, ine ndikuganiza izi zawapeza iwo, tsopano ife tilowa mu mafunso athu oyambirira amene ine ndinawawerenga poyamba.

Tsopano tiyeni tingoimirira miniti yokha, chonde.

<sup>11</sup> Atate athu Akumwamba, ife tasonkhana pano ngati gulu la amuna, amuna Achikristu amene amakukondani Inu, amene amakhulupirira mwa Inu, ndi amene tapereka miyoyo yathu ndi mautumiki ku utumiki Wanu. Pali atumiki pano, mnyamata, amuna a usinkhu wapakati, iwo ali ndi mipingo, iwo ndi oyankhira pamaso pa Mulungu. Pali madikoni pano amene ali oyankhira mu maudindo awo mmipingo yosiyanasiyana imeneyi. Pali matrastii, maudindo awo. Azibusa, avangeri, chirichonsecho, Ambuye, ndife oyankhira kwa Inu. Ndipo ndi chifukwa chake tabwera pamodzi, kuti ife tonse tikhoze kuyankhula chinthu chomwecho monga ife tinanenedwa kuti tikuyenera tizichita mu Lemba. Ife tonse tiyenera tiziyankhula mofanana.

<sup>12</sup> Ndipo Atate, ife tikuganiza, mu mtundu uwu wa gulu, kuti tikhoze kupeza mwinamwake ena a abale athu kapena ena a ife tingakhale ndi kutsemphana pang'ono pa zinthu, ndipo ena amangofunsa kuti adziwe kwenikweni Choonadi cha izo. Ndipo ife tikudziwa kuti ndife osakwanira, aliyense wa ife. Ngati nditati ndimufunse aliyense wa abale ena awa kuti abwere kuno ku mafunso awa, mwinamwake iwo akhoza kukhala okwanira basi kapena mochuluka kuposa momwe ine ndingawayankhire iwo. Koma palimodzi ife tikudalira pa vumbulutso Lanu, kuti Inu mukhoze kuwulula kwa ife kudzera mu Mawu ndi kudzera . . . mwa Mzimu Wanu, kuti izo . . . kuti ife tikhoze kukhala ndi yankho la funso lirilonse. Kutu mitima yathu . . . ife tikhoze kudzazidwa ndi mayankho ndipo ife tikhoza kuchokapo tikumverera kuti ife tinapatsidwa zida mwabwinoko ku utumiki Wanu ndi kutumikira udindo wathu kuposa—kuposa momwe tiriri tsopano. Ndicho cholinga chatu chokhalira pano, Atate. Perekani izi tsopano.

<sup>13</sup> Ndipo muyankhe mafunso athu, Atate, pamene ife tikuyembekezera pa Inu. Musalole kuti pakhale zododometsa mmalingaliro athu aliwonse, koma mulole ife tikhale ndi funso limenelo mpaka ilo litayankhidwa mokwanira ndipo ife nkukhutitsidwa ndi Mzimu, kuvomerezana mogwirizana chifukwa cha Kukhalapo Kwake. Ife tikupempha izi mu Dzina la Yesu. Amenii.

<sup>14</sup> Ine ndikungofuna kuti ndibwereze Lemba, kuti ndiyambirepo. Monga Yesaya ananena, mneneri anati:

*O bwerani. . . tiyeni tilingalire palimodzi, atero*  
*AMBUYE. . .*

<sup>15</sup> Ndipo ndikuganiza ndi chifukwa chake ife tiri pano usikuuno, ndi kuti tidzayesere kulingalira, kudzazilingalira zinthuzi. Ndipo tsopano ine ndingayambire...ndipo ndazilemba zinthu zinazo apa molingana ndi manambala ndi zina zotero, kuti ine ndinali ndi izi, M'bale Wood anali atagwira; ine ndiri ndi envelopu iyi ili ndi mayankho mmenemo. Ndipo tsopano ndikufuna aliyense wa inu, abale anga okondedwa, kuti mudziwe kuti—kuti mayankho awa a—amaperekedwa mwakudziwa kwanga kwapamwamba, zapamwamba kwambiri momwe ndikanadziwira kuzimvetsetsa kwake.

<sup>16</sup> Ndipo mayankho awa sali osalephera, mwaona, chifukwa Malemba ndiwo osalephera, ndipo monga momwe ine ndikudziwira iwo akugwirizana ndi Malemba. Ine ndikuyembekeza izo zikupanga izo kumveka. Ndipo tepiyo ikuyenera kusungidwa tsopano ndipo aliyense amene angaifune iyo, chabwino, iwo akhoza kudzakhala nayo iyo. Koma tsopano, ndikudziwa kuti Malemba ndi osalephera koma mayankho anga si osalephera. Chotero ine ndikutsimikiza kuti aliyense akumvetsa zimenezo. Ndipo ngati izo sichoncho—ngati iwo si osalephera, ndiye kuti muli ndi ufulu wodzandifunsa ine nthawi iliyonse.

<sup>17</sup> Ngati pali funso la winawake, ilo silikuyenera kukhala funso lanu, koma ngati ilo liri funso la winawake, mwinamwake inu simunaganizirepo za ilo, koma ndi chinachake chimene ife tiri pano kuti tithandizire. Ife tiri pano kuti—kuti tibwere pamodzi chifukwa tiri mmasiku otsiriza, ndipo masiku ndi oyipa, ndipo—ndipo ife tikufuna kuti tiphunzitsidwe, kuphunzitsidwa.

<sup>18</sup> M'bale Stricker, msilikali; M'bale Goad kumbuyo uko, msirikali; ndipo mwinamwake M'bale Ruddell pano, iye anali msirikali; M'bale Beeler; ndi osiyanasiyanawo amene—amene akhalapo mmoyo wa usirikali; inu mumakhala pamodzi, inu—inu mumalangizana, inu—inu mumaidziwa nkondoyo musanapite kunja kumeneko, ndi njomba zonse zimene mungathe za mdani, kuchitira kuti mukathe kukumana naye iye pa malo ake.

<sup>19</sup> Pamene ine ndinkamenya nkhonya, iwo ankamufufuza mdani wanga, chimene iye ati adzakhale, kamenyedwe kotani kamene iye ankagwiritsa ntchito, kaya kunali kumenyera mzwamba kapena chibagera chakumanzere kapena kudula ndi dzanja lake lamanja, ndiponso ngati iye anali wa dzanja lamanja kapena lamanzere, ndi momwe iye analiri wamphamvu, ndipo ngati iye ankasintha mapazi ake, ndi momwe ankagwiritsira ntchito maso ake, ndi ngodya imene amabwerera, ndi njomba zonse zosiyanasiyana zomwe tingathe. Ndipo iwo ankafufuza chimene...o—ophunzitsa anali atamuwonapo munthu ameneyo akumenya mmbuyomo. Kuchitira kuti amuyike munthu mmenemo ndi ine kuti azindiphunzitsa ine ndendende monga

momwe munthu ameneyo amamenyera, kuti—kuti ndidziwe chimene iye akanati adzachite.

<sup>20</sup> Ndipo ndicho chimene ife tadzera pano usikuuno. Ife tidziwe kumenya kwa mdani. Ife tidziwe chimene njomba zake ziri. Ndipo ife tiri pano usikuuno ndi Lemba kuti timuphimbe nalo iye kuti alephere kusuntha, chifukwa mdani ali mbali zonsezo.

<sup>21</sup> M'bale Roberson, ine ndimaganiza kumbuyo uko, pomuwona iye, iye ndithudi akuyenera kudziwa chimene msirikali amakhala. Iye ndithudi anali ndi nthawi ya izo! Ndi asirikali angati ali muno, tiyeni tiwone, amene akhala ali asirikali mu gulu la ankhondo? Tangoyang'anani apa, mwaona, gulu la asirikali inu. Chabwino, tsopano, inu mukudziwa chomwe izo ziri. Ndipo ndizo zimene inu mumaphunzira, si choncho izo, M'bale Roy, M'bale Beeler, ndi inu asirikali akale ndi ena otero? Ndi, kumuphunzira mdani, “Kodi iye adzachita chiyani? Kusuntha kwake ndi kotani?” ndipo kenako kudziwa momwe mungakumanirane naye iye.

<sup>22</sup> Ndipo ndicho chimene ife tadzera pano, kudzaphunzira kusuntha kwa mdani ndi—ndi kudziwa momwe tingakumanirane naye iye, chinthu chimene chiti chidzamugonjetse iye.

<sup>23</sup> Ndipo kumbukirani, mundirole ine ndinene izi, abale, mpingo wawung'ono unayamba pano pa mzere wa mphatso, mwaona, mphatso zikubwera mu mpingo. Koma kaya pali mphatso kapena ayi, ngati palibepo mphatso, ine ndikuuzani inu, mphatso nthawizonse siyingamugonjetse mdani, koma Mawu amatero. Mawu amakomana naye iye kulikonse.

<sup>24</sup> Ndipo Yesu, pamene Iye anali pa dziko lapansi, anatsimikizira zimenezo. Ake...Iye anali Mulungu akuwonetseredwa mu thupi. Koma Iye sanagwiritse ntchito iliyonse ya mphatso Zake zabwino kuti amumenyere nazo mdani. Ife tikupeza mu Mateyu...Ine ndikukhulupirira ndi mutu wa 2 kapena wa 3 wa Mateyu, Iye anati...Ayi, mutu wa 2 wa Mateyu, pamene Iye anakomana ndi mdani, Iye anakomana naye iye pa maziko a Mawu, “Kwalembedwa.”

Ndipo mdani anabwezanso, “Kwalembedwa.”

<sup>25</sup> Ndipo Iye anati, “Kwalembedwanso,” monga choncho, mpaka Iye anamumenya mdaniyo. Ndipo ndicho chimene ife tabwerera pano, ndiko kuti tidzakomane ndi mdani ndi zida zimene Mulungu anatipatsa ife—kuti tidzakumane naye nazo.

<sup>26</sup> Tsopano ndiri ndi mafunso pafupifupi foro apa amene ali pa...ali pa limodzi—ali pa chidutsa chimodzi cha pepala, ndipo ndinawapatsa iwo manambala: wani, thuu, firii, foro, faivi, sikisi, . . .eyiti, teni, ndi kumatsika monga choncho. Ndipo mwamsanga ndikathana ndi awa, ndiye ndilumphira mwa amenewo apo. Akuti:

**107. M'bale Branham, ngati mafunso awa ali kunja kwa mzere ndiye mungowasiya iwo, ndipo ine sindikhumudwa nazo izo chifukwa ndidziwa kuti silinali dzanja la Ambuye. Funso nambala wani: M'bale Branham, ine ndakumvani inu...kuti izo zikuyenera—zikuyenera kubwerera mu... Ine—ine—ine ndakumvani inu mukunena kuti ndikuyenera kubwereranso mu utumiki, ndipo ndaganizirapo pa izo inemwini, koma ndadikirira mawu ena otsimikizika ochokera kwa lye za izo. Mpaka pano iwo sanabwere. Tsopano, popeza ndikudziwa kuti mapeto ali pafupi kwambiri, kodi ndikuyenera ndizidikirirabe kuti Ambuye Yesu a—alankhule kwa ine? Kapena, kodi lye angasangalatsidwe kuti akuuzeni inu choti mudiuze ine, popeza ine ndikudziwa kuti inu ndi womuyankhulira Wake wa tsiku lino?**

<sup>27</sup> Chabwino, tsopano, m'bale, ine ndikana... Ine ndinalimba apa yankho langa kwa ilo. Mulungu akumuyitana m'bale uyu, kuyitana m'moyo, tsopano, pali chinthu chimodzi chachikulu chimene ife tingachitenge icho ngati mutu ndi kulalikira usiku wonse pa icho, mwaona, chinthu chimodzi chimenecho, "kuyitana." "Muzitsimikizira maitanidwe anu ndi kusankhidwa," mwaona. Ife sitikufuna kuti tizingodabwa ngati ndife oyitanidwa. Iwe ukuyenera kuyitanidwa kapena udzagonjetsedwa, ife tikumenya nkhondo. Mukuona? Ndipo ngati muli wotsimikiza, m'bale, kuti mayitanidwe anu ndi a Mulungu, ndipo inu mwaitanidwa ndi Mulungu kuti mudzaichite ntchitoyo...

<sup>28</sup> Tsopano, pali njomba yayikulu pamenepo imene mdani angasewere pa inu. Iye akhoza kukupangitsani inu kumaganiza kuti simunaitanidwe pamene munaitanidwa, kenako iye amatembenuka mozungulira ndikudzakupangitsani inu kumaganiza kuti simunaitanidwe; kapena kukupangitsani inu kuganiza kuti ndinu—inu munaitanidwa pamene inu simunaitanidwe; mosemphanitsa, mwanjira iliyonseyo. Ndipo inu mumayenera kusamalitsa izo.

<sup>29</sup> Tsopano, njira yake ndi iyi yochitira izo. Muziyamba mwafufuza... Chabwino, tsopano, ili ndi langizo, chinthu chokhacho chimene ine ndingapereke pa izi ndi langizo. Mukuona? Koma muzitsimikiza kuti maitanidwe anu akuchokera kwa Mulungu, ndipo kenako mufufuze zolinga zanu ndi zokhumba zanu. Mukuona? Tsopano, inu mukudziwa chimene ine ndikutanthauza ndi izo. Kodi cholinga chanu cholalikira ndi chiyani? Kodi icho chinali basi... Kodi inu mukuganiza kuti iyo inali ntchito yophweka kuposa imene inu muli nayo? Ndiye inu kulibwino muiwale zimenezo, izo sizinali kuitanidwa.

<sup>30</sup> Kuitana kwa Mulungu kumayaka kwambiri mu mtima mwako mpaka sungathe kupuma usana ndi usiku chifukwa

cha iko. Iwe sungachoke basi kwa iko, iko kumangokupera iwe mosalekeza.

<sup>31</sup> Ndipo—ndipo ngati ungati uzilalikira... Inu mukuti, chabwino, tsopano, cholinga china, “Ine ndikukhulupirira, pa ntchito imene ndiri nayo, ngati ndingakhale mvangeri wochita bwino kapena m’busa, kukhala ndi malipiro abwino, kukhala ndi nyumba imene ine ndikhoza kumapitako ndi zina zotero, ndi kumakhala, ndiye ine—ine ndikukhulupirira kuti icho chingakhale chinthu chabwino, chophwekerapo kuposa zomwe ndikuchita tsopano. Ndipo kwenikweni ine ndikuganiza izo zingakhale...” Tsopano, mwaona, cholinga chanu ndi cholakwika kuyamba ndi kuyamba. Mwaona, icho si cholondola. Mukuona? Inu—inu mukulakwitsa pamenepo pa izo.

<sup>32</sup> Kenako inu mungati, “Chabwino, mwinamwake chifukwa chakuti ine ndi a...ndikuganiza mwinamwake kuti ine ndingakhale wotchuka kwambiri pakati pa anthu.” Mwaona, inu mupeza kuti mwangokonzekera kugwa kwakukulu. Ndithudi, mwaona!

<sup>33</sup> Koma, tsopano, ngati cholinga chanu chikakhala chakuti “Ine sindikusamala ngati ine ndizidya chikondamoyo cha soda ndi kumamwa madzi a mngalande, ine ndizilalikira Uthenga mulimonse.” Chinachake chikung’amba mwa iwe, “Ine ndizilalikira Uthenga kapena kufa!” Mukuona? Ndiye iwe—iwe udzapita kwina kwake, chifukwa ndi Mulungu akuchita ndi iwe. Mulungu akuzidziwitsa Yekha kwa inu, chifukwa ndi Mulungu sangakuloleni inu kuti mupume. Ndipo, kawirikawiri, munthu woyitanidwa ndi Mulungu samafuna konse kuti azichita zimenezo. Kodi inu munayamba mwaganizapo za zimenezo? Munthu aliyense...

<sup>34</sup> Posachedwapa izo zinafunsidwa za ine ndi abale ena ofunika kwambiri, amene anati, “Tsopano popeza ife tabwera mu Njirayi, M’bale Branham, tsopano popeza ife tawapeza Ambuye ndipo talandira Mzimu Woyera, kodi tizifunafuna mphatso za utumiki wathu zomwe tiyenera kumachita.”

<sup>35</sup> Ine ndinati, “Musamachite konse zimenezo.” Mukuona? Musamawalangize konse anthu kuti azichita chinachake chonga chimenecho, chifukwa kawirikawiri munthu amene amafuna kuti achite izo ndi munthu amene—amene sangachite izo.

<sup>36</sup> Ndi munthu amene akuyesera kuthawa kwa izo ndi amene Mulungu amamugwiritsa ntchito. Mukuona? Ngati iye akuyesera kuthawa kwa izo, “Oh, m’bale, ine ndikukuuzani inu, ine...kuyitanako kuli mwa ine koma ine...Psyii! Amwene, ine ndimadana nazo kuti ndiyesere zimenezo.” Chabwino, ndi zimenezo pamenepo, inu mwaona. Uko—uko ndikuyesera kuthawa.

<sup>37</sup> Ngati iye—ngati iye akufuna kuchita izo kwambiri, chinthu choyamba inu mumadziwa iye amadzipeza yekha “wodzitukumula.” Monga iwe kumati, “Mulungu, Inu mundipatse ine mphamvu yosuntha mapiri, ine ndikukuuzani Inu, Ine ndikuchitirani Inu chinachake, Inu mundilole ine ndizisuntha mapiri.” Ayi, iye sangatero, iye sangakhoze nkomwe kudzisuntha yekha ku kachitidwe koyenera, mwaona, chotero sangamusunthire konse Mulungu mapiri.

<sup>38</sup> Mungotenga, mwachitsanzo, monga Paulo. Inu mukuganiza kuti Paulo akanachoka ku maitanidwe ake? Oh, m’bale! Iye sakanachita zimenezo. Izo zinkangomupera iye usana ndi usiku mpaka anasiya mpingo wake, iye anasiya chirichonse ndipo—ndipo anapita kumusi mu . . . ine ndikukhulupirira kuti kunali ku Asia, sichoncho izo? Ndipo anakakhala zaka zitatu kumusi uko, akuwerenga Malemba, kuti apeze ngati Iwo anali olondola kapena ayi, mwaona, kuti apeze ngati Mulungu anali atamuyitana iye kwenikweni.

<sup>39</sup> Chotero ngati Mulungu akukuitanani inu, m’bale, ndipo izo nkumangokukumbani mu mtima mwanu, ndiye ine ndingati “Siyani pambali cholemetza chirichonse, ndi tchimo limene silimachedwa kukufooketsani inu.” Inu mukuona? Ngati . . . Koma ngati izo sizikukudyani inu, ndiyeno ine—ine—ine sindingaganize mochuluka za izo ndiye. Mungolola izo zibwere pa malo ake.

Tsopano, iye anati, m’bale uyu ananena umu:

**M’bale Branham, kodi . . . Inu mukuganiza kuti Mulungu angayankhule . . .** (kwa ine kuti ndimuuze iye.)

<sup>40</sup> Ine ndikukhulupirira Mulungu akhoza kuyankhula molunjika kwa iye. Chifukwa, inu mukudziwa, Mulungu . . . Iye si aakulu kwambiri koma chimene Iye angalankhule kwa ife. Ndipo Iye—Iye—Iye adzayankhula nafe, chabwino. Mwaona, Iye basi . . . Iye adzayankhula nafe.

<sup>41</sup> Ndipo ndikukuuzani inu, ngati Iye akanandiuza ine, ndiye m’baleyo akanakhoza kunena, “Chabwino, Iye anamuuza M’bale Branham zimenezo, Mulungu alemekezeke!”

<sup>42</sup> Koma, inu mwaona, si M’bale Branham akukupatsani inu maitanidwewo, ndi Ambuye Yesu akukupatsani inu maitanidwewo. Mukuona? Ndipo ngati ndi Ambuye Yesu akukupatsani inu maitanidwewo, Iye azikachita kuyankhulako. Mukuona? Ine ndikhoza kuyankhula kwa inu m’makutu anu, koma pamene Khristu akuitanirani inu ku utumiki izo zimakhala mu mtima mwanu. Mukuona? Ndi pamene chinthucho chikuyenera kuzikika ndipo inu simungachoke kwa icho.

Tsopano, ine ndikukhulupirira pa funso lachiwiri . . .



43 Tsopano ngati pali funso lililonse pa izo, funso lililonse kwa izo, mwaona, kuti maitanidwe a munthu ayenera kukhala mu mtima mwake, kuchokera kwa Mulungu. Ndipo—ndipo m'bale wina . . . Oh, ine ndikumudziwa amene uyu ali yemwe analemba izi. Mwaona, ine ndikumudziwa amene analemba ilo, wofunika, wokonedwa, m'bale wachisomo amene ine ndikukhulupirira moona ali ndi maitanidwe a Mulungu. Koma ine basi . . . Ine sindikanafuna kuti iye achite zimenezo pa za ine (ndi chifukwa chake ndinayankha izo momwe ine ndinachitira), mwaona, pa ine kunena kuti; “Chabwino, inde, M'bale *Wakuti-ndi-wakuti* akuyenera kupita mu utumiki.” Mukuona?

44 Tsopano inu mukuti, “M'bale Branham anandiuza ine kuti ndikuyenera kuchita zimenezo.” Mwaona, ndipo mwinamwake nanga bwanji ngati chinachake chitachitika kwa M'bale Branham, ine nkuphedwa, kapena kufa, kapena—kapena kuchokapo? Ndiye, mwaona, kuitanidwa kwanuko kwatha ndiye. Koma ngati Yesu atakuitanani inu, m'bale, bola ngati kuli Muyaya izo zidzakhala zikulirabe momveka. Mukuona? Ndipo zikatero iwe umadziwa pamene ukuyima.

Tsopano pa lachiwiri . . .

45 Kapena chinachake chonga ichi, “Podziwa kuti ndi tsiku lotsiriza.” Ine ndithudi ndikuyamikira izo chifukwa cha m'bale ameneyo. Ine ndithudi ndikuyamikira izo za m'bale ameneyo pozindikira kuti ife tiri mu tsiku lotsiriza, ndi kuwonamtima kwa mtima wake, akufuna kumuchitira Khristu chinachake.

Lotsatira ndi:

**108. Tsopano, ngati Ambuye wathu wofunika angandilore ine kuti ndimuchitire Iye kanthu kakang'ono, kodi ndibwererenso ku madera kumene ndinatumikirako kwa pang'ono mu . . . molakwitsa (zomwe ine ndikupepesa) . . . iye wayika izo mu zikutiro . . . ndi kukayesera kuti ndikawauze iwo Choonadi? Izo zakhala chomwecho—izo zakhala chomwecho pa mtima wanga.**

46 Ayi, m'bale, sindingaganize kuti zinali zoyenera kuti inu mubwererenso ku dera lomwelo. Ndipo ndikukhulupirira, m'bale wokonedwa, pamene Ambuye akuitanani inu Iye mwina sangakuloleni kuti muzipita monga momwe munkachitira mu deralo, ndipo mwinamwake munkaphunzitsa zinthu kapena munali ndi zinthu zimene sizinali . . . zimene kwenikweni mukuziona mosiyana tsopano, mwaona, kuti inu mukhoza kuziwona mosiyana ndi momwe munkachitira nthawi imeneyo. Tsopano, ndipo Ambuye, pamene Iye anakuitanani inu, Iye akhoza . . . ngati Iye apanga icho chenicheni kwa inu, Iye akhoza kukutumizani inu kulikonse. Mukuona? Inu simuyenera kupita kudera lina lililonse kapena china chirichonse.

47 Pamene inu munali kumeneko inu munali woonamtima. Ine ndikumudziwa m'baleyo, monga ine ndikunenera, amene

walembe mafunso awa. Ndi kuzama kwa kuwonamtima, ndipo Mkhristu weniweni, inu munkachita mopambana momwe inu mukanakhoza kuchitira ndipo ndi zonse zimene inu munkadziwa kuzichita, ndipo ndizo zonse zimene Mulungu amafuna. Mukuona? Tsopano, ngati Mulungu angakuyitanireni inu kuti mubwerere ku dera limenelo, ine ndingabwerere kachiwiri. Koma ngati Iye sanatero, ine—ine ndikukhulupirira ine ndikanangopita kulikonse kumene Iye wanditumiza ine. Kodi pali funso?

Nambala firii:

### **109. Kodi wina amadziwa bwanji malo ake oyenera mu Thupi la Khristu?**

<sup>48</sup> Limenelo ndi labwino, labwino kwambiri, “Ndi motani. . .” Ilo lingakhale mtundu wa funso pakati pa ambiri a ife pano usikuuno, “Kodi inu mumadziwa bwanji molondola?” Tsopano, ndikupenekera kuti m’bale uyu akufuna kuti adziwe “Ndi udindo wanji, *wanji* mwa Khristu, ndi gawo lanji la Khristu limene ine ndikulichita?”

<sup>49</sup> Tsopano, mwa chitsanzo, ine ndinganene monga chonchi, m’bale, kuti ndikupatseni inu yankho lopambana lomwe ine ndikulidziwa. Udindo wanu ndi. . .mwa Khristu umaululidwa kwa inu ndi Mzimu Woyera. Ndiyeno ngati mukufuna kudziwa ngati uli Mzimu Woyera kapena ayi, mufufuze ngati Iye akudalitsa chimene inu mukuchitacho, kapena ayi. Ndipo ngati Iye akudalitsa icho, ndiye ndi Iyeyo. Ngati Iye sakuchidalitsa. . .

<sup>50</sup> Monga winawake ananena kwa ine osati kale kwambiri, anati, “Ambuye anandiitana ine kuti ndizilalikira.”

Ine ndinati, “Chabwino, ndiye zilalikirani.” Mukuona? Ndipo chotero iye—iye. . .

<sup>51</sup> Ine ndikuganzizi kuti izo ziri. . .Satana, ngati iye angakhoze kumupangitsa winawake kuti—kuti azichita monga choncho ndipo kenako nkuwanyenga iwo, ndizo basi zimene iye amafuna kumachita. Kenako dziko lonse limaloza chala chawo pamenepo. Wina amaganiza kuti ali ndi mphatso yoyankhula mu malirime ndi kutanthauzira; ena ali ndi mphatso ya machiritso Auzimu; ena ali ndi zinthu izi monga. . .Nthawizina iwo amalakwitsa mu zinthu zimenezo, mwaona. Ndipo nthawizina iwo amaganiza kuti alibe iwo pamene iwo ali nazo. Chotero izo ndi zanjomba kwambiri.

<sup>52</sup> Chotero nthawizonse inu muzichita zimenezi, abale, nthawi iliyonse imene inu mukumverera kuti mukuyenera kuchita chinthu, choyamba muzifufuza ngati icho chiri Mwamalemba kuti inu muchite chimenecho (ngati izo ziri Mmalemba). Osati kungolembedwa pamalo amodzi, koma ndikutanthauza Mwamalemba kwathunthu kudzera mu Baibulo kuti inu muchite zimenezo, udindo wanu, kunena ngati mungakhale mvangeri, m’busa, mphunzitsi, mneneri, chirichonse chimene

Mulungu angakuitanireniko inu kuti mukhale. Inu mukuona? Kapena ngati inu muli ndi mphatso ya malirime, mphatso yotanthauzira, mphatso ya uliwonse—mtundu uliwonse wa mphatso faivi zauzimu mu mpingo, ndipo maudindo foro auzimu a mpingo, udindo uliwonse, choyamba muwone ngati Mulungu wayitana.

<sup>53</sup> Kenako, kawirikawiri, momwe ine ndimawonera zimenezo ndekha, basi...uyu ndi ineyo, ine ndimaona chikhalidwe cha munthuyo ndi kuwona mtundu wa mphatso imene iwo akudzinenera. Mwaona, Mulungu amagwira ntchito ndi cholengedwa Chake momwe Iye anamupangira iye. Mukuona? Iye amapanga cholengedwa . . .

<sup>54</sup> Ngati inu mumuwona iye ali wosadalirika kwenikweni ndi kumapitirira, inu...ndipo nkumati, “Ambuye anandiyitanira ine *chakuti-ndi-chakuti*, kuti ndikakhale m’busa.” Tsopano, m’busa sangakhale munthu wosadalirika. M’busa amakhala wokhazikika, woyamikika. Mukuona?

<sup>55</sup> “Mulungu anandiitana ine kuti ndidzakhale mphunzitsi.” Ndipo mumuwone iye momwe amatanthauzira Mawu. Mukuona? Iye amangowasokoneza Iwo zonse ndi chirichonse, ndiye inu mukhoza kudziwa. Mukuona?

<sup>56</sup> Koma, ndiye, chinthu choti muzichita, malo anu kawirikawiri amadziwika ngati inu mungathe kuchita izo kapena ayi.

<sup>57</sup> Tsopano, pamene Mulungu anandiitana ine kuti ndidzakhale mvangeri, ine ndinkafuna kuti ndidzakhale m’busa. Ndipo ndinkaganiza kuti kukhala pakwathu pano zikanakhala zabwino basi. Ndipo Ambuye anandiitana ine. Ndipo potsiriza anthu onse anasonkhana pamodzi...Palibe mmodzi wa iwo amene watsala usikuuno muno, amene anafuula ndipo anapita kunja uko pa 1717 Spring Street. Ndipo donayo, Akazi a Hawkins cha kuno, anakomana nane ndipo anati (akulira, mu nthawi ya kupsyinjika, pamene wina koyandikana nyumba ankaphika nyemba ndipo ife tonse tinkabwera kudzadya kuchokera pamene), ndipo iye anati, “Ine ndidzapereka ana anga patebulo ngati inu mutangomanga kachisi.” Mukuona?

<sup>58</sup> Ndipo maitanidwe anga anali mvangeri. M’mawa... Ziri pomwepa pa mwalawapangodya uwu, ngati titagumula pamenepo usikuuno, inu muwona tsamba lothotholedwa kuchokera mu Baibulo langa pamene Iye anandiuza ine kuti ndikhale mvangeri. Mukuona? Ndipo ine sindinali m’busa wochita bwino, sindidzakhala, chifukwa ine ndiribe chipiriro ndi zomwe zimatengera kuti ukhale m’busa. Mukuona? Chotero chomwecho ngati nditayesera kuchita ubusa, ine ndidzangokhala kutali monga m’busa pomayesera kuti ndikhale mvangeri.

59 Mukuona chimene ine ndikutanthauza? Iwe ukhoza kuwona momwe Ambuye akukuitanira iwe, chimene malo ako ali mu Thupi. Kodi pali funso?

**110. Kodi anthu onse odzazidwa ndi Mzimu Woyera amayankhula ndi malirime posakhalitsa kapena mtsogolo?**

60 Limenelo ndi funso loyamba, “Kodi onse a Mzimu Woyera...” Ndiye, onsewo ali mu funso limodzi, ine ndiri nazo apa pa funso la nambala foro. Koma ine ndi—ine ndinena izi poyamba, inu mwaona:

**Kodi anthu onse a Mzimu Woyera amayankhula ndi malirime posakhalitsa kapena mtsogolo? Ine ndikupeza pamene Paulo ananena kuti iye “analankhula ndi malirime ochuluka kuposa iwo onse.”**

Chabwino, funso nambala foro: **Kodi onse amayankhula ndi malirime pamene akulandira a...Kapena, ayi, ilo linati: Kodi onse amayankhula ndi malirime...Ayi: Kodi anthu onse odzazidwa ndi Mzimu Woyera amayankhula ndi malirime posakhalitsa kapena mtsogolo?**

61 Tsopano, m’bale, ine...Ili ndi funso lakuya. Tsopano, apo, inu mwinamwake...Mwina ine ndikhala ndi mayankho pa ili.

62 Mzimu Woyera, gawo la Mzimu Woyera ndi kulungamitsidwa. Pamenepo ndi pamene inu poyamba... Mulungu amayenera kukuitana iwe kapena sudzaitanidwa konse. Mwaona, palibe chimene ungachite mwa iwe wekha. “Palibe munthu angabwere kwa Ine pokhapokha Atate Anga atamukoka iye poyamba.” Nkulondola uko? Koteru gawo la kulungamitsidwa ndi Mzimu Woyera.

63 Kodi inu munandinvapo ine ndikufotokoza kwa mkulu wa Chilutera uja nthawi ija za munda wa chimanga? Mwaona, “Chimanga, munthu anapita ndipo anakabzala chiwiri... anakabzala munda wake wa chimanga. M’wawa wotsatira iye atapita ndipo ‘kunalibe kanthu.’ Patapita kanthawi iye anapeza masamba awiri aang’ono akutulukira, iye anati, ‘Mulungu alemekezeke chifukwa cha munda wanga wa chimanga!’” Ndipo ine ndinati, “Kodi iye anali ndi munda wa chimanga?”

Ndipo mkulu wa Chilutera anati, “Mwakuyankhula kwina.”

64 Ine ndinati, “Uko nkulondola, mwakuyankhula kwina iye anali nawo.” Koma ine ndinati, “Mwa...” Ine ndinati, “Ameneyo anali inu Achilutera.”

65 “Pang’ono ndi pang’ono mphukirayo zinakula ndipo zinafika ku ngayaye. Ameneyo anali Methodist. Gawo lachiwiri la chimanga, ndi ngayaye.” (Ine ndikuganiza uko nkulondola, inu abale ochokera ku munda.) “Ndipo kenako ngayaye inayang’ana pansu ku tsambalo ndipo inati, ‘Huh! Ndine ngayaye, iwe ndi tsamba chabe! Mwaona, ine sindikukufunanso iwe.’ Ndipo kenako ngayaye...Unga umagwa kuchokera ku

ngayaye, kubwerera mu tsamba kachiwiri; umayenera kukhala ndi tsamba.”

<sup>66</sup> “Ndipo kenako kuchokera pamenepo mumatuluka khutu. Iyo inali Pentekoste, kubwezeretsa kwa mphatso monga zinapita pamalo oyamba, kubwerera ku chiyambi. Kenako pamene khutu linatulukira, linati, ‘Ine sindikukufuna iwe, ngayaye. Kapenanso sindikukufuna iwe, tsamba.’”

<sup>67</sup> Koma, pambuyo pa zonse, moyo womwewo umene unali mu—tsamba la chimanga unapanga ngayaye. Ndipo zimene zinali mu tsamba ndi ngayaye zinapanga njere. Chotero Mzimu Woyera kuyankhula mmalirime ndi chiyani? Ndi kulungamitsidwa kwapamwamba. Mukuona? Kodi mpingo wa Pentekoste ndi chiyani? Chilutera chapamwamba. Mukuona?

<sup>68</sup> Koma tsopano pamene kupita patsogolo kwafika, funso lingakhale ili, “Ndiye ine ndingokhala?” Ayi! Ayi, chimanga chakhwima. Mukuona? Inu mumayamba ndi njere. Kuyamba ndi a—Mawu, njere, Iwo adzabala kulungamitsidwa. Ndipo kukhala mu kulungamitsidwa mpaka Iwo atabala kuyeretsedwa. Kukhala mu kuyeretsedwa mpaka inu mutalandira Mzimu Woyera.

<sup>69</sup> Tsopano pamene mulandira Mzimu Woyera, kodi Iwo udzachita chiyani? Ndi chiyani...Mukanali ndi funso, sichoncho inu? Chabwino:

### **111. Kodi “kuyankhula ndi malirime ndi chiyani”?**

<sup>70</sup> Kuyankhula ndi malirime si kanthu koma ubatizo wa Mzimu Woyera umene unakulungamitsani inu ndi kukuyeretsani inu. Iwo ndi wodzazidwa! Tsopano, ine ndimafuna... Ndimalifuna funso ili. Mulungu akudziwa kuti ine sindimadziwa nkomwe kuti bamboyu afunsa, ayankha... kapena afunsa ilo.

<sup>71</sup> Tsopano, kodi izo nazonso... ngati mungatenthe kwambiri muno, mutsegule chitsekocho ngati muyambe kutsinza kapena chinachake. Ine ndikufuna kuti muzimvetsetse izi mwabwino ndi mokhazikika. Chifukwa mwa—mwatentha kwenikweni pang’ono, izo zingakupangitseni inu kutsinza.

<sup>72</sup> Tsopano zindikirani, zindikirani izi: kulungamitsidwa, kuyeretsedwa, ubatizo wa Mzimu Woyera.

<sup>73</sup> Tsopano taonani apa, ndi izi apa. Ndiroleni ine ndifotokoze izo. Tsopano, ine ndiri kumusi kuno, ndine wochimwa, ine ndikuyenda njira *iyi*. Kamodzi, patapita kanthawi, Chinachake chikuyankhula ndi ine. Ndipo palibe chimene chinganditembenuze ine koma Mulungu. Nkulondola uko? Ine ndinapotolokera mbali *iyi*. Tsopano, pamene ndinapotoloka, uko ndi kulungamitsidwa kwanga. Nkulondola uko? Tsopano, chithunzicho ndicho cholinga changa chopitirako, mwaona, chithunzi cha Khristu.

<sup>74</sup> Tsopano ine ndikufuna pa malo pamene ine ndingamverere bwino pozungulira Iye. Mwaona, ine ndalungamitsidwa. Tsopano ine ndafika pa siteji iyi *apa* pamene ine ndikhoza kuyankhula naye Iye, chifukwa . . . Ine ndikuzichitirabe manyazi ndekha. Ine ndimasutabe, ine ndimanamabe, ndachita zinthu zazing'ono zomwe sindimayenera kuchita, ndipo nthawi zonse *zokwera* ndi *zotsika* zanga, *zokwera* ndi *zotsika*, koma ine ndikufuna Iye andiyeretse ine ku zinthu zonsezo kuti ine ndikhoze kuyenda kwenikweni kukafika kwa Iye ndi kuyankhula naye Iye. Mukuona? Chabwino, ndi izi apa, ndi kuyere- . . . siteji ya kuyeretsewa. Tsopano, kodi izo zinachita chiyani? Zinandiwongola ine. Mukuona?

<sup>75</sup> Tsopano ine ndikupitirira ku Mzimu Woyera. Mukuona? Ndipo pamene ine ndidzafika *umu* ine ndiri mu Mzimu Woyera mwa ubatizo. Nkulondola uko? Kodi Mzimu Woyera umachita chiyani? Iwo umandipatsa ine mphamvu. Mphamvu yokhala mlaliki, mphamvu yokhala woyimba, mphamvu yolankhula ndi malirime, mphamvu yotanthauzira malirime. Iwo ndi wodzaza ndi mphamvu, pakuti Mzimu Woyera ndi mphamvu ya Mulungu. Ndipo inali mphamvu ya Mulungu imene inanditambenuza ine. Inali mphamvu ya Mulungu imene inandiyeretse ine. Tsopano ndi mphamvu ya Mulungu imene inandidzaza ine.

<sup>76</sup> Tsopano, pa chochitika chinachake, ine ndayima pano ndipo ine ndikuyesetsa kuti ndinene chinachake ndipo Mphamvu ya Mulungu imabwera pa ine mwanjira yayikulu chomwecho mpaka ine sindimatha basi kuyankhula mopitiriranso. Mukuona? Ndipo ndinayamba kuchita chibwibwi. Ngati ndimati ndinene, “Abale,” munga kuyimira chonchi.

<sup>77</sup> Ndi izi apa, ndifotokoza izo mwanjira iyi. Ndiyankhula ndi inu abale kuti mutsimikizire kuti mwamvetsetsa zimenezo. “Bwanji—bwanji—in u muli bwanji m'bale?” Mwaona, ine ndidakali wolakwa. “Uh, ine—ndine wokondwa kuti ine—kuti ine ndidakali mmodzi wa inu. Ine—ine—ndine wokondwa kwambiri, inu mwaona.” Chabwino. Tsopano, patapita kanthawi, chiyani? Ine ndikudziwa kuti inu mukuyang'ana molunjika pa ine ndipo mukudziwa kuti ndikuchitabe zinthu, ndikuchitabe zinthu zimene ziri ndi zonyansa zapadziko lapansi.

<sup>78</sup> Pakapita kanthawi ine ndimatsukidwa. Tsopano chinachake chinachitika, ine ndinayeretsedwa. Ndikhoza kukuyang'anani inu pamaso, ndine mmodzi wa inu. Mukuona? “Chabwino, m'bale. Mulungu alemenzeke! Ndine wokondwa kukhala mu gulu la Mzimu Woyera ili. Ndine wokondwa kukhala pakati pa inu abale oyera.” Bwanji? Simungayike chala chanu pa ine, ine ndayeretsedwa. Koma tsopano Mulungu andiyika ine mu utumiki. Tsopano, inde, bwana!

<sup>79</sup> “M'bale Branham, kodi inu munalungamitsidwa?”

80 “Inde! Ine ndikukumbukira pamene sindinkatha nkomwe kukuyang’anani inu. M’bale, ine ndikhoza kukuyang’anani inu pankhope tsopano.”

81 Mwaona, ndi ife pano. Tsopano, chinachi ndi chiyani? Tsopano ine ndiku. . . *Ichi* chatsukidwa ndi kuyikidwa pambali *ku* utumiki, ndipo *ichi* chikubwera *mu* utumiki. Tsopano ife tonse tikudziwa kuti liwu loti *kuyeretsa* ndi liwu la Chigriki, liwu lapawiri la Chigriki limene limatanthauza “kuyeretsedwa, ndi kuyikidwa pambali *ku* utumiki.” Ziwiyazo zinatsukidwa ndiponso pafupi ndi guwa, ndi kuyeretsedwa ndi guwa, ndi kuyikidwa pambali *ku* utumiki. Koma kukhala *mu* utumiki ndi kudzazidwa ndi kuyikidwa *mu* utumiki.

82 Tsopano, ine ndikupita cha kuno ndipo tsopano ine ndikubwera *mu* utumiki. Tsopano, anali Mulungu amene ananditembenuza ine, anati, “Tandimvera Ine. Tandimvera Ine! Tandimvera Ine!” Ndipo Iye anati. . .

83 Inu mukumvetsa chimene ine ndikutanthauza? Mukuona? Ndipo apa, [M’bale Branham akuwonetsera winawake akuyankhula mmalirime—Mkonzi.] . . . ? . . . Mwaona, apa, inu mwangokhuta kwambiri. . . Ndi zimenezotu. Ndi inu pamenepo, kumeneko ndi kuyankhula mmalirime.

84 Ndipo ine ndikukhulupirira izi tsopano: ine sindimakhulupirira kuti kuyankhula mmalirime ndi umboni uliwonse wa Mzimu Woyera. Iwo siuli! Chifukwa ndawonapo afiti aakazi, afiti aamuna, ogwira njoka, adierekezi, china chirichonse akuyankhula mmalirime, ndipo uko si machitidwe osalephera a Mulungu (pamene muyankhula mmalirime) kuti inu muli ndi Mzimu Woyera. Koma, kumbukirani, Mzimu Woyera umayankhula mmalirime ndipo mdierekezi akhoza kutsanzira izo.

85 A—umboni wakuti muli ndi Mzimu Woyera ndi moyo umene inu mumakhala, onani, “Ndi zipatso zawo inu mudzawadziwa iwo.” Ndipo chipatso cha Mzimu si (palibe paliponse mu Lemba mungapezepo) kuyankhula mmalirime. Chipatso cha Mzimu ndi chikondi, chimwemwe, chikhulupiriro, kuleza mtima, ubwino, kufatsa, kudekha, chipiriro. Mwaona, tsopano, icho ndi chipatso. Izo ndi zimene mmazipeza pa mtengo kuti mudziwe mtundu wa mtengo umene iwo uli. Mukuona?

86 Ndicho chimene amuna amayang’ana kwa inu alaliki, ndi kwa inu madikoni, ndi inu matrastii, ndi inu avangeri. Inu mukhoza kuyankhula mmalirime kunja kuno pa msewu uwu tsiku lonse, iwo sangakukhulupirireni inu nkomwe. Koma inu mumakhala moyo ndi zimene mukuzikamba, inu mumawonetsera kukoma, ndipo mizu yonse yakuwawidwa yatuluka mwa inu, ndiye munthu adzazindikira kuti pali chinachake.

<sup>87</sup> “Kuyankhula mmalirime.” Tsopano, ine ndimakhulupirira izi, kuti nthawi ina, kuti munthu wodzazidwa-Mzimu amene amakhala pansu pa guwa la Mulungu adzayankhula ndi malirime. Koma ine ndawonapo ambiri akuyankhula ndi malirime amene sankadziwa kalikonse za Mulungu. Mukuona? Iwo sankadziwa kanthu za Iye nkomwe, ndipo iwo amayankhulabe ndi malirime. Iliyonse ya mphatso zimenezo ikhoza kutsanziridwa. Mukuona?

<sup>88</sup> Koma chipatso cha Mzimu chimatsimikizira chimene Mzimu uli mkatimo, inu mumachitira umboni Moyo wa Yesu Khristu. Chifukwa ngati muli utomoni wa mtengo wa mapichesoni mu mtengo wa apulo, iwo udzabala mapichesoni motsimikiza monga dziko. Uko nkulondola. Mwaona, chifukwa ndi moyo umene uli mkati mwakemo.

<sup>89</sup> Tsopano, ndicho chinthu chomwecho chimene chiri apa. Koma tsopano, kuti ine ndikhoze kufikitsa izi kwa inu nonse, kuti ife tonse tidziwe chinthu chomwecho. Ine ndimakhulupirira kuti munthu wodzazidwa-Mzimu amene... Tsopano iye amabwera mwa Khristu mwa ubatizo, ndipo basi... uko si... Kuyankhula ndi malirime si umboni wa ubatizo. Mukuona?

<sup>90</sup> Ubatizo, iwe ukhoza kubatizidwa mu mphamvu ya mdierekezi, ndipo nkumayankhula mmalirime ndi ubatizo wa mzimu wonyenga wa mdierekezi. Kodi ife taziwona izo zikuchitika kangati? Kodi kangati kamene ine ndaziwona izo zikuchitika?

<sup>91</sup> Ine ndinadziwa ngakhale za iwo akumwa magazi kuchokera mu chigaza cha munthu ndi kumayankhula mmalirime.

<sup>92</sup> Ine ndinawawona ovina-njoka mchipululu pamene anadzikulunga njoka yaikulu iyi mowazungulira iwo ndi kumapitirira kuyankhula. Mfiti inatulukira monga choncho, ndipo iwo amakhoza kuyankhula mmalirime ndi kuwathanthauzira iwo.

<sup>93</sup> Ine ndakhalapo mmisasa yawo ya afiti kumene iwo amakhoza kuyika pensulo pansu monga choncho, ndi kuyika bukhu pansu monga chonchi, ndipo pensulo nkumathamanga chokwera ndi chotsika mu paipi, ndi kumayimba, “*Shave and a haircut, two bits,*” ndi kumalemba mmalirime osadziwika, ndipo mfiti nkumathanthauzira izo ndi kumanena ndendende zomwe zinachitika. Ine—ine ndikuzidziwa izo inemwini. Mukuona? Chotero ine... Mwaona, inu simungathe... .

<sup>94</sup> Paulo anati, “Kumene kuli malirime, iwo adzasiya. Kumene kuli maulosi, iwo adzalephera. Kumene mphatso zonsezi, izo zidzathetsedwa posachedwapa.” (Tiri ndi funso patsogolo pang’ono.) “Koma pamene icho chimene chiri changwiro chidzabwera, chimene chiri mwa gawo chidzathetsedwa.” Mukuona? Chotero ife tikufuna chinthu changwirocho, abale.



Mukuona? Ife tawona zinthu zambiri zabodza ndi kupereka kutanthauzira kolakwika kwa izo.

<sup>95</sup> Ndipo musadzakumane konse ndi munthu ndi—ndi kukhulupirira kuti iwo ali nawo Mzimu Woyera chifukwa iwo amayankhula mu malirime. Mukuona? Koma inu muzikhulupirira kuti iwo ali ndi Mzimu Woyera chifukwa cha zipatso zimene iwo akubala, pakuti Yesu anati, “Ndi zipatso zawo inu mudzawadziwa iwo.” Mukuona? Uko nkulondola, “Ndi zipatso zawo.”

<sup>96</sup> Tsopano, koma tsopano, ndiroleni ine ndisachoke kwa izo tsopano, chifukwa sindikufuna kunyozetsa mphatso yayikulu imene Mulungu wayipereka. Mukuona? Ndipo ndimakhulupirira kuti mwamuna kapena mkazi wodzazidwa ndi Mzimu, kapena mwana, amene amakhala pansu pa guwa la Mulungu, sangakhale pamene motalika mpaka iwo adzakhala akuyankhula ndi malirime. Mukuona? Ine ndikukhulupirira kuti mwamunayo adzachita zimenezo, kapena mkaziyo.

<sup>97</sup> Tsopano, inu mukhoza kulandira Mzimu Woyera ndipo mwinamwake inu simunayankhule ndi malirime pamene mumalandira Iwo. Mukuona? Koma ngati mowirikiza mungakhale pamene pamaso pa Mulungu nthawi zonse, ndi ubatizo pamwamba pa ubatizo ukukukhudzani inu, chinachake chidzachitika. Mukuona? Inu muzadzadzidwa kwambiri tsikulina mpaka inu simudzatha kuyankhula china chirichonse; mwaona, inu—inu—inu mudzayesera kunena chinachake, inu simudzatha basi kuchinena icho kenanso, ndipo basi simudzatha kuchinena icho. Ndipo nthawi zambiri ngati anthu akanazindikira kuti umenewo unali Mzimu Woyera iwo akanapitirira ndi kungotsegula mtima wawo ndi kumulola Mulungu kuti alankhule kwa iwo.

<sup>98</sup> Baibulo linati, “Ndi milomo yachibwibwi ndipo ndi malirime ena ndidzayankhula kwa anthu awa.” Yesaya 28, onani, 28:18. Tsopano, “Ndi milomo yachibwibwi ndi malirime ena ndidzayankhula.”

<sup>99</sup> Kodi ndi chiyani “chibwibwi”? Winawake amene sangathe kuyankhula bwinobwino, amati, “Huh, uh, uh, huh, uh, huh, uh, huh.” Inu basi . . . iwe umachita chibwibwi, kumangoyesera, “Huh, uh, huh.” Mwaona, basi odzazidwa ndi Mzimu! Iye akuyesetsa kuti anene . . . Monga ndimati ndinene, “M’bale Ja-Jack- . . . Ja- . . . M’bale Jack- . . . M’bale Ja-Ja-Jack-Jack-Jackson.” Mwaona, izo monga choncho, iwe ukuyesera kuti unene, ukulephera kunena izo. Mwaona, ndiko, kudzazidwa kwambiri ndi Mzimu! Iwo . . .

<sup>100</sup> Ndikufuna ndikufunsemi inu abale, kodi inu munayamba mwawumvererapo Mzimu Woyera ukukugwedezani inu kwambiri mpaka inu osatha nkomwe kunena kalikonse, munangokhala chete kwa kanthawi, kungokhala pamene

ndi kumalira? Kodi inu munachitapo zimenezo? Chabwino, umenewo ndi Mzimu Woyera. Ngati mungatero... Chifukwa chimene anthu samayankhula ndi malirime nthawi zambiri, iwo samadziwa momwe angaziperekere okha kwa Mzimu ndipo iwo amayang'ana chinachake kutali pamene Iwo uli pa iwo pomwe. Mukuona? Ndi chifukwa chake iwo sama...

<sup>101</sup> Ndiyeno anthu ena amangodzizikweza okha mu kutengeka ndi kunena mulu wa mawu opanda tanthauzo kwa izo, ndipo komabe alibe Mzimu Woyera, ndi kumayesera kunena kuti iwo ali nawo chifukwa iwo anayankhula mmalirime. “Ndi zipatso zawo inu mudzawadziwa iwo,” mwaona.

<sup>102</sup> Tsopano, kodi pali funso? [M'bale Junior Jackson akuti, “M'bale Branham?”—Mkonzi]. Inde, m'bale. [“Ndine wokondwa kuti funso limenelo linafunsidwa, chifukwa mosakayikira ena angadabwe chimene mwinamwake ine ndakhulupirira ndi kuphunzitsa kwa nthawi yayitali. Koma ine ndimakhulupirira izo monga momwe inu mwaphunzitsira izo.”] Zikomo inu, M'bale Jackson. [“Mosalabadira kuti ndi mochuluka bwanji ine ndingathe kuyankhula mmalirime, kapena chirichonse, ngati moyo wanga sukuchitira umboni chimene Baibulo limanena ndiye ine siwabwinoko kuposa galu wovuta akuyenda mu msewu.”] Uko nkulondola. [“Ndipo ine sindinayankhule chinenero chosadziwika mpaka miyezi sikisi kuchokera pamene ndinalandira ubatizo wanga.”] Umo ndi momwe ine ndinachitira izo, inenso, M'bale Jackson.

<sup>103</sup> Ine ndinalandira ubatizo wa Mzimu Woyera kuseri mu chisakasa changa, mwaona. Ndipo pafupifupi chaka kenako, kapena chinachake chonga choncho, ine ndinali—ine ndinali... ndinayankhula mmalirime.

<sup>104</sup> Ndipo pafupifupi chaka kapena ziwiri zitachitika zimenezo, ine ndinali kulalikiranso mu mpingo, ndipo ndinali—ine ndinali nditayima pa nsanja monga chonchi, ndipo ine... Pamene ndinali wamng'ono ndipo sindinali wouma ndi wokalamba monga momwe ndiriri tsopano, ndinkatha kumayendayenda mwabwinoko ndipo ndinkatengeka kwambiri polalikira. Ine ndinali nditayima pamenepo ndikulalikira ndipo ine ndinangodumphira pa desiki. Zinali mu mpingo wa Baptisti, mpingo wa Baptist waku Milltown, ndipo ndinapita mpaka mkanjira, ndikulalikira mwamphamvu basi monga ine ndikanati ndilalikire monga choncho. Ndipo nditangosiya kulalikira, Chinachake chinangonditenga ine ndi kunena mawu angapo, foro kapena faivi, kapena mawu sikisi, mmalirime osadziwika. Ndipo ndisanadziwe chimene ndinkachita, ine ndinadzimva ndekha ndikuyitana “Thanthwe mu dziko lotopetsa, Pobisalirapo mu nthawi ya nkuntho.” Mukuona?

<sup>105</sup> Ndiyeno tsiku lina ndikutsika mu njanji, ndinkayenda mu njanji, mbali iyi ya Scottsburg, ndikubwera mu njanji,

ndikulondera. Mphepo zikuwomba mwamphamvu, oh, mai, ndipo chisanu ponseponse mkanjira, ndipo ndinawoloka kuti ndithe kuyenda chotsika sarte-firii sauzande yanga; sikisite-sikisi anapita mmwamba njira yinayo, kukhala ngati molingana ndi kanjirako. Ndipo ndinkabwera chotsika mkanjirako, ndipo zonse mwadzidzidzi. . . Ine ndinkayenda motsatira pamenepo, ine ndinali ndikuimba. Ine nthawizonse ndinkayimba. Ndinali ndi malo osiyanasiyana kumene ndinkapita kukapemphera. Ndipo ine ndinkapita kumeneko, ndikuyimba, ndipo zonse mwakamodzi ine ndinadzapeza kuti ine ndinkayankhula mmalirime, mwaona, osadziwa chimene ine ndinkachita.

<sup>106</sup> Kuyankhula mmalirime kumabwera mu kuyaka kotero mpaka munthuyo samadziwa nkomwe chimene iwo akuchita, kapena, iwo samadziwa chimene iwo akunena. Ndipo kutanthauzira ndi chimodzimodzi. Iwo samadziwa chimene ati anene. Iwo alibe lingaliro linanso kuti iwo anene izo, chifukwa ndi zauzimu. Mwaona, pokhapokha ngati iwe ungapaze chachibadwa mmenemo ndiye iwe suma. . . iwe—iwe—iwe umakhala mwachibadwa, inu mwaona. Koma ngati chinachake chingokugwirani inu ndi kukugwirani inu, ndipo inu mukuchita icho. Mukuona?

<sup>107</sup> [M'bale Neville akuti, "M'bale Branham, kodi ine ndinganene chinachake pomwe apa?"—Mkonzi]. Ndithudi, inu mukhoza, M'bale Neville. ["Tsopano, iwe ukunena izo mwanjira imeneyo, iwe sukulinga kuti unene, ngakhale, kuti—kuti malirime amenewo ayenera kukhala mu dongosolo mu msonkhano ngati munthu sangathe kuwalamulira iwo? Chifukwa iye ali. . . Munthu amene ali ndi mphatso amayenera kuti azilamulira iyo."] Iye akhoza kudzilamulira yekha. Inde. Monga ngati. . . ["Iwe ukuyenera kukhala wozindikira mokwanira kumadziwa kuti iye ali pafupi kuti ayankhule mmalirime"] eya, uko nkulondola ["kapena iye sali mu dongosolo kuyamba ndi kuyamba."] Uko nkulondola, iye amamverera izo. Mukuona? Tsopano, monga Baibulo linanena, "Ngati—ngati pali wina amene amayankhula mmalirime ndipo palibe womasulira, ndiye muloleni iye akhale chete." Tsopano, ndithudi.

<sup>108</sup> Titi, mwachitsanzo, ine ndayima pano, aliyense, pamene inu mukukonzekera kufuula, chinthu chomwecho. Kodi inu munayamba mwamvererapo mphamvu ya Mulungu ikubwera pa inu pamene inu munayamba kufuula? Ndi angati anayamba achitapo zimenezo? Chabwino, tonse ife tateropo. Mukuona? Iwe umangokhala pamenepo, iwe umamverera izo zikubwera. Tsopano, zimakhalapo nthawi pamene iwe ukhoza kuzimitsa zimenezo, mwaona. Iwe ukhoza kuzigwira izo, mwaona, izo sizabwino.

<sup>109</sup> Bwanji ngati inu mukanayima, kumayankhulana ndi a—Purezidenti wa United States, kapena munayima kunja kuno

mukuyankhula ndi meya wa mzinda, ndipo inu mumayankhula za chinachake chimzake, panja pa msewu apa, mukuyankhula ndi gulu la anthu, ndipo zonse mwakamodzi iwe umangomverera ngati ukhoza kulumpha chokwera ndi chotsika, ndi kumakuwa ndi kufuula “Ulemelero! Aleluya!” ndi kukankha motsutsa chirichonse ndi kumathamanga chokwera ndi chotsika mu msewu monga choncho. Iwo anganene kuti wapenga. Mukuona? Iwo angati, “Munthu ameneyo ndi wopenga.” Mukuona?

<sup>110</sup> Chabwino, mwaona, inu mukudziwa bwinoko kuposa kutero ndiye. Iwe umadzigwira, ngakhale izo zikungokukumba mwa iwe ndipo sungazigwire nkomwe izo. Inu mukuti, “Inde, bwana. Inde, bwana. Uh-huh. Uh-huh. Eya. Inde, bwana. Uh-huh.” Mnyamata, iye akungokukumba iwe mzdutswa koma umadziwa kudzigwira bata nthawi yomweyo. Mukuona?

<sup>111</sup> Monga mu kothi kuno osati kale, iwo anali ndi Achipentekoste ena—chifukwa chochita chinachake chimzake, kukuwa mokweza kwambiri kapena chinachake, chimene iwo anali—iwo anali ovomerezeka mwamtheradi, inu mukuona, ndi kulondola. Koma nthawi iliyonse woweruza akapita kukayankhula kapena akapita kuti akanene chinachake kwa iwo, iwo amayankhula mmalirime. Mukuona? Woweruza anati, “Achotseni anthu opengawo pano.” Mukuona?

<sup>112</sup> Tsopano, ngati pakanakhala kutanthauzira kwa malirime amenewo ndi kumuwuza woweruza “PAKUTI ATERO AMBUYE,” chinthu *chakuti-chakuti* chimene chikanakhala choona, “PAKUTI ATERO AMBUYE! Woweruza, inu mwaimiranji pano kumandiweruza ine pamene usiku wathawu munali ndi hule? Dzina lake linali Sally Jones, iye amakhala kumusi ku 44 malo *Akuti-akuti-akuti*, monga choncho. Inu mukundiweruza ine chifukwa chiyani? Ndizo PAKUTI ATERO AMBUYE! Tsopano kanani zimenezo ndipo inu mugwa ndikufa.” Tsopano, oh, m’bale! Pali chinachake chosiyana pamenepo.

<sup>113</sup> Koma pamene mungoyima ndi kumayankhula, ndipo iye anati, “Ndiwe wachilendo kwa iwo.” Inu mukuona? Tsopano, iwe umadziwa nthawi yoti ukhale bata ndi nthawi yoti usachite izo. Mukuona? Tsopano, ndizo... Mwaona. Ndine... Inu mundimvetse ine tsopano, inu mukudziwa chimene ine ndikutanthauza. Mukuona? Ndiko kuti. Ndithudi. . .

<sup>114</sup> Ife tiri nalo funso limenelo pansu apa. Chifukwa chimene ine ndinaligwira monga chonchi, ife tiri ndi chinthu chomwecho, “Kodi iwo akuyenera kukhala bata?” Inu mukuona? Chimenecho ndi chifukwa ine sindinayankhe ilo mochuluka kuposa zomwe inu mumanena. Koma nthawi yake ndi imeneyo, yankhani ilo tsopano, mwaona, pakali pano. Ndipo tizitenganso izo pa funso ili pansu apa, ndipo ine ndidzangolozera mmbuyo kwa ilo. Kodi aliyense akumvetsetsa funso limenelo bwino bwino?

[M'bale Fred akufunsa, **“M'bale Branham?”**—Mkonzi].  
Inde, M'bale Fred. [**“Kodi—munthu amayankhula mu—mu  
Mzimu, nkumapereka kuyankhulako (tinene kuti iye ndi  
Mzungu ndipo amatha kuyankhula Chingerezi) ndipo kodi  
Mzimu ungapereke kuyankhulako?”**]

<sup>115</sup> Ndithudi. Inde, bwana. Mwaona, chifukwa Mzimu Woyera umayankhula mu chinenero chirichonse. Mukuona? Pa Tsiku la Pentekoste chinenero chirichonse cha pansu pa Kumwamba chinasonkhana pamodzi, mwaona. Kuyankhula mu Chingerezi. . . Tsopano, ine nthawizonse ndimadziwa zimenezi, M'bale Freddie, inemwini, kuti ine. . . ngati ine ndinalalikirako ulaliki umene muli kudzoza kulikonse kwa iwo, ndi Mzimu umapereka kuyankhulako, inu mwaona. Iwo ndi. . . Mukuona? Chotero izo zikhoza kukhala lirime losadziwika kwa munthu amene samamva Chingerezi. Komabe. . .

<sup>116</sup> Ndipo monga lirime losadziwika ilo si “losadziwika” lirimelo, ilo ndi. . . pali winawake pamenepo. . . Monga pa Tsiku la Pentekoste, iwo anati, ochimwa onse awa, iwo anati, “Ife tikumumva bwanji munthu aliyense mu chinenero chathu? Kodi ife *tikumumva* bwanji Agalileya awa akuyankhula mu chinenero chathu?” Panalibe “osadziwika” za izo konse. Palibe chinthu choterocho ngati malirime “osadziwika” pa Pentekoste. Tsopano, onani, zimenezo si Mwamalemba nkomwe. Mukuona? Panalibe osadziwika. . . ilo silinali lirime losadziwika, icho chinali chinenero. “Kodi ife tikumumva bwanji munthu aliyense mu chinenero chathu chimene ife tinabadwamo?” Palibe chosadziwika cha izo nkomwe. Mukuona? Kuti. . . funso lililonse pa izo tsopano, pakali pano ife tisanalisiye ilo? “Kodi ife tikumumva bwanji munthu aliyense mu chinenero chathu chomwe?” Mukuona?

<sup>117</sup> [M'bale akuti, “Pamenepo—pamenepo ndi pamene pali kulakwitsa pang'ono chifukwa cha kufooka kwa umunthu, ndipo pamene anthu adza—adzalephera kuvomereza chirichonse, kungoti, “Sindingakhulupirire izo mwanjira ina iliyonse, kokha molingana ndi Machitidwe 2:4.”—Mkonzi]. Chabwino, ngati iwo anali nazo molingana ndi Machitidwe 2:4 iwo ndithudi sakanayankhula mu lirime losadziwika. [“Ayi, mu chinenero.”] Uh-huh. Iwo akanayankhula mu—mu chinenero chimene anthu amakumvani inu, mwaona, chifukwa “munthu aliyense ankamva mu chinenero chake chomwe.”

<sup>118</sup> Tsopano, ngati ine ndingalandire Mzimu Woyera pakali pano, molingana ndi. . . Ine ndikunena. . . Ine ndikukhulupirira pali m'bale mmodzi pano amene akufuna Mzimu Woyera, amene ndi—ndi—ndi M'bale Wood. Nkulondola uko, M'bale Wood? Ine sindikutanthauza kuti ndikutchuleni inu, koma zonse. . . ndife abale chabe pano ndipo tikufuna kunena izi. Ndipo iye akufuna ubatizo wa Mzimu Woyera. Tsopano, ngati M'bale Banks analandira Mzimu Woyera pamenepo, njira yolondola,

ngati iye analandira Iwo molingana ndi Baibulo, iye akhoza kuimirira pamenepo, kuyankhula iwo, iye akhoza kuyankhula iwo mu Chingerezi, ndi kuti, “Yesu Khristu Mwana wa Mulungu wauka,” iye amayankhula izo ndi ulosi wamoto umene umanena izo. “Ine ndikudziwa kuti Iye ali, chifukwa Iye wangobwera mu mtima mwanga. Iye ndi Mwana wa Mulungu! Machimo anga apita, pali chinachake chachitika kwa ine.” Mukuona? Ndi zimenezotu. Kumeneko ndi kuyankhula mu. . .

“Bwanji tikumumva ife munthu aliyense mu chinenero chathu chomwe?”

<sup>119</sup> Kumati, bwanji ngati ife anthu aku Indiana tikanamayankhula chinenero chosiyana ndi anthu aku Kentucky, ndipo M’bale Banks ndi waku Kentucky? Ndipo iwo ankayankhula chinenero chosiyana ndiye, ndipo apa ife tikudziwa kuti iye sakakhoza kuyankhula chinenero cha ku Indiana. Ndiyeno iye anaimirira pamenepo nkumayankhula mu—mu chinenero cha ku Indiana, ndipo kudziwa kuti iye samachidziwa icho. Mukuona? Ndipo ife tikumumva iye mu chinenero cha ku Indiana, iye akuganiza kuti akuyankhula chinenero cha ku Kentucky. Iye akungochitira umboni, “Mulungu alemenzeke! Yesu wauka kwa akufa. Aleluya!” koma ife tikumumva iye mu chinenero chaku Indiana.

<sup>120</sup> Umo ndi momwe zinaliri pa Tsiku la Pentekoste. Mukuona? “Kodi ife tikumumva bwanji munthu aliyense,” taonani, “taonani, kodi onsewa amene akuyankhula si Agalileya,” mwaona, aku Kentucky? “Ndipo zikutheka bwanji kuti ife aku Indiana, Ohio, ndi Illinois, ndi Maine, ndi Massachusetts, ndi California, tikumumva iye mu chinenero chathu chomwe chimene tinabadwa nacho?” Mukumvetsa lingaliro? Mwaona, ndi kud zodza. Mwaona, ndi kud zodza kwa iwo kuti amve, ndi kud zodza kwa iwo.

<sup>121</sup> Mwaona, uthenga. . . chinthu chake ndi, ndi umboni wa chiwukitsiro cha Yesu Khristu. Mwaona, nkulondola kumeneko. Tsopano, ngati Mulungu sakhala Moyo umenewo mwa inu, ziribe kanthu kuchuluka kwa momwe mungachitire umboni za Iwo, inu simunawupezebe Iwo. Mukuona? Uko nkulondola. Mwabwino momwe inu. . .

<sup>122</sup> Kodi pali funso lina tsopano? [M’bale Roy Roberson akuti, “Chabwino, M’bale Branham, ine ndikuganiza kuti ife tinaziwona izo zikuchitika mu mzere wa pemphero, mtsikana wachi Spanish uja.”—Mkonzi]. Inde. Zabwino kwambiri, M’bale Roy. Uko kunali ku—kumene ine ndikupita tsopano, ku Beaumont—Beaumont. Kodi kunali ku Beaumont? Inde, bwana.

<sup>123</sup> Tsopano, mzere wa pemphero unaimitsidwa. Panali mtsikana wamng’ono wachi Spanish amene anabwera pa nsanja. Chabwino, moonana, ine ndikukhulupirira kuti ndinkatuluka panja, sichoncho izo? Howard anali akunditengera ine panja,

ndipo—ndi uyu. . . Ine—ine—ine ndinamva wina akulira, anali mtsikana wamng’ono wachi Spanish pamenepo, oh, pafupifupi fifitini, usinkhu wa zaka sikisitini, kulondola . . . mwana chabe. Ndipo—ndipo ine ndinayang’ana, ndipo iye akanakhala khadi la pemphero lotsatira ngati ine ndikanati ndipitirire patsogolo. Ine ndinali ndi angapo pamenepo, iye akanakhala khadi lotsatira la pemphero. Ine ndinati, “Mubweretseni iye.” Chotero iwo anamubweretsa iye pamwamba. Ine ndimapita ku msonkhano wina, ndipo ndinati, “Mubweretseni iye kuno.”

<sup>124</sup> Chotero, ine ndinadzapeza kuti, ine ndinamuuzza iye chinachake chonga ichi, “Tsopano, kodi iwe ukukhulupirira? Ngati Yesu angandithandize ine kuti ndikuuze iwe chomwe chiri cholakwika ndi iwe, iwe ukhulupirira kuti—kuti Iye akuchiza iwe?” Ndipo iye anangoyika mutu wake pansi. Ine ndinaganiza iye ayenera kuti ndi wogontha ndi wosayankhula. Mukuona?

<sup>125</sup> Chotero pamene ine ndinadzayang’ananso, ine ndinati, “Ayi, kungoti iye sangathe kuyankhula Chingerezi.” Chotero iwo anapeza wotanthauzira kuti abwere kumeneko, ndipo ine ndinati, “Kodi iwe ukhulupirira?” Ndipo iye anayankha cholozu. . . Ndiye iye amamva kudzera mwa wotanthauzira, ndithudi. Mukuona?

<sup>126</sup> Chabwino, kenako ine ndinati. . . Ndipo ine ndinayang’ana ndipo ine ndinawona masomphenya. Ine ndinati, “Ine ndikukuwona iwe utakhala pafupi ndi poyatsira moto pachikale ndipo ketulo yayikulu ikugwedera, yodzaza ndi ngala za chimanga chachikasu. Inu o- . . .” Inu mukukumbukira zimenezo, M’bale Roy? Ine ndinati, “Iwe unadyetsa chimanga chimenecho. Ndipo pamene unatero, iwe unadwalika kwambiri ndipo amayi ako anakuyika pa bedi ndipo unayamba kugwa khunyu.” Ndipo ine ndinati, “Iwe wakhala nazo izo kuyambira pamenepo.”

<sup>127</sup> Ndipo kenako iye anatembenukira kwa wotanthauzira ndipo anati kwa iye mu chinenero chake chomwe, “Ine ndimaganiza kuti iye samatha kuyankhula Chingerezi. . . kapena kuyankhula chi Spanish!”

<sup>128</sup> Ndipo iye anatembenukira kwa ine ndipo anati, “Inu simunayankhule Chispanish, inu munatero?”

<sup>129</sup> Ine ndinati, “Ayi.” Chotero ife tinayang’ana pa chojambulira, tinaimitsa zojambulirazo, icho chinali mwamtheradi Chingerezi.

<sup>130</sup> Komano wotanthauzirayo anati, “Iwe undiuze zimene wanena ndiye.” Mwaona, iye ankayenera kuti apeze kutanthauzira. Anati, “Iwe undiuze ine zimene wanena.” Ndipo iye ananena mawu omwewo kwa iye, ndipo iye anawanenanso kachiwiri.

<sup>131</sup> Tsopano, iye anandimva ine mu chinenero chake chomwe chimene iye anabadwiramo, ndipo ine ndimayankhula Chingerezi. Iye anamva izo mu Chispanish. “Ife tikumumva

bwanji munthu aliyense mu chinenero chathu chomwe chimene ife tinabadwa nacho?” Ndipo mwanayo anachiritsidwa. Mwaona, ndi zimenezotu, ndi ntchito zodabwitsa za Mulungu.

[M’bale akufunsa, “**Ndiye chotengera chimene chiri ndi Mzimu Woyera sichidza... chidzangokhala chotengera, ndipo Amene amachidzazitsa icho akhoza kuchidzazitsa ndi chimene Iye...?**”—Mkonzi].

<sup>132</sup> Chirichonse chimene Iye akhumba, ndiko kulondola. Kulondola ndendende. Ndiyeno muwone chimene icho chadzazidwa nacho, ndiye inu mudziwa ngati inu muli ndi Mzimu Woyera kapena ayi, ndiye. Mukuona? Mungowona chimene icho chadzazidwa nacho. Ngati a—ngati chotengeracho chadzazidwa ndi zonyansa, ndiye icho sichotengera cha Mulungu. Koma icho chadzazidwa ndi zoyera, ndiye ndi chotengera cha Mulungu. Mukuona chimene ine ndikutanthauza? [M’baleyo akuti, “Ndipo chotengeracho, zimakhhalapo nthawi zomwe chotengeracho chidzagwiritsidwa ntchito ndipo osadziwika, osadziwika panthawiyi chimene, kuti chimagwiritsidwa ntchito?”—Mkonzi]. Oh, ndithudi. [M’bale akupereka umboni.] Uh-huh. Uh-huh. Ndiko kulondola ndendende, ndithudi. Oh, ife tonse, ife timaziwona zimenezo. Ine ndaziwonapo izo nthawi zambiri. Inde, bwana. Inde, bwana. Ife tonse... Tikudziwa kuti timazidziwa zinthu zimenezo.

Ine ndikukhulupirira kuti ilo linali nambala foro: **Kodi onse—kodi anthu onse odzazidwa ndi Mzimu Woyera amayankhula ndi malirime posachedwa kapena mtsogolo? Ine ndikupeza pamene Paulo anati, “Ine ndimayankhula ndi malirime ochuluka kuposa—kuposa iwo onse.”**

Tsopano, chimene ine ndikuganiza tsopano, kuti ndimalizitse funso la m’baleyu:

**Paulo, akuyankhula ndi malirime ochuluka kuposa onse.**

<sup>133</sup> Paulo anali munthu wanzeru, iye ankadziwa zinenero zambiri, iyemwini. Mwaona, iye ankatha kuyankhula ndi... iye... Kumbukirani pamene iye anali pa mlandu, iye ankatha kuyankhula ndi lirime la mtundu uwu kapena lirime la mtundu uwo, kapena chirichonse chimene icho chinali. Ndipo amenewo ndi malirime osadziwika kwa anthu, koma izo sizinali zodzoza. Izo zinali zinenero zoyankhula, inu mwaona. Koma... ndipo...

<sup>134</sup> Koma ine ndimakhulupirira kuti munthu wodzazidwa ndi Mzimu amene amakhala moyo pansu pa guwa la Mulungu, mosakayika, posachedwa kapena mtsogolo, adzakhala ndi chimuchitikira cha kuyankhula mmalirime, chifukwa chimenecho ndi chimodzi mwa zinthu zotsikitsitsa ndi zazing’ono zimene ziripo malingana ndi kulongosola kwa Paulo. Ngati inu mungaziike izo mu dongosolo, ndi chinthu chomalizira pa mzere wa mpatso, mwaona, ndi kuyankhula ndi malirime.



<sup>135</sup> Koma tsopano, choyamba, inu mumabatizidwa... Apa, ali yense wa inu ndi mphatso. Ine ndiri kunjira. Tsopano, “Pa Khomo limodzi, Mzimu umodzi,” khomo limodzi likulowa mchipinda *ichi*. Nkulondola uko? Tsopano, ine sindingathe kubwera mwanjira *imeneyo*, sindingathe kubwera mwanjira *iyi* ndi kubwerera njira *iyoyi*. Mukuona? Ine ndimalowamo bwanji *muno*? Mwa M’bale Roberson? Ayi, bwana. Mwa, chabwino, titi, M’bale Leo? Kuti iye akhoza kukhala mphatso ya kuyankhula mmalirime, mwaona, kodi ine ndimalowa mwa Leo? Ayi, bwana. Huh-uh. Chabwino, ndimalowamo bwanji? “Mwa Khomo limodzi, mwa Mzimu umodzi.” Mzimu si malirime onse. Ayi. Mukuona? Onani, “Mwa Mzimu umodzi ine ndimabatizidwa kulowa mu Thupi ili.”

<sup>136</sup> Tsopano, *uwu* ndi Mzimu, *inu* nonse ndinu mphatso. Inu mukuti, “Chabwino, adalitsidwe Mulungu!” Ine ndipita uko ndipo, ndikati, pali—pali M’bale Wood, iye ndi zozizwitsa. Mukuona? “Oh, ine ndinapanga chozizwitsa. Ine ndikudziwa kuti ndiri ndi Mzimu Woyera chifukwa ine ndinachita chozizwitsa.” Osati mwa “chozizwitsa” chimodzi ife tonse timabatizidwa kulowa mu Thupi.

<sup>137</sup> Pitani kwa M’bale Junie ndiye, iye ndi chidziwitso, “Chabwino, chabwino, ine ndiri ndi chidziwitso cha Baibulo! Mnyamata, ine ndikukuuza iwe, ine ndikudziwa ndiri ndi Mzimu Woyera chifukwa cha zimenezo.” Ayi, njira yake yolowera si imeneyo.

<sup>138</sup> Chabwino. Osati mwa M’bale Leo, osati mwa M’bale Wood, osati—osati mwa M’bale Junie. Mukuona? Ayi. Koma mwa umodzi chiyani? [Osonkhana akuti, “Mzimu!”—Mkonzi]. Chabwino. Ine ndimabatizidwira kulowa mu Thupi ili, tsopano ine sindiri mwa ilo, tsopano kodi Atate andigwiritsa ntchito ine pati? Mukuona? Izo zinachitika kuti Leo anali atakhala pafupi ndi khomo; mosakayikira ichi chikanakhala chimodzi mwa zinthu zoyambirira kuchitika. Koma izo mwina sizingakhale. Ine ndikhoza kukhala wolemera kwambiri mu Mzimu, mpaka ine ndikhoza kupita mpaka kuno kwa M’bale Wood, kulambalala zina zonsezo. Inu simungandiuze ine tsopano kuti ine ndiribe Mzimu Woyera, chifukwa ndiri mu Thupi ili mwa ubatizo. Koma Mulungu sanandibweretse ine kuno kuti ndidzanene, “Chabwino, Mulungu adalitsike, ndikuganiza ine ndikhala panso tsopano, nditenge ‘zophweka, ine ndikupita Kumwamba.’” Huh! Mukuona chimene ine ndikutanthauza?

<sup>139</sup> Koma ine ndikhoza kubwerera mmbuyo kuchokera apa, mmbuyo mpaka uko. Mukuona chimene ine ndikutanthauza? Ine ndikhoza kuchoka ku mapeto ena kupita ku ena, kapena ine ndikhoza kupita pakati, kapena kulikonseko. Koma chinachake chidzachitika, chinachake chikuyenera kuchitika. Ndipo icho ndi chiyani? Mwa ubatizo wa Mzimu umandiwonetsa ine kuti

ndiri mu Thupi, “Mwa Mzimu umodzi.” Inu mukumvetsa zimenezo, m’bale, apa? Chabwino! Ndi zimenezotu? Chabwino.

**112. Ndi dongosolo liti limene malirime ndi maulosi akuyenera kugwiritsidwa ntchito** (Kodi iwo sakuyenera kugwiritsidwa ntchito nkomwe pa nthawi ya msonkhano! Mukuona?) **kulemekeza Mulungu** (Ayi nkomwe!), **ndi kumangiriza mpingo? Ine ndikudziwa anthu amanena kuti mzimu wa mneneri—ine ndikudziwa—ine—ine ndikudziwa...** (p...Ine ndikuganiza zimenezo... Ayi, ndikupempha chikhululukiro chanu, izo zakhala ziri “Baibulo,” B-a-i-b-u-l-o. Ine ndinayamba p-e-p-l-e kapena chinachake chonga icho. Ayi.) **a—Baibulo limati, “Mzimu wa aneneri umamumvera mneneriyo.”** (Ndendende.)

<sup>140</sup> Kuyankhula mwauzimu mmalirime ndi kulosera ndi kumangiriza mpingo, koma izo ziri ndi utumiki wake wake. Mukuona? Izo sizoti zizitisokoneza bola ngati mneneri wa mpingo ali...msonkhano uli mu dongosolo. Mukuona? Izo sizoti zizisokoneza msonkhano.

<sup>141</sup> Tsopano, onani, “mizimu ya aneneri.” Ife—ife tiri ndi funso lina tsopano, tiyeni tilole izo zipite kwa miniti yokha. Mwaona, njira yolondola yeniyeni ya izi...kugwiritsa ntchito mphatso izi...Uku ndi kuyankhira mphatso zambiri, inu mwaona. Pamene tidzafike kwa iwo tidzati tinayankha ilo mu loyamba ili, munthu uyu pa ili apa. Mukuona? Limenelo ndi nambala faivi:

**Kodi malirime ndi maulosi akuyenera kugwiritsidwa ntchito pa misonkhano kuti alemekeze Mulungu?**

<sup>142</sup> Inu mwaona, tsopano, mtumiki...ngati mtumikiyo wadzozedwa ndi Mulungu, ndipo mpingo wakhazikitsidwa mu dongosolo, tsopano, njira yolondola... Ambiri a inu mukudziwa momwe ine—ine ndayankhulapo nanu za “kuzikhazikitsa izo mu dongosolo.” Mphatso izi zimayenera...Tsopano, izi ndi zomwe ife tizichita mu kachisi, Ambuye akalola. Tsopano, ine ndikupenyetsetsa, ine ndikuwona chinachake, kumusiya M’bale Neville ndi abale ena awa apa mu dongosolo. Tsopano ndinu... Ndipo pamene ambiri a abale awa ndi abale achinyamata.

<sup>143</sup> Tsopano, ine—ndine msirikali wakale kwa—kwa inu nonse mu Njira iyi. Ndakhala zaka sarte-wani mu Ichi. Zinali pafupifupi zaka sarte zapitazo ine ndinayika mwala umenewo apo. Ndimayenera kukumana ndi chirichonse chimene ndimayenera kukumana nacho, ndipo iwe kulibwino uzidziwa zomwe ukukamba, iwenso, pamene ufika kwa izo. Iwe kulibwino kuti usamangodziwa izo, kulibwino pakhale Mulungu pamenepo kuti adzayikire kumbuyo pamene iwe udzafika—pamene udzatsirizitsa izo.

<sup>144</sup> Tsopano, njira yopambana kwambiri yo—yochitira izi tsopano, mukhoza kukhala ndi msonkhano wapadera. Ine

ndikukhulupirira izo ndi zimene iwo anachita mu Akorinto Woyamba 14 pamenepo, “Chinachake chikuwululidwa kwa mmodzi wakhala chapafupi, musiye winayo akhale chete ndiye.” Ine ndikukhulupirira izo zinali “msonkhano wapadera wa mphatso,” zomwe zingakhale zabwino. Ngati iwo akufuna kukhala ndi msonkhano wapadera kumene anthu onse a mphatso azikumana kamodzi pa sabata, iwo amene ali ndi mphatso, ndi kubwera mu tchalitchi, izo zingakhale zabwino. Asiyeni iwo akhale ndi msonkhano umenewo, palibepo... pasakhale kulalikirira, ndi wa mphatso za Mzimu.

145 Izo si za anthu akunja ndi osakhulupirira. Iwo angabwere, kudzakhala pansu, kunena... Mmodzi kudzuka ndi kuti, “ah-ah,” kuyankhula mmalirime; winayo nkuti, “wha-ah.” “Ndi chiyani m’dziko!” Iwo angabwere ndi kudzati, “Kodi kuyimba kuli kuti? Zina zonse za izo ziri kuti?” Mukuona?

146 Koma, tsopano, awa amene akuyankhula mmalirime, ambiri a iwo (ndi kutanthauzira, ndi zina zotero) ndi makanda mu Uthenga. Mukuona? Musati—musamawakhumudwitse iwo, muziwasiya iwo—muziwasiya iwo azikula kufikira mphatso imeneyo... Zina mwa izo, inu mukhoza kuwona mmene Satana amayesera kulowa mu zina. Chifukwa, akale, ife—ife—ife timaziwona zimenezo. Mwaona, ife tikhoza kuzigwira zimenezo, ndipo mudzaziwona izo.

147 Kuno osati kale kwambiri mtumiki wina, wakhala pomwe pano tsopano, anabwera kwa ine ndipo anandiuza ine ndipo ananditengera ine kunyumba kwake, m’bale wofunika kwambiri.

148 Ine sindikunena izo chifukwa iye wakhala pano, koma ndinu nonse abale *ofunika*. Ngati ndikanati sindikuganiza chomwecho, ine ndikanakuuzani inu, “Tiyeni inu ndi ine tiwongole chinthu ichi pakati pathu, poyamba.” Mukuona? Uko nkulondola. Mukuona? Ine ndimakukondani inu nonse, ndipo ine ndiri pano kokha mu mzimu wa kulolerana kwa Baibulo, inu mwaona, kuti—kuti ndithandize. Mukuona?

149 M’baleyu ananditengera ine kunyumba kwake kuti... mkazi winawake, ndipo mkazi ameneyo amalakwitsa. Ndipo uyu... Ine sindinamuwonapo mkaziyo koma ine ndinazimva izo pa tepi, iye akupereka kutanthauzira kwa malirime, ndi kumanena chinachake. Iwe umakhoza kuzitola izo pomwepo.

150 Tsiku lina, kwa mtumiki wina, ndipo ine, wa munthu yemweyo, ife tinakhala pa chitsa, tikusaka agologolo, ndipo timalankhula za izo. Ndipo atumiki awiri onsewo, amene alipo tsopano, akudziwa momwe izo zinakhallira. Mwaona, basi, inu muone.

151 Pamene atumiki inu mukumukonza winawake za mphatso, pamene inu mukuwakonza iwo, kuwakonza iwo Mwamalemba, ndipo iwo nkukhumudwa, kumbukirani,

umenewo sunali Mzimu wa Mulungu, chifukwa Mzimu wa Mulungu sungakhumudwitsidwe ndi Mawu Ake. Iye amabwera ku Mawu Ake. Mwaona, iye nthawizonse amakhala wololera. Woyera weniweni wa Mulungu amafuna kuchita zoyenera. Inde, bwana.

<sup>152</sup> Ine ndimafuna kuti ndizikonzedwa. Ine ndimafuna Mzimu Woyera uzindikonzana ine mu zinthu zimene ine ndikuchita zimene ziri zolakwika. Ine sindikufuna chirichonse cholowa mmalo. Ine—ine ndikufuna chinthu chenicheni kapena pasakhale kalikonse, mungondisiya ine ndekha, musa—musandilole kuti ndikhale ndi chirichonse nkomwe. Mukuona? Chifukwa kulibwino ine ndichite izo kuposa kubweretsa chitonzo pa Khristu.

<sup>153</sup> Ndipo ine sindingaphunzitse chirichonse ndipo ine sindinganene chirichonse pokhapokhapo Lemba . . .

<sup>154</sup> Ndipo ngati m'bale wina, m'bale wina wa Chikristu angandiwone ine ndikuphunzitsa chinachake cholakwika, ine ndingayamikire izo ngati mungandiyitanire ine ku mbali imodzi utatha msonkhano, ndi kuti, "M'bale Branham, ine ndikufuna kuti ndibwere ku chipinda chanu ndi kudzayankhula ndi inu, inu mukulakwitsa pa chinachake." Mukuona? Ine ndinga—Ine ndithudi ndingayamikire zimenezo, m'bale, chifukwa ine ndikufuna kuti ndikhale wolondola. Ine ndikufuna zimenezo.

<sup>155</sup> Tsopano, tonse a ife tikufuna kukhala olondola, ndi chifukwa chake timafuna kutero—ife timafuna kuti tiziyankhula zinthu izi. Ndipo izo zikuyenera kubwera kudzera mu Lemba, inu mwaona, kudzalipanga Lemba kumangirirana pamodzi.

<sup>156</sup> Tsopano, kuyankhula mmalirime kumayenera kukhala . . . Tsopano, patsogolo pang'ono . . . Tsopano, zisiyeni izo zipite pakali pano, kwa kanthawi. Mwaona, ine ndikukulangizani inu kuti mungozisiya izo zipite ndi kuzilola izo kuti zikhale. Kwa inu atumiki tsopano, inu azibusa, mungolola izo zipite mpaka ana awa adzakule pang'ono pokha. Tsopano, mwinamwake, posachedwa kapena mtsogolo, ngati ali mdani amene akuyesera kuti amunyenge munthu ameneyo, izo zidzawonekera. Ife sitiri otsimikiza kwambiri.

<sup>157</sup> Tsopano, zitatha izi, inu musanayambe izi, mutengere mzimu wina wazeru mmenemo, kuzindikira kwina kwa mizimu, inu mwaona, kuti mufufuze. Chinthu choyambirira, inu mukudziwa, inu mumayamba kuzindikira kuti winawake wayamba kuwona kuti pali chinachake chaching'ono cholakwika, ndiko kuzindikira zamumtima. Kenako, ndi kuzilera izo kanthawi pang'ono. Mukuona? Kenako pamene inu muona kuzindikira zamumtima kukulakwika, ndiye muzikonze izo. Ndipo ngati chinthu chimenecho . . . ngati icho chiri cha Mulungu, iye adzayima kukonzedwako ndi Mawu. Mukuona?

<sup>158</sup> Titi, mwa chitsanzo, ine ndinena kuti ife tinalankhula mmalirime, winawake, ndife...ili ndi a—gulu la mphatso la anthu. Ndipo Leo anadzuka ndipo anayankhula mmalirime; kenako, ndipo m'bale apa, Willard, anapereka kutanthauzira. Chabwino. Tsopano, ine ndikufuna kunena kuti M'bale Neville ndi M'bale Junie ndi M'bale Willard Collins anali ozindikira zamumtima, mwaona. Tsopano, chifukwa Leo anayankhula... Tsopano, ife tiri pano basi ngati mu msonkhano wawung'ono wa overa, msonkhano wa mphatso, ndipo Leo anayankhula ndipo Willard nkupereka kutanthauzira apa, ndipo iye anati, "PAKUTI ATERO AMBUYE! 'Lachitatu usiku pakubwera mkazi muno ndipo iye adza—iye adzakhala wosokoneza. Mumuuze M'bale Branham kuti asadzamudzudzule iye, chifukwa iye ndi wamisala. Koma mumuuze iye kuti adzamatengere iye pakona, chifukwa panali pakona pamene iye anachita chinthu choyipacho nthawi ina ndipo chinthu chinachake chinachitika.'" Mukuona? Izo zikumveka zabwino kwambiri, sichoncho izo? Mukuona? Chabwino.

<sup>159</sup> Tsopano, koma chinthu choyambirira, inu mukudziwa, mu Lemba Lakale, ziribe kanthu zomwe mneneri ananena kapena chimene wina aliyense ananena, izo zinkayesedwa ndi Urimu Tumimu, poyamba. Mwaona, izo zinkapita ku Mawu. Ndipo ngati kuwala kumeneko sikunathwanime, iwo ankazisiya izo zokha. Mukuona?

<sup>160</sup> Ndipo chinthu choyamba, tsopano, tiyeni tizitengere izo kubwerera ku Mawu. Tsopano, munthu *uyu* anayankhula mmalirime, zinamveka zabwino. *Uyu* anatanthauzira, zinamveka zabwino. Koma Mawu anati, "Mulole izo ziweruzidwe ndi oweruza awiri kapena atatu, poyamba." Muzitengere izo ku Urimu Tumimu.

<sup>161</sup> Tsopano, chinthu choyamba, Willard Collins akuti, "Izo zinali za Ambuye." Junie akuti, "Izo ndi za Ambuye—Ambuye." Ndi awiri mwa atatu. Chabwino, izo ziyikidwe pa kachidutswa ka pepala, izo zayankhulidwa pomwe pano mu tchalitchi muno. Ndiye pamene anthu amene aziwona izo zikuwerengedwa zisanachitike konse, ndipo kenako nkuziwona izo zikuchitika, iwo amati, "M'bale, ameneyo ndi Mulungu! Mwaona, ameneyo ndi Mulungu!"

<sup>162</sup> Koma bwanji ngati izo sizichitika, ndiye chimachitika ndi chiyani? Mukuona? (Tsopano tifika ku chinthu china chimene ndingachifikire pomwe pano, "Kodi uneneri wonse kwathunthu...kutanthauzira konse ndi mauthenga ndi ulosi?") Tsopano, miniti yokha. Tsopano, bwanji ngati izo sizichitika? Ndiye kuti *Leo* wayankhula mu mzimu wabodza; *iye* anapereka kutanthauzira kwabodza; ndipo *inu* munapereka chiweruzo chabodza. Ndiye chichotseni chinthu chimenecho mwa inu. Inu simukuchifuna icho. Icho ndi cholakwika. Chisiyeni icho chokha. Ameneyo ndi mdierekezi. Mukuona? [Malo opanda

kanthu pa tepi—Mkonzi]. “*Ine* si mlaliki, koma *ine* ndi—*ine* ndi wotanthauzira. Mwaona, ndine wotanthauzira, Ambuye, *ine—ine* si mlaliki. *Ine . . .*” M’bale *Leo* akuti, “Ambuye, *ine* si mlaliki, koma *ine—ine* ndiri ndi mphatso ya malirime ndipo mdierekezi amandikwiyitsa *ine* pa izo. Mulungu, chotsani chinthu chimenecho kwa *ine*.” *Inu* mukuti, “Ambuye, *Inu* mwandipatsa *ine* mzimu wa kuzindikira zamu mtima, ndipo *ine* ndakuwonani *Inu* mukuchita izo nthawi zambiri, kodi izo zimachitika motani? Atate, ndiyeretseni *ine*! Chinachitika ndi chiyani?” *Inu* mwaona, ndi *inu* apo, ndiye *inu* muli nazo izo zenizeni.

<sup>163</sup> Mwaona, umenewo ndi msonkhano wanthawizonse wa ojera. *Ine* ndikuganiza izo ndi zomwe zinkakhala mu Baibulo, chifukwa Paulo anati, “Ngati wina alosera ndipo chinachake chikuloseredwa, chinachake chima . . . ndipo chinachake nkuwululidwa kwa wina atakhala; muloleni iye asunge bata mpaka uyu ayankhule kaye, ndiye iye akhoza kuyankhula. Ndipo *inu* *nonse* mukhoza kulosera mmodzi ndi mmodzi.” Tsopano, izo sizingakhale mu msonkhano wamba, *inu* mukudziwa zimenezo, aliyense sangati apereke.

<sup>164</sup> Tsopano, kuti mukhale otsimikiza kuti izo ndi za Mulungu, mwaona, chifukwa ngati ziri zopusa basi izo si za Mulungu. Ngati izo sizichitika, izo si za Mulungu. Mukuona? Izo zikuyenera kuchitika. Ndipo—ndipo chotero mmipingo yathu, *inu* mwaona, m’bale, ife tiri ndi mpingo wolimba ndiye, mwaona, kumene palibe aliyense angathe kunena kuti chirichonse chinayamba chanenedwa kapena kuchitidwa . . .

<sup>165</sup> Onani chimene izo zimandiyika *ine*, pamene *ine* ndiri pamwamba apo pamaso pa anthu. Tayang’anani pa izo! Nanga bwanji cholakwika chimodzi pa izo? Mukuona? Chifukwa *ine* ndimamudalira Iye. Mukuona? *Ine* ndimamudalira Iye. Winawake akuti, “*Inu* mukuwopa kulakwitsa, M’bale Branham?” Ayi, ayi, uh-huh, sindikuwopa kulakwitsa. *Ine* ndikumukhulupirira Iye. Iye ndi Chitetezo changa. *Ine* ndinadzozedwa kuti ndizichita izi chotero ndizikhala pomwepo.

<sup>166</sup> Ngati Mulungu wakudzodzani *inu* kuti muzichita chinachake, ndiye Iye ndi Chitetezo chanu. Mwaona, Iye adzakutetezani *inu*. Ngati Iye anakutumizani *inu*, Iye adzayimira kumbuyo mawu anu. Ndinu kazembe ndiye. *Ndinu* kazembe ndi mphatso ya malirime; *ndinu* kazembe ndi mphatso ya kutanthauzira; *ndinu* kazembe ndi mphatso ya kuzindikira; atatu a *inu*. Mukuona chimene *ine* ndikutanthauza? Ndiye *inu* muli ndi chiyani? *Inu* muli ndi mpingo wokhawikika. *Inu* simungawoqe. Kuyima, eya, osati kuposa dzulo . . .

<sup>167</sup> Kuno, *ine* ndinali mu msonkhano kumusi kuno. Mnyamata wamng’ono Wachinguzu wochokera ku England anabwera kuno, anali akuyesera kuti adziphe. M’bale Banks anabwera kumeneko

ndipo anati, “Iye anali ali kumeneko masiku foro kapena faivi.” Ine ndinali ndi zinthu zambiri zoti ndichite, koma iye anati, “Mnyamatayo adzipha.” Hotelo ya Waterview kumusi uko inkandiuza ine za chikhalidwe cha mnyamata ameneyo.

<sup>168</sup> Ndipo ine ndinapita mu chipindamo kuti ndikamupempherere iye. Ndinatuluka ndipo ine ndinati, “Tsopano, M’bale Banks, ine sindinamuwonepo mwamunayo kapena kudziwa kanthu za iye, koma ndikuuzani inu chimene liri vuto ndi iye ine ndisanafike kumeneko.” Ndi kulondola kumeneko, M’bale Banks? Ndipo pamene ife tinafika kumeneko, Mzimu Woyera unatsika pansi ndipo unamuza iye chimene chinachita izo ndi zonse za iye, ndi kumene iye anali ndi zonse za moyo wake. Iye anangogwera pamenepo, pafupifupi.

<sup>169</sup> “Kodi inu mukuwopa kulakwitsa, M’bale Branham, inu kumuza munthu chinachake chonga icho?” Nanga bwanji pa nsanja, kumuza mwamuna kuti akukhala mosayenera kwa mkazi wake, ali ndi mwana ndi mkazi wina? Iye angakuponyere iwe mu ndende. Iwe uyenera kukhala wolondola! Mukuona? Mukuona? Osamachita mantha, ngati ali Mulungu. Koma ngati sukuchita mantha . . . Ngati—ngati sukudziwa kuti ndi Mulungu, ndiye khalani bata mpaka inu mutadziwa kuti ndi Mulungu. Nkulondola uko? Mukhale otsimikiza kuti mukulondola kenako muzipitirira.

<sup>170</sup> Tsopano, uku ndi kuphunzitsa kolimba, m’bale, koma inu ndi abale anga. Ndinu—ndinu—ndinu atumiki aang’ono amene mukubwera, ndipo ndine bambo wachikulire, ndidzachoka limodzi la masiku awa. Mukuona? Ndipo kotero inu mutsimikizire kuti izo ndi—ndi zolondola.

<sup>171</sup> Ndikutuluka mchipinda cha . . . Mwinamwake ndidzazipeza izi patsogolo pang’ono apa. Mnyamata . . . Chabwino, ine ndidzanena gawo la izo tsopano. Dzulo, M’bale Banks ndi ine, otanganidwa kwenikweni, takhala (oh, mai) molimba momwe ine ndikanathera, ndipo ine ndi—ine ndikuuzani inu chimene ndikanachita pa msonkhano uno. Leo ndi Gene ndi gulu la ife timati tipite kumeneko, ndi abale, ndi kuti ife timati tipita kukasaka nkumbwa, kukasaka nguluwe. Iwo ali ndi masiku faivi osaka nguluwe za javelina, mu Arizona, msonkhano ukatha, msonkhano wathu ukatsekedwa. Ife tipita ku Phoenix kwa tsiku limodzi, ndipo tikuyenera kudikira masiku faivi tisanakhale ndi wina, masiku foro asanakhale ndi msonkhano wina kulikonse. Ife tikuyenera kukakhala kumeneko ku Arizona. Chabwino, zachitika kuti ndi nthawi yomweyo imene nyengo ya nguluwe za javelina yatsegulidwa.

<sup>172</sup> Chotero ine ndimafuna kuti ndipite kukawombera mfuti yanga yaing’ono, kuti ndikawone ngati iyo inali bwino. Banks amapita ndi ine. Tinawuyamba kutuluka pa chipata, tinayamba kutuluka pa chipata. Apa panabwera munthu akulowa mkati,

pamwamba pa chikwangwani chimenecho (mwaona, chinati, “Chonde musafunse za M’bale Branham”).

<sup>173</sup> Mwaona, chifukwa chimene iwo amachitira zimenezo . . . si chifukwa cha anthu amene akudwala. Yanga, ndipo kunyumba, mufunsemi Banks, iye amakhala pafupi ndi ine. Anthu amabwera, usana ndi usiku ndi china chirichonse, ndi ana odwala, chirichonse. Ife sitimamubweza munthu woteroyo. Koma . . .

<sup>174</sup> Ndipo iwo anandiyitana ine, Leo ndi iwo, kuchokera kunja uko pa ngolo, ndi Jim ndi iwo, “Pali winawake pano ali ndi mwana wodwala. Ndipo pali bambo pano ali ndi khansa.” Ife timasiya chirichonse ndi kunyamuka kupita kwa iye.

<sup>175</sup> Usiku wathawu ndinaitanidwa ku chipinda cha chipatala kumene winawake anandiyitana ine, ndipo mwamunayo sanandilore ine nkomwe kuti ndilowe nditafika kumeneko. Mwaona, winawake anangotengeka. Koma izo ziri bwino, ine ndinapita mulimonse. Mukuona? Chifukwa ndi ntchito yanga kuti ndipiteko, mwaona, ndi kuyesera kuti ndikamuthandize winawake.

<sup>176</sup> Chabwino, chimenecho sindicho chimene tinaikira chikwangwanicho. Koma mwamuna uyu, basi pamene timakalowa mgalimoto, ndipo M’bale Banks akudziwa kuti ndimayenera kutero . . . Ine ndinadikirira mnyumba mmenemo mwanjira ina. Panali winawake amene anadzabwera kwa M’bale Banks amene anamuchedwetsa iye. Ndipo atangofika kumeneko, ine ndinachedwetsedwa. Kenako titangotenga mfuti yathu ndi kuyamba kukwera mgalimoto, apa panadzabwera mwamuna akulowa mkati. Iye anayenda kukwera pamene.

<sup>177</sup> Ndipo ine ndinali ndikukonzekera kuti ndimuwuze iye kuti apite kukayimba nambala ija kunja uko (pa BUtler 2-1519) pamwamba pa chikwangwani chimenecho. [Nambala yafoni inasinthidwa.—Mkonzi]. Ine ndinati, “Ife tiri pachangu.”

Anati, “Ndikuganiza kuti inu muli pa changu, bwana.”

Ine ndinati, “Dzina langa . . .”

<sup>178</sup> Choyamba ine ndinanyamuka, iye anati, “Inu muli bwanji?” Ndipo ndinawona kuti iye samadziwa kuti ine ndinali ndani.

Ine ndinati, “Dzina langa ndi Branham.”

Iye anati, “Ndinu M’bale Branham?”

Ine ndinati, “Ndi ineyo.”

<sup>179</sup> Ndipo iye anati, “Ine—ndine . . . Ine ndimafuna kukumana nanu, M’bale Branham.” Anati, “Ndikuwona kuti mukukonzekera kunyamukapo.”

Ine ndinati, “Inde, bwana, ine ndikutero.”

Iye anati, “Ndikudziwa kuti mukufulumira.”

Ine ndinati, “Ine ndikutero pakali pano, bwana.”



180 Ndipo iye anati, “Chabwino, ine ndimangofuna kuti ndiyankhule nanu maminiti pang’ono.”

181 Ndipo ine ndinali woti ndikukangomuuya iye; ndipo Mzimu Woyera unati, “Mutengere iye mchipindamo, iwe ukhoza kumuthandiza iye.” Tsopano, apo, izo zimasintha chirichonse. Mfuti inangoyikidwa pambali, ndi chirichonse monga choncho, ntchito ya Mulungu izikhala yoyambirira. Mukuona? Ndipo iye anati . . .

182 Ine ndinati, “Bwerani, mupite ndi ine.” Ine ndinati, “Ine ndibwerera pakapita kanthawi, M’bale Banks.”

Iye anati, “Ndi zokhudza solo yanga, M’bale Branham.”

Ine ndinati, “Chabwino, lowani.”

Tinapita kudutsa mnyumbamo, Meda anati, “Kodi inu simunapitebe?”

183 Ine ndinati, “Ayi, ayi, ayi, ndi winawake kunja kuno.” Ine ndinati, “Ukawayike ana mu chipinda chinacho.” Ine ndinamutengera iye mchipinda chaching’ono, tinakhala pansi. Posakhalitsa titakhala pansi . . .

184 Mwamuna ameneyo anali mu tchalitchi usiku watha. Kapena kodi iye anabwera, Banks? Kodi inu . . . Eya, chabwino, iye amayenera kuti abwere usiku watha. Iye anali basi . . .

185 Chinthu choyambirira, Mzimu Woyera unayamba kumuuya iye chimene iye anali, chimene iye anali atachita, chimene chinachitika kudutsa mmoyo wake, chirichonse cha izo, mwaona, kumangapitirira basi, kumuuya iye chirichonse. Banks ndi mboni. Sanatsegule pakamwa pake ndi kunena koma pafupifupi mawu awiri kwa ine; ndipo apo Iwo unabwera kumuuya iye, unati, “Iwe wakhala woyendayenda, iwe kwenikweni umakhala ku Madison. Iwe wangobwera kumene kuchokera ku Evansville, Indiana. Iwe wakhala kumusi uko mu sukulu ya Baibulo iyi, kagulu kachipembedzo, unangosokonezeka yense. Iwe wangobwera kumene ku Louisville maminiti pang’ono apitawo. Panali mwamuna, ndipo mwamunayo anakuuza iwe (amene unakhala ndi kumadya naye), anakuuza iwe kuti ubwere kuno ndi kudzandiwona ine ndipo ‘iye akakuwongola iwe kuchoka mu vutolo.’” Ine ndinati, “Ndizo PAKUTI ATERO AMBUYE!”

186 Mwamunayo atangokhala, akuphethira maso ake, akundiayang’ana ine, anati, “Inde, bwana!”

Ine ndinati, “Zakudzidzimutsa iwe, sichoncho izo?”

Iye anati, “Izo zatero.”

Ine ndinati, “Kodi iwe umakhulupirira Mzimu Woyera?”

Iye anati, “Ndikufuna kutero, bwana.”

187 Ndipo ine ndinati, “Kodi iwe ukufuna kuti ndikuuze zimene iwe ukuganiza?”

188 Iye anati, “Inde, bwana.” Ndipo ine ndinamuza iye. Iye anati, “Ndipo, m’bale, izo ndi zoonā.”

Ndipo ine ndinati, “Sintha zoganza zako.”

Iye anati, “Chabwino, ine ndatero.”

Ine ndinati, “*Ichi* ndi chimene iwe ukuganza.”

Iye anati, “Izo nzoona! Izo nzoona!”

189 Ine ndinati, “Tsopano, iwe sukusowa masomphenya, ukungosowa kuwongoledwa.” Ndipo ine ndinamuza iye chinachake pamenepo chimene inu simukanafuna ine ndikuuzeni. Ngati izo zikanakhala pa inu, inu simukanatero. Ndi chinthu china choyipa chomwe chinali chosakhala bwino, chotero inu simukanafuna kuti ndi chinene ngati icho chikanakhala pa inu. Ndipo ine sindimanena zimene Ambuye amandiwonetsa pa anthu. Chotero ine ndinangoti, “Chabwino, iwe ukachita zimenezo?”

Iye anati, “Ine ndikatero.”

Ine ndinati, “Uyambepo ulendo wako.”

190 Iye tinali mmenemo pafupifupi osapitirira maminiti teni, sichoncho izo, M’bale Banks? Pafupifupi, pakati pa maminiti seveni ndi teni. Tinayenda kutuluka, tinabwereranso mu msewu, ndi kumapita kumusi mumsewu, iye ndi ine ndi Banks ndi mnyamata wanga wamng’ono, Joe, ine ndikukhulupirira anali, akuyenda motsogozana limodzi, kupita motsika kachitunda. Iye anapotokera kwa ine, iye anati, “Bambo, ine ndikufuna ndikufunsi inu funso.”

Ine ndinati, “Chabwino.”

191 Iye anati, “Ine ndasokonezeka pang’ono.” Iye anati, “Inu munadziwa bwanji zinthu zonsezo pa ine?” Mukuona? Banks anali atakhala pamenepo.

192 Ndipo ndinati, “Bambo, kodi inu munayamba mwamvapo za masomphenya anga ndi utumiki wanga?”

193 Iye anati, “Ine sindimadziwa dzina lanu mpaka pafupifupi ora lapitalo. Winawake anandiuza ine, anangonena uko ku Louisville, anandiuza ine kuti ndibwere kuno, ndipo ine ndinayenda kuwoloka mlathowo.” Nzoona zimenezo, Banks? Iye anati, “Ine sindimadziwa nkomwe dzina lanu, kudziwa yemwe inu munalu.”

194 Ine ndinati, “Mu utumiki wanga, iyo ndi mphatso ya Mulungu imene Iye anatumiza.”

195 Iye anati, “Ndiye ngati umo—umo ndi momwe izo ziliri,” anati, “tsopano ndine . . .” Anati, “Ndine basi zonse . . . Ine ndiri bwino tsopano,” iye anati, “chirichonse chapita.” Mukuona? Iye anati, “Chimene icho chiri, ameneyo anali Mulungu akuyankhula kudzera mwa inu kwa ine.”

Ine ndinati, “Kulondola.”

<sup>196</sup> Iye anati, “Tsopano, ine ndinamva mu Baibulo kuti... Nthawi ina ndinawerenga mu Baibulo ndipo, linati, Yesu ankayankhula ndi ophunzira Ake,” chimene ankatanthauza “anthu,” inu mwaona. Anati, “Ankayankhula kwa ophunzira Ake ndipo Iye anawauza iwo zinthu zimene ankaganiza.” Mwaona, “kuzindikira maganizo awo” ndi chimene ankafikirako. Iye anati, “Ndipo Iye anati anali Atate Ake amene ankayankhula kudzera mwa Iye.”

Ine ndinati, “Uko nkulondola.”

<sup>197</sup> Iye anati, “Tsopano, tsopano, Atate ndiye anangokugwiritsani inu ntchito kuti alankhule kudzera mwa inu kwa ine, kuti andiuze ine zinthu izi, kuti ndikhulupirire kuti chimene inu munandiuza ndi choonadi.”

Ine ndinati, “Kodi chinali choonadi?”

Iye anati, “Inde.” Ndinati, “Ndiye akuyenera kukhala Mulungu.”

<sup>198</sup> Ndipo ine ndinati, “M’bale, inu mukudziwa zambiri za izo tsopano” (ine ndi Banks tinali kuchitira ndemanga) “kuposa ena amene akhala mu msonkhano kwa zaka teni ndipo samatero panobe.” Basi uyo—mwamuna ameneyo! Tsopano, izo ndi zomwe izo ziri. Mukuona?

**Ndipo Mzimu (mwadongosolo) mu malirime ndi uneneri woti uzigwiritsidwa ntchito pa nthawi ya utumiki?**

<sup>199</sup> Ayi. Izo zikuyenera kugwiritsidwa ntchito mwanjira *iyi*, ndipo kenako *kunenedwa* mu utumiki. Koma kwa nthawi ino, kwa nthawi yapano, aloleni iwo alankhule. Tsopano, ngati izo zifika povuta, ndiye izo siziri, inu mukuyenera kuziyang’ana izo. Tsopano, nthawizina akhoza kukhala Mulungu. Ndipo ana aang’ono amenewo, monga ngati mwana wamng’ono akuyesera kuyenda, tsopano, ngati iye agwa pansi kanayi kapena kasanu... Tsopano, ine ndaziwona izi kuyambira pamene ine ndakhala ndiri kuno mu mpingo, ndipo—ndipo, chabwino, ine ndi—ndingozisiya izo monga choncho. Mukuona? Ndipo, koma, inu mukuona, koma bwanji za izo, ndiye inu mungati, “M’bale Branham, chifukwa chiyani inu simunakonze izi?” Ayi, ayi.

<sup>200</sup> Pamene Billy Paul kumbuyo uko ankayamba kuyenda, iye anali ankayima ndi kugwa, ndipo kugwa kunkaposa momwe iye ankaimiririra. Koma iye sankadziwa momwe angayendere. Koma ndikukhulupirira kuti iye anali ndi mphatso yoyenda. Mukuona? Ine ndinkamusiya iye kuti ayende pang’ono. Ndiyeno pamene iye anafika popunthwa mapazi ake aakulu, ine ndimamuza iye za izo tsopano. Inu mukuona chimene ine ndikutanthauza? Mukuona? Kumapitirira ukuyang’ana chinachake ndi kumalowa mu chinachake, ine nkumati, “Nyamula mapazi ako, mnyamata. Iwe uli kuti?” Mukuona? Tsopano, ndiko—ndiko kusiyana kwake, inu mwaona.

<sup>201</sup> Tsopano, kuwalola iwo—kuwalola iwo azipunthwa ndi kuwalola iwo azikole kanthawi pang’ono. Tsopano, pamene iwe ukuyenera kuwakonza iwo, ngati iwo azikana izo ndiye iwe umadziwa wekha kuti sanali Mulungu. Chifukwa Mzimu wa Mulungu ndi womvera. Monga inu munamvera pano pang’ono pokha, “Mzimu wa uneneri umamumvera mneneri.” Mukuona? Uko nkulondola.

[M’bale Stricker akuti, **“M’bale Branham, ine ndikufuna kukonzedwa kwina.”**—Mkonzi]. Chabwino, m’bale. [**“Nthawi zambiri ndakhalapo mmisonkhano ndipo ndamvapo kuyankhula mmalirime ndi kutanthauzira, ndipo nthawi zambiri ndamvererapo moyipa kwambiri za izo. Ndipo ndimapita kunyumba ndipo ndimawoneka ngati ndizilapa njira yonseyo. Kodi chinali chifukwa chakuti ndinamverera kuti izo sizinali za Mulungu, kapena zimakhala chifukwa chakuti sizinali mu dongosolo?”**]

<sup>202</sup> Izo zikanakhoza kukhala, m’bale, izo zikanakhoza kukhala mulimonse. Mukuona? Ine ndikhoza kunena kuti... Tsopano, uyu ndi—uyu ndi William Branham, mwaona; mpaka ine nditalowa mu Lemba, bwanji, ndikadali inebe, inu mwaona. Tsopano, ichi ine ndinganene, M’bale Stricker, kuti icho chikhoza kukhala chimodzi mwa izo. Izo zikhoza kukhala kuti izo zinali kunjira kwa dongosolo; zikhoza kukhala kuti chinali chinachake cholakwika ndi inu; zikhoza kukhala kuti panali chinachake cholakwika ndi munthuyo; chinachake cholakwika ndi uthengawo; kapena chirichonse chikanakupangitsani inu *kumverera* moyipa.

<sup>203</sup> Tsopano, tsopano, ndiroleni ine ndingokuthandizani inu pang’ono pokha, M’bale Stricker, apa. Mukuona? Nthawizonse... Musamachiweruze chirichonse pogwiritsa ntchito kumverera kwake, inu mwaona. Muzichiweruza icho ndi zikhumbo zake, inu mwaona; chirichonse chimene icho chimabala chipatso, inu mwaona. Chifukwa nthawizina...

<sup>204</sup> Chifukwa, ife tikuzindikira kuti pali zinthu zomwe inu mumazimverera, kumverera mwachizimbwizimbwi uko. Ine ndimazipeza izo inemwini, ndipo, mnyamata, ndimayamba kusuntha kuchokako—mophweka, inu mukudziwa. Koma ine sindinena kanthu. Ndimangozisiya izo zokha chifukwa ine sindimadziwa chimene izo zingakhale, inu mwaona, mpaka ine *nditadziwa* chimene izo ziri.

<sup>205</sup> Tsopano, monga momwe anthu ambiri amanenera, “Psyii! M’bale, ine ndikudziwa ine ndiri ndi Mzimu Woyera! Aleluya! Mulungu alemekezeke!” Ndipo iwo nkukhalabe opanda Mzimu Woyera. Iwo amatha kuyankhula ndi malirime, ndi china chirichonse, ndi kufuula ndi kuvina mu Mzimu, ndipo osakhalabe ndi Mzimu Woyera. Chifukwa mvula imagwera pa

olungama ndi osalungama. Izo siziri mwa zomverera, ziri ndi *chipatso* chawo.

<sup>206</sup> Kunena kuti pali a . . . Mukukumbukira masomphenya anga a izo? Momwe izo . . . Ahebri 6, inu mwaona, “Mvula imene imabwera mowirikiza padziko lapansi ndi yoti izithirira izo, zimene zalimidwa, koma minga ndi nthula zimene ziri pafupi kukanidwa zimene mathero ake ndi kukawotchedwa.”

<sup>207</sup> Mundikhululukire ine, ndilowetsa mpweya pang’ono, ndikudziwa kuti nonse mukuyamba kugona ndipo mukuyamba kutopa. Chotero tsopano, dikirani, ndikuyenera kuti ndifulumire nazo izi mwaliwiro kapena sindizitenga izo. Izi ziyenera . . . Ife tiri pa maziko a—a zonse za izo, mu a mmanja awa apa. Koma iwo . . . Mwaona, a . . .

<sup>208</sup> Apa pali—munda wodzadza ndi tirigu. Ndipo mmunda umenewo mwaferedwa udzu, zisoso, kapena zina zotero, udzu. Chabwino, chilala chayamba. Tsopano, kodi udzu wa kamfiti ndi chisoso sizimva ludzu chimodzimodzi basi monga tirigu? Ndipo ndi mvula ya mtundu wanji . . . mvula yapadera imagwera pa tirigu ndipo kenako mvula yapadera imagwera pa chisoso? Nkulondola uko? Ayi, mvula yomweyo imagwera pa icho. Nkulondola uko? Mzimu womwewo umagwera pa wachinyengo ndi umene umagwera pa Mkristu, chinthu chomwe chomwecho. Koma mwa chawo “chipatso”! Kodi zimenezo zikulowerera mkati, abale?

<sup>209</sup> Umboni wa Mzimu Woyera ndi chipatso cha Iwo, chipatso cha Mzimu. Chabwino, izo . . . Chabwino, tsopano, inu mukuti, “Ine ndi tsinde, ine ndi chisoso. Ine ndi tsinde mofanana ndi tsinde la tirigu.” Koma mwa inu muli moyo wa mtundu wanji? Moyo umene uli mmenemo umabala zomata, nthawizonse kukangana ndi kudula, ndipo, “kufuula,” woipa ndi wodwala, ndi chirichonse. Mukuona chimene ine ndikutanthauza? Wamwano, mwaona, chimenecho si chipatso cha Mzimu. Chipatso cha Mzimu ndi kufatsa, chipiriro, kudekha, mwaona, zonsezo. Mukuona?

<sup>210</sup> Iye akhoza kunena kuti, “Chabwino, ine ndikhoza kufuula mokweza basi momwe inu mungathere. Mulungu adalitsike, Mzimu Woyera umagwera pa ine!” Izo zikhoza kukhala chidutswa chirichonse choona, koma moyo umene iye amakhala sumayikira kumbuyo chimene iye akukamba. Mukuona? Iye anali udzu, iye anali udzu kuyamba ndi kuyamba.

<sup>211</sup> Tsopano, ife tifika pa funso lalikulu tsopano, mwaona, pa *kusankhidwa*, inu mwaona. Chotero ndizo . . . Inu mukuyenera kukhala chimenecho. Inu mukumvetsa zimenezo.

<sup>212</sup> *Iwo* anali chisoso kuyamba ndi kuyamba; *iye* anali tirigu kuyamba ndi kuyamba. Chotero chilala chinali chitayamba; mvula inagwera pa olungama ndi osalungama. Chabwino, mukumvetsa zimenezo?

[Mbale akufunsa, **“Nanga bwanji zipatso za mlaliki, kodi izo. . . kumeneko ndi kulalikira Mawu?”**—Mkonzi].

<sup>213</sup> Kuti, mlalikiyo, apobe, ngati iye atayima pamenepo ndi kumalalikira Mawu monga Mngelowamkulu, mwaona, nkumamvetsa zinsinsi za Baibulo, ndipo nkukhala m’busa wabwino kwambiri, kumapita ndi kukachezera anthu ndi zinthu monga zimenezo, iye akhoza kutayikabe. Mukuona? Ndi chipatso chake chimanena izo nthawi iliyonse, m’bale. Mukuona? Iye, ziribe kanthu momwe iye aliri wabwino kapena chimene iye ali, iye akuyenera kukhala ndi Mzimu Woyera mmoyo wake. Mukuona?

<sup>214</sup> Tsopano, kodi Yesu sanati, “Ambiri adzadzwa kwa Ine tsiku limenelo ndipo adzati, ‘Ambuye, kodi ine sindinanenere (kulalikira) mu Dzina Lanu, ndipo ndinachita zozizwitsa mu Dzina Lanu?’” Iye anali atayankhula ndi malirime, iye anali atachita zozizwitsa, anapereka kutanthauzira, zinthu za chinsinsi za Mulungu, ndi zinthu zonsezo apo; Iye anati, “Chokani kwa Ine, inu akuchita kusaeruzika, Ine sindinakudziweni inu nkomwe.” Mukuona chimene ine ndikutanthauza?

[M’bale Taylor akufunsa, **“Nanga bwanji munthu wobweretsa a—a uthenga wolakwika? Ine ndikutanthauza, iye—iye amaganiza kuti akulondola koma kulalikira zolakwika.”**—Mkonzi].

<sup>215</sup> Chabwino, ine ndikukhulupirira kuti munthu ameneyo ndi woonamtima, monga m’bale amene wakhala apa amafuna kuti abwererenso ku zake. . .kuzitsatira mmbuyo zinthu izi monga choncho. Ngati munthu ameneyo ali wosankhidwa ndi Mulungu, ndipo nkubweretsedwa pamaso pa Choonadi, iye adza—iye adzachizindikira Icho. Mwaona, “Nkhosa Zanga zimadziwa Liwu Langa.” Inu pansi-. . .Mukuona chimene ine ndikutanthauza, M’bale Taylor? Kodi izo ndi zomwe mumanena? Mukuona?

<sup>216</sup> Tsopano, mwachitsanzo, titi M’bale Crase—Crase—Crase, kunena kuti iye anali mlaliki wa Baptisti ndipo iye samadziwa kalikonse za ubatizo wa Mzimu Woyera, ngakhalenso iye samadziwa chirichonse cha zinthu izi, mphatso za Mzimu, ndipo iye anali wabwino, mlaliki wokhulupirika wa Baptisti. Mukuona? Koma chinthu choyamba inu mukudziwa, Ichi chikubwera pamaso pake. Ndipo ine ndikukhulupirira kuti mwana aliyense wa Mulungu adza. . .m’badwo uliwonse udzazigwira izo mpaka Iye atamupeza iye. Ufumu sungabwere mpaka chifuniro cha Mulungu chitachitika. Uko nkulondola. Ndipo palibe mmodzi adzawonongeke, inu mwaona. Tsopano, mwaona, imeneyo ndi njira yake.

<sup>217</sup> Ndipo Ufumu wa Kumwamba uli ngati munthu akuponya khoka mu nyanja ndi kulitulutsa ilo. Pamene iye anapeza, iye

anapeza mitundu yonse. Iye anasunga nsomba, ndipo akamba ndi nkhasi zinabwerera m'madzi. Iye analiponyanso ilo, anapeza zinanso, mwinamwake anapeza nsomba imodzi. Koma Iye anapitirira kumagwira mpaka izo zonse zinagwidwa. Mukuona chimene ine ndikutanthauza tsopano?

<sup>218</sup> Koma nsomba imeneyo inali nsomba pachiyambi. Iyo inangoyikidwa kuti igwiritsidwe ntchito ndi Mbuye, ndizo zonse, kuyika iyo mu dziwe lina limene linali labwinoko, loyera. Koma Iye anali akugwirabe mu dziwe la achule ili mpaka Iye atapeza nsomba zonse mmenemo. Mukuona chimene ine ndikutanthauza? Inu mukumvetsa chimene ine ndikutanthauza, M'bale Taylor. Inu mukuyenera kudziwa ndi anu kumtunda uko.

Chabwino, tsopano:

**113. Kodi iye amachita . . . Kodi iye nthawi zonse amakhala ndi ulamuliro pa Mzimu za nthawi ndi momwe angachitire?**

<sup>219</sup> Inde, bwana. Inde, bwana, Mzimu Woyera umalamulira. Inde, bwana. Iwo umakhala ndi ulamuliro pa inu ndipo inu mumakhala ndi ulamuliro pa Iwo, ndipo Iwo sungakupangitseni inu kuchita chirichonse chosiyana ndi Lemba. Iwo udzapanga. . . “Mzimu sumadzipangitsa Wokha mosayenera.” Uko nkulondola. Chabwino.

<sup>220</sup> “Kuchokera kwa iye amene amakukondani inu. . .” Eya, ndizo—izo ziri mu malo awa. Chabwino, tsopano ife tilumphira ku lina apa ndi kuwona pamene ife tiri.

<sup>221</sup> Tsopano, ine ndikuganiza izo zinali ndi maziko. Tsopano—tsopano, pamene ine ndikutchula izi tsopano, ngati pali funso. . . Kodi panalinso funso lowonjezera pa izi? Ife tonse tikumvetsa zimenezo? Ife tikumvetsa momwe timakhulupiririra Iwo tsopano?

<sup>222</sup> [M'bale akuti, “Ine ndiri ndi funso limodzi.”—Mkonzi]. Pitirirani nazo. La izi apabe? Chabwino. [“Inde, za izo apo. Ndinakhala ngati ndajejema, koma. . .”] Musajejeme, izi ndi—izi ndi. . . [“Inu mumakamba za munthu amene akulalikira, ndipo ngati iye sakulalikira Uthenga umene Khristu anawubweretsa, ndipo mosalabadira zomwe zikuchitika mu utumiki wake. Pamene iye afika pokumana ndi Choonadi ndipo iye nkuchikana Ichu, ndiye chiyani?”] Iye watayika. Mundikhululukire ine miniti chabe chifukwa. . . [“Ine ndimalozera ku kukonzedweratu kapena kudzozedweratu maziko a dziko lapasi asanakhazikitsidwe.”] Uko nkulondola. Uko nkulondola. Mukuona? [“Ndiye, momwe izo zinaliri, iye sankayenera kukhala moteromo?”] Samayenera kukhala mwanjira imeneyo pachiyambi, mwaona. “Iwo anachoka pakati pathu chifukwa iwo sanali a ife.”

<sup>223</sup> Mwa chitsanzo, monga chonchi, ndi chinthu chomwecho mu Ahebri 6. Mukuona? Anthu amatanthauzira molakwika Lemba limenelo mochuluka kwambiri, iwo amaganiza

kuti ndi “zosatheka.” Iye anati, “Ndi zosatheka kwa iwo amene anawunikiridwapo ndi kupangidwa ogawana nawo za Mzimu Woyera, ngati iwo adzagwa.” Mwaona, iwo basi samalandira Iwo. Iye akuti, “Ndi kosatheka kwa iwo amene anawunikiridwapo ndi ogawana nawo a Mzimu Woyera, powona kuti iwo agwa kuti adzikonze okha kachiwiri ku kulapa, powona kuti iwo akudzipachikira kwa iwoeni Mwana wa Mulungu kachiwiri ndi kumuyika Iye ku manyazi a poyera; anawerengera Magazi a pangano amene Iye anapachikidwa nawo ‘chinthu chosayera,’ kuchita mosasamala ku ntchito za chisomo.”

224 Chabwino, kwa ine, ndi vumbulutso. Ndithudi. Izo ziri monga ngati Machitidwe 2:38, ndi Machitidwe... ndi Mateyu 28:19. Inu mukuyenera kungochigwira Ichu, inu mwaona.

225 Tsopano taonani, ndi ichi apa, chinthu chomwecho. Chabwino, tsopano, iye akuyankhula kwa Ahebri. Mukuona? Tsopano werengani mpaka mmusi kudutsa mutuwo, motalika mmene iwo amapitira patsogolo ndi kuti, “Pakuti ndi chinthu chowopsya kugwera mu—kugwera m’manja a Mulungu wamoyo.” Tsopano, apa pali munthu monga wokhulupirira wammalire uja. Apa, apa pali a... Apa, chinthu chomwecho chinali apa, chitsanzo changwirowo chimene ine ndikuchiwona mmalingaliro anga.

226 Mulungu anamuitana Israeli kuti atuluke mu Igupto. Anthu onsewa anabwera, aliyense wa iwo anawomboledwa, anawoloka pa Nyanja Yofiira anakalowa mu chipululu. Nkulondola uko? Nyanja Yofiira... Pamene iwo anakonzeka, anamvetsera uthenga wa Mose, anayamba kuguba, (kulungamitsidwa) iwo anatembenuka, anayambira apa.

227 Iwo anafika pa Nyanja Yofiira, (Magazi), ndipo anapita kuwoloka Nyanja Yofiira, ndipo mmbuyo mwawo onse owagwiritsa ntchito anali atagona, atafa. Iwo anali pafupifupi masiku atatu kuchokera ku dziko lolonjzedwa pomwe apo. Mukuona? Ndizo zonse zomwe iwo anali, kuchepera mailosi forte, mwaona. Chotero ndi awo pamene, masiku awiri okha akanawayika iwo kumeneko bwinobwino.

228 Ndicho chimene ine ndikulinga kuti ndikalalikire ku Phoenix mmasiku angapo kuchokera pano, pa msonkhano wa Amuna Azamalonda, *Kukhala pa Phiri ili*. Koma Iye anawasunga iwo pomwe apo kwa zaka forte chifukwa iwo... Uh-huh! Mukuona?

229 Chotero iwo anabwera ku ichi ndipo anayang’ana m’mbuyo, (oyeretsedwa), “Oh, aleluya! Mulungu alemekezeke! Ulemelero kwa Mulungu. Aleluya! Apo pali chinthu chakale chimene nthawi ina chinkandivutitsa ine, chafa. Ndudu zakale zomwe ine ndinkasuta zapita. Kachasu wakale amene ine ndinkamwa yense



ali mu nyanja yofiira ya Magazi a Yesu Khristu. O ulemelero kwa Mulungu! Aleluya!”

<sup>230</sup> Aliyense wa iwo anabwera kuno, iwo anakomana ndi Kenani tsopano, anawoloka Yordani. Chabwino, iye anatenga woyimira kuchokera mu fuko lirilonse. Nkulondola uko? Ndipo iye anawatumiza iwo kumeneko. Chabwino, ena a iwo anati, “Ah, ah, ah, ife sitingachite zimenezo. Ayi, izo—izo... Bwanji, ife tikuwoneka ngati ziwala pambali pa iwo!” Mukuona?

<sup>231</sup> “Tsopano, kodi ndi mpingo wantundu wanji umene ine ndikanawulalikira ngati ine ndikanaphunzitsa Mzimu Woyera ndi zinthu zonsezo monga choncho? Bwanji, ine ndikanakhala ndi mipando yosakhaliidwa. Anthu anga Amethodisti akanatuluka, anthu anga Abaptisti, Apresbateria anga.” Aloleni iwo atuluke. Iwo anali mbuzi kuyamba ndi kuyamba! Inu mukufuna nkhosa, mwaona. Mukuona? Inu simukuchitira ubusa mbuzi. Muzichitira ubusa nkhosa! Ndi zantchito yanji kuchitira ubusa mbuzi pamene...?...ndipo pali nkhosa zoti zichitidwire ubusa? Mukuona? Ndipo apa—apa inu muli apa, mwaona. Ine nthawizonse ndimati ndingakhale ndikulalikira kwa nsanamira zinayi ndi kulalikira Choonadi, Mpingo. Inde, bwana, bwerani kuno.

<sup>232</sup> Koma onani tsopano, kodi iye wachita chiyani? Iwo anabwerera, ndipo Yoswa ndi Kalebu, thuu peresenti, kapena ndi mtundu umenewo wa peresenti... thuu kuchokera mwa... thuu pa thwelofu a iwo, thuu pa thwelofu. Chabwino, analipo thwelofu a iwo, amenewo angakhale awiri mwa thwelofu, thuu pa thwelofu a iwo anakhulupirira Izo. Iwo anapitirirabe mpaka ku dziko lolonjzedwa, anati, “Mnyamata, ano ndi malo abwino kukhalako.” Yoswa ndi Kalebu wakale, mnyamata, iwo ankadalira Mawu; Mulungu anapereka ilo kwa iwo, anati “ilo ndi lanu.” Iwo anapita kumeneko, iwo anakathyola phava lalikulu la mphesa, ndipo apa iwo akubwera akukokera ilo mmbuyo monga *chonchi*. “Tiyeni, amzanga! Ano ndi malo abwino! Idyani,” mwaona, mphesa pafupifupi kukula *chomwecho*.

<sup>233</sup> Ndipo, oh, bambo, iwo anawawona iwo, anati, “Ah, ife sitingathe kuchita zimenezo.” Pamene iwo anabwerera, iwo anati, “Ayi, m’bale, Mose amene uyu watibweretsa ife mu chipululu muno,” Mzimu Woyera uwu, mwaona, umene iye ankawuyimira, “watibweretsa ife kuno mu chipululu. Ndipo apa ife tiri, utumiki wathu wawonongeka, ndipo ife sitikanachita chinthu chonga chimenecho.”

<sup>234</sup> “Bwererani,” mwaona, “iwo amene anawunikiridwapo kamodzi, kulungamitsidwa mwa chikhulupiriro, kuyeretsedwa.” Mwaona, iwo anadzadutsa guwa lachiwiri ili ndipo anayang’ana uko mdziko lolonjzedwa. “Ife amene tinawunikiridwapo ndipo takhala... tinalawa za mphatso za Kumwamba.” Onani,

“tinalawa” za Izo. Iwo anabweretsanso izo. “Ife tikuwona kuti Izo ndi zolondola. Ife tikuziwona Izo kwenikweni.” “Tinalawa za mphatso Zakumwamba, tinapangidwa ogawana nawo a Chinthu ichi, inu mwaona, Mzimu Woyera uwu, tinadyapo za Iwo.”

<sup>235</sup> “Izo ndi zabwino, mnyamata, tayang’ana pa uyo—mwamuna uyo. Bwanji, ine ndikudziwa iye anali wakhungu, tsopano iye akukhoza kupenya. Tayang’anani pa wachikulire uyo... Mnyamata, chinachitika ndi chiyani kwa munthu ameneyo? Ndani ankaganiza kuti mwana uyo kunja uko wopanda maphunziro... kotaliko iye akuyima ndi Moto pa dziko.” Inu mukuona? Mukuona? Mukuona?

<sup>236</sup> Ndipo kenako nkugwa, mwaona, ndipo ali. . .kuzikonzanso okha, kubwerera ku kulapa, kubwerera kuti akalalikire kulapa mmalo mwa chimene Iye ananena poyamba, kuyikapo a . . .tiyeni ife . . .Inu mukudziwa, za kuyikanso maziko a ntchito zakufa ku kulapa, ndi zina zotero. Ife tidzatero, Mulungu akalola, inu mwaona. Mwaona, ife tidzachita zimenezo. Ife tidzabwereranso ndi kukayika maziko awa mmbuyo uko, koma kubwerera ku kulapa iwoeni, ku kalapa za izo chifukwa chopezeka kumeneko. “Ine ndikupepesa kuti ndinapezeka kumeneko,” ndi kuwerengera Magazi a pangano amene iye anayeretsedwa nawo ngati kuti Iwo anali “chinthu chosayera,” ndipo kuchita monyoza ntchito za chisomo. Iye wapita, m’bale! Ndizo zonse. Iye watha. Mukuona?

<sup>237</sup> Chabwino, tsopano, onani, ndi zosatheka kuti mwana wosankhidwa achite zimenezo. Iye sachita zimenezo. “Nkhosa Zanga zimadziwa Liwu Langa.” Ngati izo ziyitanidwa ku Kenani kapena kulikonse kumene kuli, izo zidzapita. Mukuona? “Nkhosa Zanga zimadziwa Liwu Langa.”

[Mbale akufunsa, “**Ndipo iwo akuyenera kukhulupirira Machitidwe 2:38, nawonso, sichoncho iwo?**”—Mkonzi].

<sup>238</sup> Izo zingatenge izo, chidutswa chirichonse cha Lemba, kutenga Izo zonse. Ndiko kulondola ndendende, m’bale.

**114. Kodi alipo awiri, kodi—kodi pali mitundu iwiri yosiyana ya malirime a m’Baibulo? Kodi pali kusiyana mu malirime olankhulidwa mu pemphero lamseri, ndi mu tchalitchi momwe kumasulira kumafunikira? Pa Tsiku la Pentekoste malirime anamvedwa ndi anthu amafuko osiyanasiyana; koma pa Akorinto Woyamba 14:2, malirime osadziwika anayankhula kwa Mulungu, osati kwa munthu. Akorinto Woyamba 13:1 amasonyeza kwa munthu woteroyo . . . (A-k-o, ine ndikuganiza ndi Akorinto 13, ndi chiyani . . .) . . . kwa munthu woteroyo ndi kwa ena a angelo.**

<sup>239</sup> Oh, inde. Mukuona? Chabwino, izo . . .Tsopano, m’bale, aliynse amene inu muli, inu—inu mwadziyankha nokha apa. Mukuona? Onani:

**Kodi alipo malirime awiri osiyana?** (Alipo malirime ambiri osiyanasiyana. Mukuona?) **Kodi alipo malirime awiri osiyana mu Baibulo, malirime awiri osiyana?**

<sup>240</sup> Pa Tsiku la Pentekoste fuko lirilonse pansi pa Kumwamba linali kumeneko ndi malirime. Mukuona? Chabwino.

**Ndipo kodi pali kusiyana pakati pa malirime oyankhulidwa mu pemphero lamseri ndi mmatchalitchi mmene kumasulira kumafunikira?** Inde.

<sup>241</sup> Paulo analankhulanso cha apa mu Akorinto kumene inu mumafunsa apa, ndipo iye anati, “Pali malirime a angelo ndipo pali malirime a anthu.” Tsopano, malirime a angelo ndi pamene munthu akupemphera kwa iye—kwa iye ndi Mulungu, yekha. Koma pamene iye akuyankhula a—chinenero, icho chikuyenera kutanthauziridwa mu tchalitchi, kwa kumangiriza kwa mpingowo. “Iye amene ayankhula mu lirime losadziwika adzimangiriza yekha; koma iye amene ayankhula... iye amene anenera amangiriza mpingo.” Chotero iye anati, “Ine kulibwino ndiyankhule mawu asanu ndikumvetsa kuposa teni sauzande mu lirime losadziwika, kupatula, pokhapokha patakhala kumasulira.” Ndiye ndi—izo zimalankhulidwa ndiye mwa uneneri umene ukumangiriza. Mukuona chimene ine ndikutanthauza?

<sup>242</sup> Tsopano, a... Tsopano, pali malirime awiri osiyana, anthu ndi angelo. Mukuona? Ndipo Paulo anati, “Ngakhale ndingayankhule malirime a anthu ndi angelo,” onani, awiri onse anthu ndi angelo, malirime awiri onsewo, amodzi amene sanga...

<sup>243</sup> Tsopano, pamenepo ndi pamene anthu Achipentekoste, anthu a umboni wa malirime amene amati, anandiuza ine, iye anati, “Tsopano, M’bale Branham, inu mwasokonezeka.”

<sup>244</sup> Anati, ine ndinati, “Chabwino, ngati inu mukuzitenga izo molingana ndi Machitidwe 2:4, ndiye aliyense anakumvani inu mukuyankhula mu chinenero chimene iwo anabadwiramo.”

“Oh!” iye anatero. Ndipo “Ayi! Ayi!” iye anatero.

Ine ndinati, “Ndithudi. Inde, bwana.”

<sup>245</sup> Anati, “Tsopano, M’bale Branham, inu mwangosokonezeka.” Anati, “Inu mukukamba za...” Anati, “Pali malirime a ‘angelo.’ Ameneyo ndi mngelo wa Mzimu Woyera amene amabwera pansi ndi kudzayankhula kudzera mwa inu.”

<sup>246</sup> Tsopano, izo zikumveka bwino, mwaona, izo zikumveka ngati izo zikhoza kukhala zoonza kwambiri, koma izo zonse si Choonadi. Pamene Satana anamuuza Eva, “ndithudi inu simudzafa,” icho chinali... iye anamuuza iye zoonza zambiri, koma icho sichinali Choonadi. Mukuona?

247 Tsopano, anati, “‘Anthu ndi angelo,’ ndipo mngelo amene amamukamba anali. . .”

248 Tsopano, tiyeni tiwone momwe izo sizingavine ndi Lemba. Mukuona? Tsopano, izo “sizingagwirizanike,” ine ndikutanthauza kuti ndinene. Mundikhululukire ine, sindimafuna kunena kuti “sizingavine” ndi Malemba. Ndikutanthauza “kugwirizanika” ndi Malemba, kapena “kutsatira, kugwirizanitsa” ndi Malemba ndiwo mawu oyenera.

249 “Tsopano, munthu akuyankhula ndi malirime a angelo,” iye anati, “amenewo ndi malirime a Mzimu Woyera amene” iye anati, “tsopano, pamene inu, ife, iwo analandira Mzimu Woyera.”

Ine ndinati, “Kodi . . . Ndi liti, kodi inu munawulandira Iwo kuti?”

250 Chabwino, iye anandiuza ine ndendende malo ake, miniti ndi ora. Ine sindikukayika koma chimene iye anachita. Mukuona? Ine ndiribe. . . Ine si woweruza wake. Mukuona? Iye anati, “Pamenepo ndi pamene ndinayankhula izo.” Iye ankawadziwa ndendende malowo. Anati, “Chinachake chinachitika kwa ine.”

251 Ine ndinati, “Ine ndikukhulupirira izo. Mukuona? Koma apobe umenewo sunali umboni wa Mzimu Woyera kwa iwe, mwana.”

“Oh, inde!” Anati, “Uwo, sunali iwo!”

Ndipo, “Ayi.”

Iye anati, “Tsopano, penyani, ine ndikufuna kuti ndikuuzeni inu chinachake, m’bale.”

252 Ine ndinati, “Kodi anthu mwa omvetsera anu, mpingo umenewo mu Indianapolis kumene inu munati munalandira Iwo, kodi anthu amenewo anakumvani inu mukuyankhula mu Chingerezi kuwauza iwo za chiukitsiro ndi mphamvu ya Mulungu ndi chirichonse?”

Iye anati, “Bwanji, ayi! Ine Ndinayankhula mu—mu malirime osadziwika.”

253 Ine ndinati, “Inu simunachite izo molingana ndi Machitidwe 2:4, chifukwa chirichonse. . . panalibe mawu amodzi osadziwika. ‘Ife tikumumva munthu aliyense mu chinenero chatu.’”

254 “Oh,” iye anati, “M’bale Branham, ine ndikuwona pamene inu mwasokonezeka.” Iye anati, “Inu mwaona,” iye anati, “pali malirime amene ali malirime a angelo, pamene iwe ulandira Mzimu Woyera,” anati, “ndiye umayankhula mmalirime ndipo palibe amene akuyenera kuwathanzuzira iwo, umenewo— umenewo ndi Mzimu Woyera ukuyankhula. Mukuona? Komano umakhala ndi mphatso ya malirime, ndipo iwo ndi oti azitanthauziridwa.”

<sup>255</sup> Ine ndinati, “Ndiye kuti uli ndi ngolo patsogolo pa kavalo. Pa Tsiku la Pentekoste iwo anayika ngolo patsogolo pa kavalo. Iwo asanalandire Mzimu Woyera, malirime osadziwika, iwo anayankhula mu malirime omwe ankamveka.” Mukuona? Kotero izo kwenikweni . . .

<sup>256</sup> Pali malirime awiri osiyanasiyana. Malirime a angelo, ameneyo ndi munthu mu pemphero lamseri kunja uko kwinkakwaka akuyankhula kwa Mulungu, akuyankhula kwa Mulungu mu malirime a angelo. Ine ndikhoza kungokubweretserani inu chochitika pompano, koma ndiribe nthawi. Inu mukukumbukira pamene mkazi anabwera mnyumba yoyankhuliramo uko, kumene Dokotala Alexander Dowie amachokera, Zion. Mukundikumbukira ine kumusi uko? Ndipo Billy ananditsatira ine kumusi uko kuti adzanditenge ine kuti ndipite ku msonkhanowo, ndipo ine ndinati, “Billy, bwerera uko.” Ndipo ine . . .

Iye anati, “Inu mukulirira chiyani? Winawake anali pano?”

<sup>257</sup> Ine ndinati, “Ayi, bwana. Iwe ubwerere, ukamuze M’bale Baxter kuti alalikire usikuuno.”

<sup>258</sup> Ndipo ndinagwada pansu ndipo ndinati, “Ambuye, chavuta ndi chiyani ndi ine?”

<sup>259</sup> Ndipo zonse mwadzidzidzi ine ndinamva Winawake pakhomo, akuyankhula mu zinenero zina. Ine ndinaganiza . . . Icho chinali Chijeremani. Ine ndinaganiza, “Chabwino, munthu ameneyo wabwera kudzamutengera iye . . .” Ine ndinaima, inu mukudziwa, ndikupemphera, ine ndinamumvetsera iye atayima pamenepo monga chonchi. Ndipo ine ndinaganiza, “Chabwino, kodi munthu ameneyo adzamvetsa bwanji zimenezo?” Chifukwa ine ndimamudziwa munthu amene amayendetsa motelo imeneyo, pafupifupi mailosi faivi kuchokera mu mzinda, inu mukudziwa. Ine ndinkayenera kupita kunja uko (anthu ochuluka kwambiri mozungulira), tauni yang’ono. Ine ndinati, “Chabwino, izo ndi zachirendo. Uh.” Ndipo ine ndinati, “Apo . . . Chabwino, mnyamata, kodi iwe unamvapo a . . . chimene . . . Munthu ameneyo amalephera nkomwe kuti apume, nkomwe.” Mwaona, ine ndinkaganiza zimenezo, mozama pamene iye anali kuyankhula! Chabwino, ine ndinati, “Chabwino, izo, bwanji, ndinali ine!” Chotero ine ndinangokhala chete kwenikweni, mwaona, sindinanene chirichonse . . . ndinangokhala chete kwenikweni. Patapita kanthawi Iye anamaliza kuyankhula, ndipo, pamene Izo zinatero, izo zinamveka ngati ndikanakhoza kuthamanga kudutsa gulu lankhondo ndi kudumphira pa khoma.

<sup>260</sup> Ndipo ine ndinatuluka ndipo Billy anali akutuluka pa chipata ndipo ine ndinamukuwira iye, “Dikira miniti!”

<sup>261</sup> Iye anabwerera, iye anali akumwa chakumwa cha soda. Ndipo iye anati, “Adadi, vuto ndi chiyani?”

262 Ine ndinati, “Dikira miniti yokha, miniti yokha, ine ndipita ndi iwe.”

263 Ndinayamba kusukusula nkhope yanga mwaliwiro kwenikweni. Iye anati, “Vuto ndi chiyani?” Iye amadziwa bwino kuposa kuyankhula nane, popita ku msonkhano. Iye anati, “Vuto ndi chiyani?”

264 Ine ndinati, “Palibe, palibe, palibe, nkomwe. Ingopitirira ku msonkhano.”

265 Iye tinapitirira mpaka ku msonkhano, M'bale Baxter anali atakhala pamenepo akuyimba, “*Palibe chirichonse pakati pa moyo wanga ndi Mpulumutsi.*” Iye analowa, iye anati, “Psyii! Ndimaganiza kuti inu simukubwera!”

Ine ndinati, “Sh.” Ndinapita pamwamba ndipo ndinangoyamba kulalikirira.

266 Pamene ndinamaliza, pafupifupi nthawi imene ndinamaliza kulalikirira, chabwino, mnyamata, winawake amakhala ngati akutenga kuseri kwa chipinda, kuseri uko mchipinda choyankhuliramo chachikulu icho. Anakokera choyankhulira chowonjezera kumbuyo uko, ndipo uko kunali mkazi kumbuyo uko akungoyenda chokwera ndi chotsika mkanjirako, akufuula mokweza momwe iye akanafuulira.

267 Ndinadzapeza kuti, iye anali ndi TB, ndipo anali atachoka ku Twin Cities, Saint Paul, ambulansi sikanamubweretsa iye chifukwa iwo amawopa kuti angaphulitse mapapu ake. Adokotala anati, “Chirichonse, mapapu ake anali ngati malesa a uchi,” anati, “ngati iwo angasweke konse iye akanafa. Izo zikanakhala zonsezo.” Ndipo oyera ena anatenga galimoto ya Chevrolet yakale ya '38, ndipo anatenga mpando wakumbuyo ndipo anawukonza iwo, anamuika iye mmenemo ndipo anali panjira. Ndipo iwo anamenya bampu laling'ono kapena chinachake kumusi uko, ndipo iye anayamba kuwukha magazi, ndipo iye anayamba kulavula magaziwo, ndi iye. . . iwo ankadutsa mu mphuno zake ndi chirichonse monga choncho. Iye anayamba kufooka ndi kufooka, ndipo potsiriza. . . Iye sankafuna kufera mu galimoto, anawauza iwo kuti ayime ndi kumuyika iye pa udzu.

268 Iwo anamutulutsa iye. Ndipo onse anali atayima pa iye, akupemphera, ndipo mwadzidzidzi iye anati chinachake chinamukhudza iye ndipo anadzuka. Ndipo anapita kutali, akufuula chotsika msewu umenewo, molimba momwe iye akanathera. Apa iye anali ku tchalitchi, akungoyenda chokwera ndi chotsika mkanjirako.

269 Ine ndinati, “Mlongo, imeneyo inali nthawi yanji?” Ndendende basi nthawi yomweyo imene Mzimu Woyera umayankhula kudzera mwa ine. Chimenecho chinali chiyani? Mphatso.

270 Chimenecho ndi chiyani—oposamu yakale ija itagona kumtunda uko pa chipata kuti apemphereredwe? Chinyama chosazindikira, osati ngakhale solo, sichimadziwa chabwino ndi cholakwika; mwaona, chiribe solo, (chiri ndi mzimu), chiribe solo kwa icho.

271 Icho chinali chiyani? Mzimu Woyera ukupanga kupembedzera. Mulungu anatumiza mphatso ku dziko lapansi, ndipo Mzimu Woyera sunathe kudikira kenanso chotero Iye anangobwera kudzanditenga ine ndipo anayamba kuyankhula Yekha monga choncho, kubwerera Yekha, kupanga kupembedzera Yekha. Ndipo pamene ife tinayang’ana nthawi, pa miniti yomweyo imene iye. . . iwo anamuyika iye pa bwalo monga choncho, iwo ankafuna kuti awone. . . Chifukwa iwo ankadziwa kuti iye amafa, iwo ankayenera kuti adzanene nthawi imene iye anafa. Inali miniti yomweyo imene Mzimu Woyera unagwera pa ine kuntunda uko ndi kuyamba kupanga kupembedzera, zoyankhula, mawu, sindingathe kuwamvetsa iwo, mwaona, monga choncho, kupereka zoyankhula. Umenewo ndi Mzimu Woyera ukuyankhula.

272 Ine sindinkayenera kuti ndidziwe zimenezo. Mwaona, sindinatero. Ameneyo anali iye. . . mwinamwake mngelo wake. Ife tifika kwa izo mu maminiti pang’ono, mwaona, amene anabwera kumeneko ndi kudzapereka uthenga umenewo, inu mwaona.

273 Tsopano—tsopano, ndiko—uko nkulondola. Pali malirime awiri osiyana, amodzi a iwo akuyenera kukhala. . .

274 Kodi pali funso? Chabwino, ndikuyesera kudziwa zomwe Mulungu akunena, inu mwaona. Tsopano, ine ndikanati—ine ndikanati, M’bale Stricker, mu zimenezo, mokhudzana ndi zimenezo, yesetsani kusaganizira za zimenezo, mwaona. Mungolola Mzimu uzilankhula Iwowokha. Musamayesere kuzimvetsa izo, mwaona, chifukwa mungodzipereka nokha kutali kwa Mzimu. Mukuona? Chifukwa inu mukuyesetsa ku—ku—kunena, “Hei, inu mukuti chiyani?” Mukuona? “Hei, mukuyankhula ndi ine? Huh?” Inu mwaona, iye. . . mwaona, iye akuyesetsa.

115. Tsopano. **Kodi ndi zabwino kuti munthu aziyankhula ndi malirime pamene akuwapempherera ena pa guwa** [Malo opanda kanthu pa tepi—Mkonzi]. **popanda kutanthauzira?** [Malo opanda kanthu pa tepi.]

275 Ndiroleni ine ndiwone zomwe ndinalembe pa ilo, ine ndikuyenera kuyang’ana. Ngati palibe wotanthauzira, aloleni iwo akhale chete. Mu Akorinto Woyamba, mutu woyamba. . . mutu wa 14 ndi ndime ya 28. Ndani ali ndi Baibulo? [M’bale akawerenga Akorinto Woyamba 14:28—Mkonzi].

[. . .ngati palibe womasulira, muloleni iye akhale chete mu mpingo; . . .]

276 Chabwino. Tsopano, ngati palibe wotanthauzira, nthawi iliyonse mu tchalitchi, kulikonse mu tchalitchi, khalani chete ngati palibe wotanthauzira.

277 Pa guwa, chinthu chokhacho chimene winawake. . . Nthawi zambiri mumamva za anthu akupita ku guwa. Ine ndinamumva m'bale wofunika posachedwapa pa guwa, anangopita pansi ndi kumamugwedeza winawake ku nsana, ndipo kenako nkumayankhula mu malirime iwoeni, kumayankhula iwo ngati iwo amayesera kuti awasonyeze iwo choti achite. Mwaona, ndiko kukhala ngati kubweretsa Mzimu Woyera mopeka (kuyesetsa kutero) kwa anthu. Musamachite zimenezo. Mukuona? Chinthu choyenera kuchita ndi kungomusiya munthu ameneyo yekha. Aloleni iwo akweze manja awo mmwamba mpaka Mzimu Woyera ubwere, inu mwaona. Mukuona? Chotero izo—izo—izo ndi zolakwika. Ayi, iwo akuyenera kukhala chete mu mpingo, inu mwaona.

278 [M'bale akufunsa, "M'bale Branham?"—Mkonzi]. Inde, m'bale. ["Tinene kuti munthu anali mu msonkhano ndipo—ndipo pakutha pa msonkhano, kawirikawiri pamene uthenga ubwera, munthu amene ali ndi mphatsoyo, amatha kudziwa, kapena akhoza kusiyanita pakati pa—mngelo. . . lirime la mngelo kapena uthenga umene umabwera kudzera mwa iye?"]

279 Tsopano, tiyeni tiwone. Tsopano. . . [Malo opanda kanthu pa ngati—Mkonzi]. . . bola ngati angamabwere muno ndipo nkudzachilemba chinthu chimenecho, kudzachiyika icho pa desiki langa. Mukuona? Ndipo ine nkuwerenga izo monga chonchi. Koma pamene ndinadzalowa mchipinda chimenecho uko, m'bale, izo zinali zonse za izo. Mukuona?

280 Ndipo iwo asanabwere muno, iwo amayima kumbuyo kuno ndipo aliyense ali chete basi momwe akanathera. Ndipo mlongo amakhala ali pamenepo, Mlongo Irene, pamenepo pa—pa guwa, akuyimba pamenepo, akuyimba *Kumusi pa Mtanda*. Ife sitikana. . . Othandizira amangoyenda kumbuyo ndi mtsogolo." Akawona aliyense akuyankhula, iwo amati, "Shii, shii, shii." Mukuona? Ndipo ngati ana apezana. . . Iwo amakhala pansi mokoma kwenikweni ndipo nkumati, "Nyumba ya Ambuye, wokonedwa. Inu simuyenera. Inu muyenera kumakhala ndi khalidwe m'nyumba ya Yehova."

281 Ndipo mwamuna ndi mkazi, ndi onse a iwo, iwo amawalola iwo kupachika zikhotho zawo mmwamba ndi zinthu monga choncho. Winawake apa pa khomo kuti aziwawona iwo mwamsanga pamene chitseko chatsegulidwa. A. . . ndipo chirichonse chakonzeka kuti chizipita, inu mukudziwa, kuyika mpingo moyenera. Aliyense kuwapezera iwo mpando ndi kuwona ngati iwo akhala pansi.

282 Ndipo ine ndinali mchipinda, ndikupemphera, ndinakhala ndiri mmenemo mwinamwake kuyambira thuu kapena firii



koloko madzulo amenewo. Palibe amene anandisokoneza ine. Ine ndinapita kumeneko ndi uthenga wanga.

<sup>283</sup> Ndipo kenako pa nthawi yoti tiyambe, wotsogolera nyimbo anayambitsa nyimbo, “Tiyeni titsegule ku nyimbo nambala *yakuti-ndi-yakuti*,” monga, *Pa Mtanda pamene Mpulumutsi wanga anafera*, kumapitirira monga choncho, inu mukudziwa, ndi kumapitirira nayo monga choncho. Kenako pamene inu muyimba pafupifupi zapadera ziwiri. . .Ife sitimayika nthawi yochulukwa kwambiri mu kuyimba; ndi Mawu. Ngati iwo ali ndi kuyimba nyimbo, izo ndi zomwe iwo amakhalira ndi kuyimba nyimbo kwanthawi konseku. Ndife—ndife. . .Mawu ndi chinthu chofunikiracho chimene anthu amabwerera kumeneko, iyo ndi nyumba yodzakonzedwerako.

<sup>284</sup> Ndipo kenako mwinamwake wothandizira, monga M'bale George, M'bale George DeArk, amaimirira ndi kupereka pemphero. Ndipo kenako timakhala ndi yapadera, monga yoyimba mmodzi kapena chinachake chonga icho. Ndipo kenako inafika nthawi, winawake amandidziwitsa kuti inali nthawi yoti ndituluke. Ngati izo zitero, chabwino, ine ndimatulukira mwatsopano pansu pa kudzodza. Mukuona?

<sup>285</sup> Chabwino, mwinamwake sabata imeneyo iwo anali ndi msonkhano kwinakwake kuno mu mpingo, anali ndi msonkhano wawowawo. Mwinamwake msonkhano usanatsegulidwe nkomwe usiku umenewo, iwo anali ndi msonkhano. Ndipo apa izo zinali. . .Ndiri nazo apa, ndikuti, “Zalembedwa apa pa pepala ili kuti kukubwera nkuntho wina wake udzadutsa mdziko lino sabata ya mawa,” kapena chinachake, chinthu, inu mukudziwa, chinachake chonga icho chichitika. “Izo zinalembedwa, zinayankhulidwa mmalirime, ndi kutanthauziridwa ndi oyera awiri apa mpingo pano, M'bale *Wakuti-ndi-wakuti* ndi M'bale *Wakuti-ndi-wakuti*. Mboni ziwiri za izo zinapereka umboni apa, iwo ali ndi maina awo alembedwa apa, kuti izo zinalembedwa kuti ‘zidzakhala za Mulungu,’ ndi *zakuti-ndi-zakuti* ndi *zakuti-ndi-zakuti*.” Limenelo ndi gawo langa loyamba.

<sup>286</sup> Kenako ine ndimati, “Chabwino, ife tikonzekera izi, aliyense akhale mu pemphero. Mukuona? Tsopano kodi pali chopempha chapadera, aliyense?” Inu mukudziwa. “Tiyeni tipemphere.” Amayima ndi kupemphera. Molunjika kumene ku Mawu, mpaka ku Mawu.

<sup>287</sup> Kenako mwamsanga msonkhanowo ukatha, kuyitanira kuguwa kunapangidwa. Mukuona? Kuitanira paguwa kunali kumene ife tinkachitapo mwamphamvu, kuyitanira paguwa, kuwatengera anthu ku guwa. Ndipo kenako kuyitanira kuguwa kuja kukatha, mwinamwake ndiye ine ndimapempherera odwala, mwaona, kapena chinachake chonga icho.

288 Msonkhano wonse umatengedwa chifukwa mzimu wa aneneri umamumvera mneneri.

289 Ndicho chimene ine ndimaganiza za. . . Inu mukukumbukira usiku umene ine ndinawona masomphenya pamene mngelo anabwera akuyenda kumabwera kwa ine? Ine ndinali nditakhala pamenepo mchchipinda, ndikuganiza. Pafupifupi, oh, mkati mwa usiku, ndikuti, “Mzimu wa aneneri ndi. . .’ Izo zingakhale bwanji?” Ine ndinayang’ana pa Kuwala kuja kukuthwanima, ndipo apa Iye anabwera akuyenda kudutsa pamenepo mpaka kumene ine ndinali. Mukuona? Pamenepo ndi pamene Iye anandituma ine apo pomwe, mwaona, ku misonkhano iyi.

290 Tsopano, ayi, ndi—munthu amene akupereka uthengawo. Ilo, funso lanu ndi chiyani, ine ndikukhulupirira, “Munthu amene akupereka uthengawo, angakhale iye. . .kodi—kodi munthu amene akupereka uthengawo, iye angadziwe kuti anali mngelo wa Ambuye kapena ayi?”

291 [M’bale akuti, “Tsopano, funso linali, inu mukuti pali malirime a angelo. . .” Malo osajambulidwa pa tepi—Mkonzi]. Ine sindikuganiza kuti iye angathe. Tsopano, ndi momwe ife tazimvetsera izo tsopano. Koma, onani, pamene ife tifika momwe ife tikuyenera kukhalira, kumene iwo amakhala ndi msonkhano wachizolowezi wa izo, kuwalola. . .

292 Mwaona, uliwonse wa iwo ndi utumiki. Kunena, *inu* mumayankhula mmalirime, *iy*e amatanthauzira, ndipo *iy*e amayankhula mmalirime, *iy*e amalosera; inu ndi osonkhana chabe pano, mpingo, komabe inu muli ndi utumiki ndipo inu muli ndi chinachake. Inu mukuyesetsa kuti muwuthandize Ufumu wa Mulungu, kuwuchitira iwo chinachake, mwaona, ndipo chotero inu abale muzikomana pamodzi. Ndi chifukwa chake azibusa, monga chonchi, timakomana pamodzi, ife tiri ndi chinachake chofanana. Inu abale muzikomana pamodzi, muziphunzira Malemba, ndi kuyankhula mmalirime ndi kutanthauzira, ndi kupereka mauthenga, inu mwaona.

293 Koma, tsopano, ngati munthu uyu, ndiye, ngati iye azindikira. . .Iye wakhalapo ku msonkhano, iye ali ndi mphatso ya malirime. Chabwino, iye akafika ku msonkhano, iye amayankhula mmalirime koma palibe kutanthauzira kumene kumaperekedwa, wotanthauzira samamva izo.

[M’bale akufunsa, “**Kodi munganene kuti anthu amenewo amamangiriza Thupi, koma maudindo monga ngati abusa, aphunzitsi, ndi izo, amapangitsa Thupi kukhala langwiro?**”—Mkonzi].

294 Inde, icho ndi chifukwa chake, ungwiro. Mukuona? Izi zimaperekedwa kwa ungwiro, inu mwaona. Ine ndikukhulupirira, a—a—Mizimu imaperekedwa kuti ipangitse ungwiro, ungwiro wa mpingo.

<sup>295</sup> Tsopano, iwo, anthu awa amene amayankhula, iwo ndi odzazidwa-Mzimu, palibe kukayikira. Tsopano, apa pali mwamuna, mwinamwake iye akuyankhula muno mu msonkhano, ndipo iye akupereka... Tsopano, iye ali pamaso pomwe pa otanthauzira, mwaona, ndipo komabe palibe amene akumva kutanthauzirako, pali chinachake cholakwika. Wotanthauzira sangachitire mwina, mwaona. Iye— iye akuyenera kutanthauzira mwa kudzodza mofanana ndi amene akuyankhula izo. Ndipo iye akhoza kukhala ndi mphatso yeniyeni yolankhula mmalirime, koma iye alibe mphatso ya malirime, chinenero. Mwaona, iye. . .

<sup>296</sup> Ndiyeno chinthu choti iye achite ndicho, pamene iye agwiritsa ntchito lirime ili, ndiye iye amawona... Tsopano, chimene iye—iye sakuyesera... Ngati iye akuyesera kudzikweza yekha kachiwiri, iye ndi wodzikweza. Iye alibe... Iye—iye akulakwitsa kuyamba ndi kuyamba, inu mwaona, iye sadzapita kulikonse. Mwaona, inu mukuganiza, “Chabwino, Mulungu adalitsike, munthu ameneyo sakufuna basi kutanthauzira malirime anga. Ndizo zonse zomwe zilipo kwa izo.” Tsopano, mwaona, iye akulakwitsa kuyamba ndi kuyamba. Pamenepo iye ali ndi—ali ndi cholinga cholakwika, chokhumba cholakwika. Mukuona?

<sup>297</sup> Koma ngati iye ali wokoma ndi wodzichepetsa, kuti, “Chabwino, mwinamwake Ambuye sanafune kundigwiritsa ntchito ine mu utumiki Wake. Koma komabe ine... Iye amangodalitsa solo yanga. Iye akufuna kundimangiriza ine, kuti ndidziwe kuti ine ndimakhala pafupi ndi Iye pamene ine ndikuyankhula mmalirime. Chotero ine ndipita m'munda wa maapulo, ‘O Mulungu!’ Ndipo mphamvu imayamba kugwera pa ine ndipo ine ndimayamba kuyankhula mmalirime. Ine ndimabweramo nditatsitsimutsidwa, inu mwaona.” “Oh, Inu mwaona, Inu mukuyankhula kwa ine, Ambuye, Inu mukungondiyika ine pamzere poyankhula mmalirime.” Mukuona? “Ndipo, Ambuye, lero ine ndimayenera kuti ndiyankhule kwa munthu ameneyo. Ndikhululukireni ine pa izo, Ambuye. Ine—ine—ine ndinadutsa chinachake chimene sindimayenera kutero. Atate, chonde ndikhululukireni ine.” Ndipo, molunjika, izo zimapita kutali kuyankhula mmalirime. “Ah, psyii, ndikumverera bwinoko za izo tsopano!”

<sup>298</sup> Inu mwaona, izo zonse nzabwino. Mwaona, yanu—mphatso yanu si yoti igwiritsidwe ntchito mu mpingo, koma ndi yoti ikumangirizeni inu. “Iye amene ayankhula lirime losadziwika (losadziwika) adzimangiriza yekha.” Mukuona? Tsopano, ngati palibe wotanthauzira, ndiye... Mukuona chimene ine ndikutanthauza? Mwaona, ndi zimenezotu. Chotero iye sangadziwe iyemwini. Iye basi... Koma iye adzadziwa pamene iye ali limodzi.

Tsopano, tsopano inu mukuyenera kungozisiya izo kuti

zipite pamodzi, inu mwaona, ndicho chinthu chokhacho chimene inu mungachite mpaka inu mutalekanitsa icho. Chimenecho ndi chifukwa ine ndikuganiza icho. . .

### 116. Tafotokozani Akorinto Woyamba 14:5.

<sup>299</sup> Ndani wapapeza pamenepo mwamsanga? Mmodzi wa inu wapapeza? [Malo opanda kanthu pa tepi. M'bale akuwelenga Akorinto Woyamba 14:5—Mkonzi].

[. . . onse anayankhula ndi malirime, koma makamaka kuti munenere: pakuti wamkulu ndi iye amene anenera kuposa iye amene ayankhula ndi malirime, pokhapokha iye amasulire, kuti mpingo ulandire kumangirizidwa.]

<sup>300</sup> Chabwino. “Ine kulibwino. . . Ine ndikanakonda kuti inu nonse mukanamayankhula ndi malirime.” Paulo ankayesera kunena. . . Monga mpingo, inu—inu mukhale mpingo wanga. Ina ya mipingo Paulo siinali yayikulu monga mamembala ambiri monga amene ine ndiri nawo pano. Uko nkulondola, nthawizina teni kapena thwelofu. Mukuona? Mukuona? Tsopano, tsopano iye anati, “Ndikanakonda kuti inu nonse muziyankhula ndi malirime.” Izo zimakudabwitsani inu?

<sup>301</sup> Mwaona, pamene a—a—mpingo umene. . . mu Machitidwe 19, ine ndikukhulupirira iwo unali ndi pafupifupi mamembala thwelofu mmenemo. Mukuona? Basi waung’ono kwambiri, utumwi, inu mwaona. Chotero nthawizonse zakhala ziri mwa apang’ono, mwaona. Ndipo ine ndikuganiza izo zinanenedwa ndipo apo panali pafupifupi ochuluka kwambiri, amuna thwelofu ndi akazi, inu mwaona, mmenemo.

<sup>302</sup> Tsopano, ngati inu—mukuwona apa, iye anati, “Ndikanakonda kuti inu nonse mukanamayankhula ndi malirime. Ine—ine ndikanakonda inu nonse mukanamayankhula, nonse mukanamayankhula ndi malirime, kungodzadzidwa kwambiri ndi Mzimu Woyera mpaka inu kumangoyankhula ndi malirime. Koma” anati “Ine ndingakonde kuti inu munenere; pokhapokha izo zitakhala ndi kutanthauzira, pangakhale kutanthauzira.”

<sup>303</sup> Kodi zimenezo zikuwerengeka bwanji pamenepo? Ndani. . . Kodi muli nazo pamenepo, kulondola. . . ? . . . Tiyeni tiwerengenso izo. Tsopano mveterani:

<sup>304</sup> [M'bale akuwerenga Akorinto Woyamba 14:5—Mkonzi].

[Ndikanakonda kuti inu nonse muyankhule ndi malirime, . . .]

Tsopano gwirani zimenezo miniti, “Ine ndikanakonda kuti inu nonse mukanamayankhula ndi malirime.”

[. . . koma makamaka kuti muzinenera. . . ]

“Ine ndikanakonda kuti nonse muzinenera.”

[. . . *pakuti wamkulu ndi iye amene anenera kuposa iye woyankhula ndi malirime, . . .*]

Tsopano gwirani izo miniti.

<sup>305</sup> Tsopano, ndi ndani, “Wamkulu kuposa iye amene anenera”? Ndi zomwe inu mumafuna kuti ndiyimepo? [M’bale akuti, “Ine ndimangoti, ‘Izo zinali zosiyana . . . ? . . .’”—Mkonzi]. Eya. Mukuona? Eya. Mukuona? Tsopano, apa ndi pamene . . .

<sup>306</sup> Tsopano, inu mukuti mwachitsanzo, tsopano, ife tiri ndi amuna awiri osaphunzira pakati pathu usikuuno. Iwo sakudziwa kalikonse ka izi, ndipo ine ndikubwera muno ndipo inu nonse muli . . . nkuyamba muno mu msonkhano, ndipo—ndipo inu nkungoyamba kuyankhula mu malirime, aliyense wa inu kumangoyankhula mmalirime, kuyankhula mmalirime, ndi kumayankhula mmalirime, ndi kuyankhula mmalirime. Ndipo, chabwino, ndi chiyani zimenezo? Mwaona, munthu wosaphunzira anena kuti, “Uh! Iwo onse ndi openga!” Mukuona? Koma ngati wina alosera, mwaona, ndiye iye akunena chinachake chimene iye angathe kuchimvetisa.

<sup>307</sup> Tsopano, pitirirani ndipo muwerenge zonse za ilo tsopano. [M’baleyo akupitiriza—Mkonzi].

[. . . *kupatula iye atatanthauzira, . . .*]

Ndi zimenezotu pamenepo. Tsopano, “kapatula,” mwaona. Ine—ine ndikana . . . Iwo amene—amene akunenera ndi aakulu kuposa iye amene akuyankhula mmalirime *kupatula* uyu atapereka kutanthauzira. Tsopano, pitirirani patsogolo, mwaona.

[. . . *kuti mpingo ulandire kumangirizidwa.*]

Ndi zimenezotu pamenepo, mwaona, mpingo umamangirizidwa.

<sup>308</sup> Tsopano, mwa kuyankhula kwina, bwanji, mpingo, munthu uyu. Apa—apa ochuluka *chonchi* awa pano ndi osaphunzira, inu mwangokhala pakati pathu usikuuno; ife tiri ndi msonkhano uwu. Ife tonse tiri muno kufunafuna zathu . . . tikufuna kudziwa za Ambuye, nonse a inu nkungoyamba kuyankhula mmalirime. Palibe amene ananena kanthu, kungoyamba kuyankhula mmalirime. “Ine ndikukufuna inu . . . Ine ndikana . . . Izo zingakhale bwino,” Paulo anatero. “Nonse a inu mukunayankhula mmalirime, izo zikanakhala zabwino.” Koma nanga bwanji ngati ena a inu anenera, kudzuka ndi kudzati, “PAKUTI ATERO AMBUYE, ‘Pali mwamuna wakhala pano ndipo iye ndi mlendo pakati pathu. Dzina lake ndi *John Doe*. Iye amachokera ku malo *akuti-akuti*. Iye wasiya mkazi wake ndi ana foro kumeneko. Iye ali pano usikuuno chifukwa akufuna thandizo. Iye anali ndi dokotala lero ku Memphis, Tennessee. Ndipo iye anati . . . Adokotala anamuza iye kuti ali ndi khansa ya m’mapapo. Iye akufa”?”

309 Iye anati, “Ngati nonse muyankhula mmalirime ndipo osaphunzira nkubwera pakati panu, iye angati. . .kenako iye adzati, ‘Kodi nonsenu si amisala kapena openga?’ Koma ngati wina anenera ndi kuulula zinsinsi za mu mtima, kenako iwo adzagwa pansu, ndikuti, ‘Ndithudi Mulungu ali ndi inu!’” Mukuona pamenepe?

310 Chabwino, tsopano, apa. Tsopano inu mukuyankhula mmalirime, koma wina aperekd kutanthauzira, ndikuti, “PAKUTI ATERO AMBUYE,” pansu pa kutanthauzira, “Pali mwamuna wakhala pakati pathu, anasiya mkazi wake, anali ku Nashville lero,” kapena Memphis, kapena chirichonse chimene chinali, “ndipo iye ali ndi khansa ya m’mapapo. Wabwera muno, ndipo dzina lake ndi *John Doe*,” *Wakuti-ndi-wakuti* monga choncho. Mukuona?

311 “Kupatula izo zitakhala ndi kutanthauzira,” kapena, mwaona, ndiye izo zimapereka kumangiriza. Mukuona? Kenako iwo adzati. . .Kenako munthu ameneyo adzatuluka, ndikuti, “Ndiroleni ine ndikuuzeni inu chinachake, musandiuze ine kuti Mulungu sali ndi anthu amenewo kumtunda uko. Ndithudi! Anthu amenewo sankandidziwa ine nkomwe.” Mukuona?

312 Chotero ife tikufuna mphatso za uneneri *kuphatikiza* mphatso za kuyankhula mmalirime. Koma, mu kuyankhula ndi malirime, mwaona, payenera kukhala ndi kutanthauzira. Ndipo kenako, pamene iwo atanthauziridwa, iwo amakhala ulosi. Mukuona? Iwo ndi ulosi. Tsopano, ine ndiri ndi funso limenelo pano mu miniti, chotero ine—ine ndifika kwa ilo mwamsanga momwe ndingathere. [Malo opanda kanthu pa tepi—Mkonzi].

## 117. Mateyu 18:10.

[M’bale akuwerenga Mateyu 18:10—Mkonzi].

[. . .*kuti musanyozetse mmodzi wa aang’ono awa; pakuti ndinena kwa inu, Kuti kumwamba angelo awo—angelo nthawizonse amawona nkhope ya Atate anga amene ali kumwamba.*]

313 Chabwino. Tsopano, m’bale, aliyense yemwe inu muli, chifukwa palibepo maina, matikiti aang’ono basi, inu mwaona, amene ananena izi. Ine ndikutsimikiza ine. . .

314 Tsopano, inu mukhoza kutenga njira ziwiri za izo, inu mwaona. Koma ndikuganiza kutanthauzira, ngati mutangondifunsa ine, “Fotokozani izi,” momwe ndimatanthauzira izi ndi umu.

315 Tsopano, inu mutsegule ku Akorinto Wachiwiri, winawake, 5:1, amanena izi, “Ngati msasa wapadziko uno upasuka. . .” Inu mukudziwa chimene icho chiri, mwaona. “Ngati msasa wapadziko uno upasuka, ife tiri nawo wina kale,” inu mukudziwa, “ukuyembekezera.” Chabwino.

<sup>316</sup> Tsopano, tsopano Iye akana... Ngati inu munazindikira, mu Mateyu 18:10, Iye anayankhula za kutenga aang'ono "ana." Iwo anali ana aang'ono, tiana tating'ono, zaka zitatu kapena zinayi zakubadwa, anawanyamula iwo. "Iwo anabweretsa kwa Iye ana, mwana." Ana amachokera ku dzina la "mwana." Mwana amangokhala wamng'ono chabe—mwana wamng'ono, osati khanda koma pakati pa izo ndi wa zaka zammadini. Mukuona? Iye sanafikebe pokhala ndi udindo.

<sup>317</sup> Tsopano, Iye anati, "Samalani kuti *musanyozetse*." Ngati inu mungatenge kwenikweni kutanthauzira kwa mawu amenewo, ndi "kuzunza." Mwaona, "Kumuzunza mmodzi wa iwo." Kumuzunza mwana, musamachite zimenezo. Iwo ndi ana, iwo samadziwa. Mukuona?

<sup>318</sup> Ndipo tsopano zindikirani, anati, "Chifukwa iwo... angelo awo nthawizonse amawona nkhope ya Atate Anga amene ali Kumwamba," inu mwaona. Mwakuyankhula kwina, "Angelo awo, awo—amithenga awo, matupi awo, matupi a ungelu amene iwo adzapite akadzamwalira, nthawizonse amakhala pamaso pa Atate Anga Kumwamba." Mukuona?

<sup>319</sup> Tsopano, "Ngati msasa wapadziko uno upasuka, ife tiri nawo wina umene ukuyembekezera kale." Nkulondola uko? Limenelo ndi thupi.

<sup>320</sup> Taonani apa. Ngati ndikanangokhala ndi nthawi yoti ndidutse mu izi! Chifukwa, ine ndikudziwa—ine sindikhala nayo iyo. Koma, apa, ndiroleni ine ndingozipereka izo kwa inu kuti zikhale pa tepi, ndipo inu mudzazipeza izo mulimonse.

<sup>321</sup> Taonani, usiku wina Petro anali mu ndende. Iwo anali ndi msonkhano wa pemphero kumusi ku nyumba ya Yohane Marko, mwaona. Ndipo chotero Mngelo wa Ambuye anabwera, Lawi la Moto lija, Kuwala kunatsika pansu, ndipo Petro ankaganiza kuti iye anali akulota pamene iye anawona Kuwala uku kukubwera kwa iye. Baibulo linati, "Uko kunali Kuwala." Mukuona? Ndipo ine ndikukhulupirira Iye ndi Mmodzi yemweyo amene ali ndi ife, mwaona, Iye anatsika pansu. Ndipo ife timalowa mu vuto lomwelo, mwinamwake chinthu chomwecho chingachitike. Mukuona? Ndipo anabwera mmenemo, ndipo chotero Iye anati, "Bwerani, mupite ndi Ine."

<sup>322</sup> Chotero Petro anaganiza, "Ine ndikulota tsopano, kotero ndingowona chimene loto ili likutanthauza." Chotero iye anayenda pafupi ndi alonda, ndipo anaganiza, "Uh-huh. Tsopano ife tikupitirira, chitseko chinangotseguka chokha." Anatulukira pa khomo linalo, lotseguka lokha. Anapita kudutsa zipata za mzindawo, ndipo izo zinatseguka zokha. Ndipo iye ankaganizabe kuti anali akulota. Kotero pamene iye anayima pamenepo, ndipo anati, "Chabwino, ndine mfulu, kotero ine ndingopita kumusi ku nyumba ya Yohane Marko ndi kukakhala ndi chiyanjano china."

323 Iwo anali kumbuyo uko, “O Ambuye, tumizani Mngelo Wanu ndi kumupulumutsa Petro.”

324 Ndipo pafupifupi nthawi imeneyo chinachake chinamveka [M’bale Branham akugogoda—Mkonzi.] Mtsikana wamng’onyo anapita pakhomo ndipo anati, “Ndi ndani ali mmenemo?” Anakwezera mmwamba kophimba kakang’onoko, anati, “Bwanji, ndi Petro!” Chotero iye anabwerera, anati, “Heyi, inu—inu mukhoza kusiya kupemphera tsopano, Petro ndi uyo apo.”

Iye anati, “Oh, mai! Kazipitirirani,” anati, “ndinu—ndinu—ndinu. . .” Mukuona?

325 [M’bale Branham akugogoda kachiwiri—Mkonzi.] Anati, “Tsegulani! Ine ndikulowa.” Mukuona? Ndipo kotero iye anati. . .

Chotero iye anabwerera, anati, “Ayi, ndi—ndi Petro ali pa chitseko.”

326 “Oh,” iwo anati, “iwo amudula kale mutu wake, ameneyo ndi mngelo wake pakhomopo. Mwaona, kachisi wake wa Kumwamba, iye anali atamulandira kale iye, kuti wapadziko lapansi uyu anali atapasuka, chifukwa iye an kayembekezera Kumwamba kuti iye abweremo.”

327 Chimene ine ndinachiwona tsiku lina mmasomphenya aja, inu mukudziwa, nditawolokera kumeneko. “Ngati msasa padziko lino upasuka, ife tiri nawo wina.”

328 Ndipo ana aang’ono awa amene sanachite tchimo panobe, inu mwaona. . . Mukuona?

329 Pamene mwana akukhala—mwana akuwumbidwa mmimba mwa amayi, mwamsanga iye akaikidwa mmenemo. . . Mukuona? Mukuona? Koma choyamba umakhala mzimu. Ndipo pamene mzimu umenewo ukuyamba kuvala thupi, nyongolosi yaing’ono ya moyo imayamba kuvala thupi, ndipo mwamsanga iye akangogwa kuchokera mu lake. . . Tsopano, mmimba, ndi minofu yaing’ono, yonjenjemera, yogwedezeke. Ife tikudziwa zimenezo. Amenewo ndi makhungu. Chimodzimodzi monga inu mutenge tsitsi la kavalo ndi kuliyika ilo mmadzi, ilo limabwera pamwamba ndipo limasuntha, ndipo inu mukaligwira ilo ndipo ilo limalumpha. Umo ndi momwe mwana amakhalira.

330 Koma mwamsanga akangobadwa m’dziko lino ndi kupuma mpweya wake woyamba, iye amakhala solo yamoyo. Mukuona? Chifukwa mwamsanga pamene thupi lapadziko lapansi likangobadwa mdziko lapansi, pali thupi lakumwamba, kapena thupi lauzimu, kuti limugwire iye. Ndipo mwamsanga pamene thupi lachirengedwe ili lagwa, pali kachisi Wakumwamba akudikirira ilo. “Ngati msasa wapadziko uno upasuka, alipo kachisi wa Kumwamba akuyembekezera iwo.” Mwamsanga basi pamene—pamene mwanayo agwera mu dziko lapansi



mthupi, pali thupi lauzimu limakhala likuyembekezera kuti limulandire iye. Ndipo mwamsanga pamene thupi lauzimu... thupi lachirengedwe lipasuka pamakhala thupi lauzimu likuyembekezera uko. Mukuona? A “fiofane” ife timalitcha ilo, mwaona, fiofane.

[M'bale akufunsa, “**Chabwino, tsopano, thupi ili ndi limenelo a...kodi ilo ndi la kanthawi, loyembekezera chiwukitsiro cha thupi ili?**”—Mkonzi]. Eya. Mukuona? Eya. Oh, inde. [**“Chimenecho ndi chikhalidwe chimene ife tidzakakhalemo mpaka a—chiukitsiro?”**] Uko nkulondola. Mukuona? Mukuona?

<sup>331</sup> Izo sizinawululidwebe kwa ana a munthu. Ine ndikukhulupirira... Ine—ine ndikudziwa kuti ndinaliwona ilo. Mukuona? Koma sindikudziwa kuti ilo ndi thupi lotani, koma ine ndimakhoza kuwamverera iwo mofanana basi monga ine ndinamverera manja anu kapena china chirichonse. Chifukwa, izi ziri pa tepi ndipo mwina inu mudzakhala mukuisewera iyo zaka zambiri ine nditapita. Inu mukuona? Koma... Ndipo icho, chirichonse chimene icho chinali, mwaona, ine ndinali—ine ndinawagwira anthu amenewo ndi kuwagwira iwo, ndipo izo zinali zenizeni basi monga—monga inu muli enieni, ndipo komabe izo sizinali... Iwo sankadya kapena kumwa. Kunalibeko dzulo kapena mawa. Mwaona, iwo unali Muyaya.

<sup>332</sup> Ndipo tsopano pamene kachisi ameneyo... iwo anachoka mmenemo mu thupi limenelo, iwo anabwerera ku dziko lapansi, ndipo thupi la mtundu umenewo iwo anali atavala chisavundi. A—fumbi la dziko lapansi linasonkhanitsidwa mu fiofane imeneyo mwanjira yina ndipo iwo anadzakhalanso anthu, ankayenera kumadya monga iwo ankachitira mmunda wa Edeni. Mukuona? “Koma ngati msasa wapadziko lapansi uno upasuka, ife tiri nawo wina umene ukuyembekezera.”

<sup>333</sup> Chotero ana aang'ono awa amene analibe tchimo, mwaona, analibe tchimo apobe, *angelo* awo, “matupi” awo (limene Petro anabwereramo...) mwaona, linali likuyembekezera. “Kumawona nkhope ya Atate, Kumwamba,” ilo nthawizonse limakhala pamaso pa Iye; “iwo amadziwa zimenezo.” Ndi limenelo.

<sup>334</sup> [M'bale akuti, “Koma izo zinali zovuta pang'ono kumeneko pamene Yesu anati, mu gawo loyambirira la chiwukitsiro Chake, Iye anati, ‘Musandigwire Ine,’ Iye anali asanakwere mmwamba. Ndiyeno pamene Iye anadzalowa mchipinda mmene munali Tomasi, Iye anati, ‘Bwera kuno ndipo udzayike dzanja lako mu mbali Yanga; dzayike chala chako.’”—Mkonzi]. Ndiko kulondola, Iye anali asanakwere mmwamba apobe. [“Ndipo a—kusiyanana kwa awiriwo, kumene mmodzi Iye—Iye anawauza iwo kuti asamukhudze Iye, ndipo uko Iye anamuuza Tomasi kuti abwere adzamukhudze Iye.”] Iye anali asanakwere konse

mmwamba, inu mwaona. Iye . . . [“Pakuti Ine sindinakwere kwa Atate Anga.”]

<sup>335</sup> Uko nkulondola, mwaona, Iye sankayenera kuti akhudzidwe mpaka Iye . . . pambuyo pa chiwukitsiro Chake. Iye anali atabwera kuchokera pa dziko lapansi, inu mwaona. Iye anabwera kuchokera pa dziko lapansi ndipo ankayenda pakati pa anthu, koma Iye anali asanakwere mmwamba. Iye anati . . . Iye anamuza Mariya, Iye anati, “Usandikhudze Ine.”

Iye anati, “Rabboni.”

<sup>336</sup> Iye anati, “Kundikhudza . . . Usandikhudze Ine, pakuti Ine sindinakwerebe kwa Atate. Koma Ine ndakwera kwa Mulungu Wanga ndi kwa Mulungu wanu, kwa Atate Anga ndi Atate anu.”

<sup>337</sup> Ndiyeno usiku umenewo, Iye atapita mmwamba pamaso pa Mulungu, ndipo anawuka kwa akufa, anapita mmwamba pamaso pa Mulungu. Akubwerera, Iye anamuitana Tomasi kuti abwere kudzagwira m’mbali Mwake. Mwaona, Iye anali atakwera mmwamba pamaso pa Mulungu. Uko nkulondola. Chabwino.

**118. Tsopano. Mu Akorinto Woyamba 14, “Tsatirani—tsatirani chikondi, ndipo funani mphatso zauzimu, koma makamaka kuti inu muzilosera.” Webster, akuti, “kulosera: kuneneratu zodzachitika mtsogolo, makamaka mwa kudzodza kwaumulungu.” Kodi uthenga. . . Tsopano iwo . . . izo—izo ndi zomwe Webster ananena ndi zomwe—m’baleyo anafunsa. Kodi uthenga ungatchedwe “ulosi” umene sukunena zodzachitika mtsogolo?**

Ayi, bwana. *Kulosera* ndi kuti “kuneneratu.” Mukuona? Chabwino.

**119. Tsopano. Akorinto Woyamba 14:27, ine ndikukhulupirira kuti mauthenga onse akuyenera kutanthauziridwa ndipo kuti osati kupitirira mauthenga atatu mu malirime adziperekedwa mu msonkhano umodzi.**

<sup>338</sup> Limenelo ndi Lemba. Ine ndazilemba izo apa. Chifukwa, ife sitiri . . . Ife timazidziwa izo ndipo tikuzidziwa izo, inu mwaona. Ndizo . . . Inde, bwana, ndizo . . . akuyenera kukhala motsatizana atatu okha. Umo ndi mu Akorinto Woyamba 14, aponso. Mukuona? Uko nkulondola, “motsatizana atatu.” Tsopano inu muziwone izo mmisonkhano yanu, abale. Tsopano, inu mu—mupeza izo zikubwera tsopano, mupeza kuti anthu ambiri amasangalatsidwa. Ndipo sindikunena kuti iwo alibe Mzimu Woyera, tsopano. Koma, inu mwaona, Paulo anapita kumusi kuti akawukhazikitse mpingo waku Akorinto mu dongosolo. Ife tonse tikudziwa zimenezo, sichoncho ife? Iye ankayenera kuwuyika iwo mu dongosolo. Ndipo iye anati, “Zinthu zonse zichitike mwabwino ndi mwadongosolo.”

<sup>339</sup> Tsopano, ngati inu munazindikira, Paulo, popita uko, iye nthawizonse ankakhala ndi vuto ndi mpingo waku Akorinto. Inu simunamupezepo iye mwanjira imeneyo ku... Iye sananene kalikonse za izo kwa mpingo wa Aefeso, iye amakhoza kuwaphunzitsa iwo chitetezero Chamuyaya. Palibe chirichonse chokhudza chitetezo Chamuyaya mu—mu mpingo waku Akorinto. Iwo nthawizonse anali makanda, akuyesera, “Wina amakhala ndi lirime, wina amakhala ndi salmo.” Sikulondola uko? Mukuona? Ndipo ngati inu mulola osonkhana anu kuyamba pa zimenezo...

<sup>340</sup> Monga Martin Luther, iye anadzadzidwa kwambiri ndi Mzimu mpaka iye anayankhula mmalirime. Iye ananena, mu zolemba zake, iye anati, “Ine ndinayankhula ndi malirime,” iye anati, “koma ndiwaphunzitsa anthu anga zimenezo” anati “iwo adzafunafuna mphatso m’ malo mwa Woperekayo.” Uko kunali kulondola, mwaona, iwo adzakhala akufunafuna mphatso mmalo mwa Woperekayo.

<sup>341</sup> Ndipo chimenecho ndi chimene anthu amapeza, ndiyeno iwo amakhumudwa onse ndi kudzitukumula pamene iwo awalola iwo kuti aziyankhula ndi malirime kapena chinachake chonga icho. Ndipo ngati icho sichiri cha Mulungu, ndiye izo sizitero... zidzakhala zopanda pake. Koma ife...

<sup>342</sup> Tsopano, mipingo yamakono imatembenuza chinthu chonsecho, koma ife sititero. Ife timakhulupirira kuti iyo ndi mphatso ya Mulungu ndipo ikhoza kuyikidwa mmenemo ndi Mzimu wa Mulungu. Nanga bwanji zimenezo, M’bale Roy? Uko nkulondola. Inde, bwana. Kuyikidwa mu mpingo! Iyo ndi ya mu mpingo. Mphatso yoyankhula mmalirime ndi ya mmenemo, mwaona, mu Mpingo wa Mulungu.

<sup>343</sup> Tsopano, tiyeni tiwone tsopano ndendende chimene funso lake linali apa. Linanena, kuti:

**Ine ndikukhulupirira kuti mauthenga onse... (uko nkulondola)... akuyenera kutanthauziridwa, ndipo motsatizana atatu.**

<sup>344</sup> Uko nkulondola, mwaona, chifukwa ngati inu mulola a... Tsopano tiyeni tinene kuti, mwachitsanzo, ngati inu munali ndi msonkhano ndipo ife takhala muno ndi—ndi... Tsopano, izo zikanachita ubwino wanji kumulola *iye* kuti ayankhule mmalirime, *iye* ayankhule mmalirime, *iye* ayankhule mmalirime, *iye*? Bwanji, ife tonse tikanakhala osokonezeka kwambiri ife sitikanadziwa nkomwe chimene ife tinkachita. Mukuona? Mwa kutsogozana atatu, tiyeni... monga, Hollin, iye akuyankhula mmalirime, ngati iye ayankhula mmalirime...

<sup>345</sup> Ndipo pakuyenera kukhalanso wotanthauzira. Tsopano, pakhoza kukhala wotanthauzira mmodzi pokhapokha inu mutatanthauzira lirime lanu lomwe. Tsopano, inu... “Muloleni iye amene ayankhula mmalirime apempherenso kuti

atanthauzire.” Iye akhoza kutanthauzira malirime ake omwe zimene ziri basi ngati—ngati zololedwa basi monga izo ziri kwa wotanthauzira wina. Koma pakuyenera kukhala wotanthauzira mmodzi malirime asana. . . Ngati inu muli ndi gulu la anthu oyankhula mmalirime ndipo palibe wotanthauzira, ndiye mupemphere nokha kuti muthe kutanthauzira chimene inu mu—chimene inu mukunenacho.

<sup>346</sup> Tsopano, musangochita izo kuti mudzitukumule nokha, chifukwa inu mukungodzimangiriza nokha ndiye, inu mwaona. Musamachite zimenezo. Koma muziyankhula mmalirime kuti mukhoze kumangiriza Mulungu, mukhoze kumangiriza mpingo. Inu mwaona, zonsezo ndi za chifukwa chimodzi chachikulu, m’bale. Mphatso izi ndi zomangiriza Mulungu, kuwumangiriza mpingo, kuwabweretsa anthu kwa Mulungu, kuwadziwitsa iwo kuti Mulungu ali nafe. Iye si Mulungu wakufa, Iye ndi Mulungu wamoyo akugwira ntchito pakati pathu. Mukuona?

<sup>347</sup> Ndipo ife tikuyenera kungoyang’ana izo mwatcheru kwenikweni chifukwa, amwene, mdierekezi amadana nazo izo monga chirichonse, inu mwaona, kuwona mphatso zenizeni zoon. Chifukwa mphatso ndi zofooka, ndipo iye akhozadi kukagwira ntchito pa mphatso zimenezo. Munthu, oh, munthu, iye akhoza kwenikweni kutsanzira aliyense wa iwo. Kotero chimenecho ndi chifukwa. . .

<sup>348</sup> Tsopano, taonani, kusiyana kwa pakati pa mphatso ya uneneri ndi mneneri, pali kusiyana kwa mailosi milioni basi. Ulosi usanachitike. . . Munthu amene ali ndi mphatso ya ulosi akhoza kuuzidwa pamaso pa mpingo, awiri kapena atatu ayenera kuti azizindikire izo ndi kunena “izo ndi zoon.” Uko nkulondola. Koma osati mneneri. Mukuona? Mneneri ndi udindo. Mphatso ya uneneri ndi mphatso. Mneneri amabadwa, amakhala ndi PAKUTI ATERO AMBUYE, m’bale, kumangopitirira pitirira. Palibe kanthu mmenemo, mwaona. Ameneyo ndi mneneri. Koma mphatso ya uneneri, imeneyo ndi mphatso, inu mwaona. Winayo ndi udindo wa Mulungu, mmodzi winayo ndi mphatso ya Mulungu. Mukuona? Ndipo ndiko kusiyana kwake.

<sup>349</sup> Tsopano, mauthenga, titi, tsopano, mwachitsanzo, umu ndi momwe izo zingakhalire. Tsopano, ife tinene kuti, monga M’bale Junie, usikuuno, iye atanthauzira. Ife tikudziwa kuti iye ndi wotanthauzira. M’bale Neville ndi wotanthauzira, mwaona, amatanthauzira malirime. Ife tikudziwa zimenezo. Tsopano, bwanji ngati ife titakhala pano usikuuno, oh, Mzimu wa Mulungu ukungophulika kuti uyankhule. Mai, ubwino! Ndipo ife sitiri. . . ife tikuyenera kutero. . . ife tiri. . . Dikirani, mpingo uyamba mu maminiti pang’ono. Mwaona, ndife—ife tikukumana mpingo usanayambe. Ine ndikuziyika izo mu dongosolo monga ife tikanachitira pano.

<sup>350</sup> Chabwino, ndiye, chinthu choyambirira inu mukudziwa, akudzuka M'bale Ruddell ndipo akuyankhula mmalirime. Dikirani miniti yokha. Mukuona? Junie akulumpha, "PAKUTI ATERO AMBUYE, 'Chinthu *chakuti-chakuti*.'" Chabwino, winawake cha kuno, alembi akuzilemba izo pansi apa, mwaona, chirichonse chimene chinanenedwa; uh-huh, tiyeni tingozitenga izo mofulumira, chifukwa izo...mumvetse izo mwatsopano, chimene iye ananena. Chabwino, iwo...Ngati—ngati izo zakanidwa, ndiye inu—inu kulibwino mungozisiya izo, mwaona, kuzing'amba izo. Koma ngati izo sizinakanidwe, izo zimavomerezedwa ndi anthu awiri, ndiye izo zimalembedwa apa, iwo analemba dzina lawo pa izo. Mukuona? Izo—izo—izo ndi za mpingo wanu. Ndizo. . .Ine ndikukuzani inu nonse kwa phindu lanu, mwaona, ine sindikudziwa ngati iwo anachita izo pachiyambi kapena ayi.

<sup>351</sup> Ndipo chinthu choyambirira inu mukudziwa, Hollin akulumphira mmwamba, akuyankhula mmalirime. Tsopano, wotanthauzira akhoza kusuntha uthenga womwewo, mwaona, icho chikhoza kukhala chinthu chomwecho, chinthu chinachake kuti chichitika, ulosi; mwaona, chinachake chimene chikukonzekera kuti chichitike, kapena chinachake chimene inu mukuyenera kuchita. Mmwamba kulumpha M'bale Roberson, kumbuyo, akuyankhula mmalirime. Chabwino. Iwo ukhoza kukhalabe uthenga womwewo, kupereka kutanthauzira komweko, mwaona, kapena iwo akhoza kukhala mauthenga atatu.

<sup>352</sup> Tsopano, Mulungu sangayike mauthenga fifite usiku umodzi. Ife tikudziwa zimenezo, chifukwa inu—inu simunathe kuwamvetsa iwo. Inu mukuona? Koma chirichonse chimene chikuwupsyinja mpingo, monga. . .kapena chinachake chimene chikuchita, ndi cha kumangiriza kwa mpingo. Mukuona? Ndiye ine—ine—ine sindingalole enanso kuposa zimenezo, mwaona, chifukwa Ilo linati, "Izo zikhale motsatizana atatu." Mukuona?

<sup>353</sup> Basi kutsatizana atatu, ndiye—ndiye ine ndingati "Pitirirani ndipo mulembe zimenezo, ndipo mukaziyiye izo pamwamba apo pa guwa." Mukuona? Kenako mawa usiku tidzakumanenso. Mukuona? Ndipo ngati pali chirichonse chimene chikukonzekera kuchitika pakati pa tsopano ndi mawa usiku, Mulungu adzayankhula izo mu umodzi wa mauthenga amenewo. Mukuona chimene ine ndikutanthauza? Mulole izo zikhale motsatizana atatu. Ndipo ine ndikuganiza tsopano, Webster amati, ulosi ukhoza. . .

**Kodi funs-...uthenga ungatchedwe ulosi umene sukuneneratu za mtsogolo?**

<sup>354</sup> Ayi. Ngati iwo uli ulosi, iwo ukunenera, kuneneratu chinachake chimene chiti chidzachitike. Uko kulondola, aponso.

<sup>355</sup> Chabwino, ndipo ine ndikuganiza... Tsopano, ili ndi lomaliza mpaka ife titafika kwa awa apa.

**120. M'bale Branham, kodi—kodi aliwonse a awa... M'bale Branham, lirilonse la mafunso awa... Izi zalembedwa ndi makina olembera ndipo izo ziri pafupifupi kufufutika. Kodi lirilonse la mafunso awa... M'bale Branham, lirilonse la mafunso awa amene inu simukumverera kutsogozedwa kuti muwayankhe kapena kuwapereka pa... kapena kuperekerana ndemanga (eya), kuperekerana ndemanga, liyikeni ilo pambali, ine sindikhumudwa konse ndi izo. Kodi ntchito zathunthu za dikoni ndi chiyani molingana ndi Lemba?**

<sup>356</sup> Chabwino, ine—ine ndikukhulupirira iwo ali nazo izo kunjika uko. Ngati izo... Ine ndikudziwa kuti ndi mmodzi wa madikoni a mpingo wathu. Chotero ine ndikukhulupirira iwo ali ndi dongosolo la izo pamenepo. Ife tikuyenera kuti titenge zochulukira za zolembe zimenezo ndi kumupatsa aliyense wa madikoni athu ngati ife tiribe izo. Ndikudabwa ngati ife tingakhoze kupeza chimodzi cha izo, Gene, chimodzi... kapena, inu kapena M'bale Leo, kapena ena a iwo, za... mutenge pafupifupi sikisi kapena eyiti ya izo ndi kuzipereka izo kwa madikoni athu. Izo zimapereka ntchito, Mwamalemba, chimene dikoni akuyenera kuchita.

**121. Mwinamwake titakhala ndi ulosi kapena uthenga mmalirime mopanda dongoloso, kodi tikuyenera kuzikonza izo motani?**

<sup>357</sup> Tsopano, imeneyo ndi nkhani yabwino yadzidzidzi, mwaona. Mukuona? Tsopano, akudalitseni inu, dikoni amene wanena izi, chifukwa ichi ndi chinthu chabwino. Iwe umafuna kuzigwira izo ndi magolovesi a rabara. Tsopano, ngati inu mupereka a... Ngati wina abwera mu mpingo wathu kuno ndi kudzapereka uthenga kapena ulosi kunjika kwa dongosolo, palibepo nkomwe chirichonse chimene inu mungachite ngati iwo ayimirira kale. Mukuona? Inu basi... Iwo amadziwa kuti siali mu dongosolo ndipo izo—izo... zikhoza kuwononga msonkhano. Mukuona? Koma, ngati izo zitero, basi chinthu chabwino kuchita, kwa madikoni, ndi kungokhala chete basi. Mukuona? Chifukwa mneneri wa pa nsanja ndi amene kwenikweni amakhala ndi... Ndinu—ndinu ndinu chitetezero chake, ndinu wa polisi wake, mwaona, ndinu alonda motizungulira ife. Mukuona?

<sup>358</sup> Tsopano, ngati ali winawake mwa osonkh... Ngati izo ziri kunjika kwa osonkhana athu, munthuyo ndi wosaphunzitsidwa, mwaona, iwo sanaphunzitsidwe. Icho ndi chimene ife tikuyesera kuti tilowe muno, mwaona, kuti ife—ife tidziwe choti tichite. Ife timadziwa momwe timaphunzitsira anthu athu. Koma ngati izo—ngati izo ziri kunjika kwa osonkhana athu, chabwino, ife sitikudziwa momwe munthu wosaukayo anaphunzitsidwira.

<sup>359</sup> Mwachitsanzo, ngati... Billy akukumbukira izi, Costa Mesa, California. Nthawi iliyonse pamene ine ndakonzeka kuyitanira kuguwa pamakhala mkazi amalumphira mmwamba, ndi kumathamanga mokwera ndi motsika tinjira timeneto, akuyankhula mmalirime, ndipo iye ankangong'amba mzidutswa kuyitanira kuguwa kumeneko. Ndipo ine ndinkangochokapo kumapita panja. Inu mumakhoza kuwuwona Mzimu ukuchita—utakhumudwitsidwa, inu mwaona. Palibe chimene chingawukhumudwitse Mzimu wa Mulungu ngati izo ziri mu dongosolo. Mukuona? [Malo opanda kanthu pa tepi—Mkonzi]. . . basi iye asanakonzekere kuti ayambe, momwe iye angazikonzekeretse yekha, chifukwa ine ndinkamuyang'ana iye. Mtumiki aliyense angachite zimenezo pamene iye awona chirichonse sichiri mu dongosolo. Ndiye mkazi yu anali kumbuyo uko ndipo iye anamuza Billy, ndipo Billy anadzandiuza iye pamene ine ndinkabwera kuno usiku umenewo, anati, “Adadi, inu mukudziwa mkazi uja amene anasokoneza—kuitanira kuguwa kuja, mausiku awiri?”

“Eya.”

<sup>360</sup> Anati, “Iye anakhala kunja uko,” anati, “iye anati, ‘Ulemelero kwa Mulungu, Billy, ine ndiri ndi uthenga wina usikuuno!’”

<sup>361</sup> Chabwino, tsopano, inu mwaona, ine ndinamuyang'ana iye pansu mwa omvetsera. Panali masauzande a anthu pamenepo; ndi pamene *Reader's Digest* inalemba izo za kuchiritsidwa kwa Donny Morton, inu mukudziwa, *Chozizwa cha Donny Morton*. Chotero ine ndinamuwona mkaziyo, ndipo basi pafupifupi nthawi imene ine ndinayamba kuitanira kuguwa kwanga, iye. . . Tsopano, iye anali wosaphunzitsidwa; mosakaikira, mkazi wabwino. Koma iye anayang'ana mozungulira, iye anayamba kuzikonza tsitsi lake. Iye anali ndi tsitsi lometa, mwaona. Chotero, inu mwaona, iye anali wa Assemblies kapena ina ya mipingo imene—imene imaloleza izo. Iye anali akukonza tsitsi lake. Iye anafikira pansu ndipo anakoka mastonkeni ake, anakonzeka monga choncho. Ndipo basi pafupifupi nthawi imene ine ndinayamba kupanga guwa. . . Ine ndinati, “Tsopano, ndi angati muno. . . ndi angati amene ali pano tsopano amene akufuna kubwera kutsogolo ndi—ndi kudzapereka mitima yawo kwa Ambuye Yesu?”

<sup>362</sup> Iye analumphira mmwamba. Ine ndinati, “Khala pansu.” Iye anapitiriza. Ine ndinati, “Khala pansu!” Mukuona? Ndipo, mnyamata, aliyense. . . Ine ndinangoyima. Iye anachita ngati sanandimve ine, ndipo ndinadzafuula mokweza kachiwiri. Iye anandimva ine nthawi imeneyo, chifukwa ine ndinakhala ngati ndikugwedeza nyumbayo ndi cholankhulira chachikulu chimenecho nditaima pamenepo. Ndipo anadzakhala pansu.

<sup>363</sup> Ine ndinati, “Tsopano, pamene ndimati, ndi angati akufuna

kubwera ku guwa ndi kudzapereka mitima yawo kwa Mulungu?" Ndipo ine ndinapitirira ndi msonkhanowo, mwaona.

<sup>364</sup> Ndipo usiku umenewo pamene ine ndinayamba kupita ku galimoto, ndinazunguliridwa. Ndipo apa gulu la akazi awo litayima pamenepo ngati gulu la nkukhu, inu mukudziwa, "Inu munachitira mwano Mzimu Woyera."

<sup>365</sup> Ine ndinati, "Ine ndinatero?" Ine ndinati, "Kodi ndingachitire mwano bwanji Mzimu Woyera potsatira mala- . . . kulengeza kwa Malemba?" Mukuona?

<sup>366</sup> Ndipo mkazi uyu anati, "Ine ndinali ndi uthenga wochokera kwa Mulungu."

<sup>367</sup> Ine ndinati, "Koma iwe umawupereka iwo mu nthawi yolakwika, mlongo." Ine ndinati, "Ine sikuti . . ."

"Inu mukuti izo sizinali—izo sizinali za Mulungu?"

<sup>368</sup> Ine ndinati, "Ine sindingakuuze iwe, dona." Ine ndinati, "Ine—ine—ine ndikukhulupirira izo zinali, mwaona." Ine ndinati, "Ine ndinena izo kwa phindu lako, kuti, 'Ndikunena kuti ndikukhulupirira kuti izo zinali.' Ndipo ine ndikukhulupirira kuti ndiwe mkazi wabwino, koma iwe unali kunjja kwa dongosolo."

<sup>369</sup> Ndipo apo panali m'busa wake atayima pamenepo. Ine ndinadziwa kuti iye anali m'busa wake, mwaona. Ndipo ine ndinati . . . Ine—ine ndinati, "Pali chinthu chimodzi chokha chimene ine ndinganene, kuti mwina iwe unali mu thupi kapena iwe uli ndi m'busa amene anakuphunzitsa iwe amene samadziwa kanthu za Malemba." Ine ndinati, "Iye akuyenera kubwera ndi kudzayankhula kwa ife kanthawi pang'ono za Malemba. Izo ndi zolakwika, inu muli kunjja kwa dongosolo. Inu munataya miyoyo yambiri, usiku wa dzana, ndi yambiri usiku watha kachiwiri, ndipo mukanachita chinthu chomwecho usikuuno."

<sup>370</sup> Ndipo mwamuna uyu anati, "M'bale Branham," anati, "Ndikupempha kukhululukira kwano."

Ine ndinati, "Mukutanthauza chiyani?"

<sup>371</sup> Anati, "Iye anali ndi ufulu wopereka uthenga umenewo, inu munali mutamaliza."

<sup>372</sup> Ine ndinati, "Ine ndinali pa nsanja, ndipo mzimu wa aneneri umamumvera mneneri. Ine ndikadali pa nsanja."

Ndipo iye anati, "Chabwino . . ."

<sup>373</sup> Ine ndinati, "Ine ndinali nawobe Uthenga. Ine ndimapanga kuyitanira kuguwa kwanga, ndiko kukokera mkati. Ine ndinaponya ukonde wanga kunjja, ine ndimawukoka iwo tsopano. Musati muponyere waya waminga kunjja uko kapena chinachake choti chisokoneze izo, mwaona." Ine ndinati, "Ine ndimakokabe ukonde wanga." Ndipo—ndipo ine ndinati, "Iye anasokoneza ndi—ndi kubweretsa miyoyo. A . . . Izo zingachite



ubwino wanji kulalikira kapena china chirichonse ngati inu simuitana ndi kupeza ochimwa kuti abwere uko? Mukuona?”

<sup>374</sup> Ndipo iye anati, “Chabwino, uthenga wake unali mochedwerapo kuposa wanu. Wake unali wochokera pa nsanja pomwe. . . Wake unali wolunjika kuchokera kwa Mulungu.”

<sup>375</sup> Ine ndinati, “Ngati munthu aliyense aziyesa yekha kuti ndi wauzimu, kapena mneneri muloleni iye azindikire kuti chimene ndikunenachi ndi Malamulo a Ambuye. Koma ngati iye ali wosadziwa, mungomulola iye akhale wosadziwa. Ife tiribe mwambo woterowo, kapena Mpingo wa Mulungu,” kubwereza zonenza za Paulo, inu mukudziwa. Ine ndinati, “Ayi, bwana, palibe chatsopano! Iye. . . Yesu anati, ‘Mulole mawu a munthu aliyense akhale bodza ndipo Anga akhale Owona.’ Paulo anati, ‘Ngakhale Mngelo wochokera Kumwamba atabwera ndi china chirichonse kupatula chimene chiri Pano, mulole icho chikhale chotembereredwa.’” Ine ndinati, “Bambo, inu mwachoka kwenikweni pa mzere.” Ine ndinati, “Kodi inu muli ndi mpingo wamtundu wanji? Ndikukhulupirira kuti ndi gulu lalikulu la chisokonezo. Mukuona? Ngati inu mungawalole anthu amenewo kuti azichita zimenezo inu mumapanga bwanji kuitanira kuguwa kwanu? Iye ali ndi utumiki, iwo onse ali ndi utumiki, koma inu muli ndi nthawi ya utumiki wanu, mwaona, imene imaperekedwa.”

<sup>376</sup> Chotero uko nkulondola. Ayi, ndipo tsopano ngati izo zichitika mu mpingo *wathu* monga choncho, monga chonchi, ndi abale athu kapena alongo athu muno mu mpingo amene amayankhula ndi malirime, tsopano, madikoni akatha mapemphero, gulu ine ndikuganiza likuyenera kukomana nawo iwo pamodzi, ndi kuti, “Ndiroleni ine ndilozere mobwerera kwa inu pa tepi, kwa maminiti pang’ono okha, inu mwaona.” Mwaona, ndinu basi. . . Kapena—kapena, abusa, akuti, “Ine—ine ndikutsimikiza abusa akufuna kuyankhula nanu inu. Kodi mungangokumana nafe kuno mu mowerengera kanthawi pang’ono, mwaona, m’bale.” Pamene, ndiye nkupita mmenemo ndi kukayankhula naye iye mwabwino kwenikweni. Mukuona? Ndi kuti. . .

<sup>377</sup> Koma, tsopano, ngati iwo azichotsa onse mu dongosolo ndi kuwasokoneza abusa anu, mwaona, ngati—ngati iwo akuwasokoneza abusa anu, ndiye inu akulu akulu mukuyenera kupita kwa iye ndi kukati, “Dikirani pang’ono.” Ndipo ngati abusa akuwonetsani inu kuti muwaletse iwo, ndiye iye wawugwira kale mzimu pamenepo, kuti ndi. . . kuti iwo akuswa mzimu wa msonkhano, inu mwaona.

<sup>378</sup> Chotero ngati abusa ayima ndi kuweramitsa mutu wawo molemekeza, musanene kalikonse. Mukuona? Musanene kalikonse; asiyezi abusa. Koma inu muziwayang’ana abusa. Ngati iwo asonyeza kwa inu monga choncho, kuti muyimitse

izo, ndiye mupite ndi chikondi cha Chikhristu, nkukati, “M’bale wanga, mlongo,” aliyense amene angakhale, “Ine ndikukhulupirira kuti inu mwachoka mu dongosolo, chifukwa inu mukumusokoneza mneneri, inu mwaona. Iye ali ndi uthenga wochokera kwa Mulungu. Iye akamaliza uthenga wake, ndiye ife tiwona za izo pambuyo pake.” Mwaona, ngati izo zikumusokoneza iye.

<sup>379</sup> Koma ngati ali winawake kunja uko, ndipo abusa mwaulemu angoyima ndi kudikirira miniti, ndiye iye...mwinamwake iwo adzayambiranso, inu mwaona. Chotero...Ndipo ngati inu mungazindikire, nainte peresenti ya nthawi monga choncho, kutanthauzira, ndi nthawizonse kumangobwereza Lemba lina kapena chinachake chonga icho, zomwe ziri mwina zathupi ku mathero onse awiri a mzere. Inu mukudziwa chimene ine ndikutanthauza monga choncho. Mukuona? Chabwino.

## **122. Kodi woposa mmodzi amaloledwa kuyankhula uthenga mu malirime popanda kutanthauzira?**

<sup>380</sup> Ayi. Akuyenera kubwera mmodzimmodzi. Mukuona? Mmodzi apereke...Mmodzi ayankhule, ndipo kenako apereke kutanthauzira. Mukuona? Ndiyeno ngati wina ayankhula, kutanthauzira; chifukwa ngati inu simutero, wotanthauzira sadziwa chimene iye akuchita chifukwa pali mauthenga awiri kapena atatu apa akumenya pa iye nthawi imodzi, inu mwaona, ndipo zimenezo zingakhale zosokoneza kwa iye. Ndipo Mulungu siwoyambitsa chisokonezo, inu mwaona. Chotero muzilola mmodzi aziyankhula, ndipo wina atanthauzire. Mukuona? Ndipo kenako...Aperereke mauthenga atatu, koma mulole uthenga uliwonse utanthauziridwe.

<sup>381</sup> Kenako ife tidzakhala...Monga ngati M’bale Ruddell angayankhule ndipo M’bale Neville angapereke kutanthauzira, M’bale Fred angokhala chete. Mwaona, amvetsere kutanthauzira kumeneko. Choyamba, izo zikuyenera kuweruzidwa poyamba, kuti muwone ngati izo ziri za Mulungu kapena ayi, mmalo oyambirira. Mukuona? Ndipo chabwino. Tsopano, ngati M’bale Ruddell wayankhula, M’bale Beeler wayankhula, M’bale Neville wayankhula, wotanthauzira wosaukayo ali ndi mauthenga atatu motsogozana; chiyani—chiyani, iye akadziwira pati choti achite? Mukuona? Musiyeni iye yekha. Perekani uthengawo ndipo kenako khalani chete, muzingodikirira. Mulole chinachake chiwululidwe kwa wina amene wakhala pafupi ndi iye; musiyeni iye akhale chete, angokhala bata. Mukuona? Ndipo kenako mulole kutanthauzira kubwere.

<sup>382</sup> Ndiye, pamene inu mutero, mulembe izo ndiye, muwone zomwe ozindikira zamumtima ati anene. Mukuona? Ngati iwo akuti, “Chabwino, izo ndi—izo ndi za Mulungu.” Chabwino, pali uthenga, mwaona, lembani izo. Ndiye mudikire miniti yokha.

Ndipo chinthu choyambirira inu mukudziwa, chabwino, ndiye Mzimu ukuyenda pa iye, iye aziyankhula. Ndiye wotanthauzira adikire miniti, awone zomwe Mzimu Woyera uti unene. Apa Iye akubwerera Uthenga umenewo, inu mwaona. Ndipo kenako iye adzazilemba izo, mwaona. Ndipo mulole izo zikhale atatu motsatizana.

**123. M'bale Branham, ife tikudziwa kuti inu ndi mtumiki wotumizidwa kuchokera kwa Mulungu ku m'badwo uno wa mpingo. Zizindikiro zomwezo zomwe zinkamutsatira Yesu tikuziwona zikukutsatirani inu, ndipo ife tiri... tikumvetsa chifukwa chimene ena amene amakudziwani inu bwino akuganiza kuti ndinu Mesiya. Kodi mungafotokoze kusiyana kwa ubale wanu kwa Mulungu ndi wa Khristu?**

<sup>383</sup> Chabwino, ine ndikudziwa, abale, izo ndi zoon. Mwaona, koma tiyeni tidikire, ine ndalemba chinachake cha izo apa, kwa miniti yokha. Mwaona, nthawi zambiri sizimamvetsedwa bwino. Mukuona? Koma, tsopano, mwa munthuyo nthawiyina... Ndipo ine ndikufuna ena a inu kuti mutsegule ndi ine ku Luka, mutu wa 3 ndi ndime ya 15. Pamene inu mukuchita zimenezo, ine ndikhoza kumamena kwa inu... Pamene mukupeza izo, kuti ndi Luka 3, ndi... mwina... izo ziri mu... Ndiroleni ine basi... ine sinditseka chitseko, chifukwa palibe aliyense pamenepo. Mundilole—mundilole ine ndingotengera izi kwa inu, abale. Inu mwamvapo izo, izo ziriponse. Koma ndiroleni ine ndikuuzeni inu, mwaona, izo zikuyenera kubwera mwanjira imeneyo. Izo zikuyenera kubwera mwanjira imeneyo. Ngati izo sizinali mwanjira imeneyo ine ndikanalapa pa uthenga wanga.

<sup>384</sup> Mvetserani, abale, inu ndikukuchondelelani pamaso pa Khristu kuti inu—inu—inu mugwire mbali iyi ya bata lanu, koma ngati inu mukanakhala auzimu mukanamvetsa. Mukuona? Kodi inu simukudziwa chinthu choyamba chimene Iye ananena kumusi uko pa mtsinje? Kodi inu simukukumbukira chimene Iye ananena? “Monga Yohane M'batizi anatumidwa kuti adzatsogolere kudza koyamba kwa Khristu, Uthenga wako...” Ndi Uthenga umene udzatsogolere Kudza Kwachiwiri kwa Khristu. Chimenecho ndi chimene Mngelo wa Ambuye ananena.

<sup>385</sup> Tsopano, tsopano zindikirani. Tsopano, “Monga Yohane M'batizi...” Tsopano, nonse a inu mwazimva zimenezo. Inu mwaziwerenga izo mmabukhu, ndipo mwawamva anthu amene anayima pamenepo akumva Izo, ndi china chirichonse, pamene Mngelo uja Mwiniwake anayankhula uthenga umenewo, “Monga Yohane M'batizi anatumidwa kudzatsogolera kudza koyamba kwa Khristu, iwe watumidwa ndi Uthenga uwu, udzatsogolera Kudza Kwachiwiri kwa Khristu.” Tsopano, “Uthenga.”

<sup>386</sup> Tsopano, ngati inu mungazindikire, ndipo ine...Willie

wamng'ono kunja uko anayika dzina langa pansi pa nyenyezi iyo kunja uko, ndipo ndicho chifukwa ine ndinalambalala icho, inu mwaona, chifukwa ine—ine sindikuganiza. . . Tsopano, ine ndikhala woona mtima momwe ndingathere, Ine sindikuganiza kuti ine ndikanakhala ndi chirichonse chochita ndi mtumiki ameneyo, mwaona. Uko nkulondola. Ine ndikukhulupirira kuti mwinamwake ine ndatumidwa kwa kagawo mu Mpingo Wake, kuti ndidzathandizire kuwumanga Uthenga umenewo kufika pamalo amene ungate kufikapo pamene wotsogolera uyu azidzabwera, kuti iye abwere.

<sup>387</sup> Koma ine ndikukhulupirira, ine pokhala chimene ine ndiri, ine ndiri. . . Ine ndikukhulupirira kuti ine ndiri ndi Uthenga wa tsikuli. Ine ndikukhulupirira kuti uku ndi Kuwala kwa tsikuli, ndipo ine ndikukhulupirira iko kukuloza ku nthawi ikudzayo, inu mwaona, ine ndikukhulupirira kuti Uthenga umene iye ananena kumusi uja, “Uthenga umene inu muli nawo.” Tsopano, ngati inu mungazindikire Nyenyezi ija imene inatuluka kumbuyo uko, inali. . .

<sup>388</sup> Mundirole ine ndipange izo. . . Ndikudziwa ine—ine ndikutsina nthawi yanga apa, ndipo ine ndiri ndi ena awa, mafunso abwino chotero. Ine sindikufuna. . . Iyi—yadutsa teni tsopano, kotero, ndipo ine ndikudziwa kuti inu mukufuna kuti muzipita kwanu. Mukuona? Koma mvetserani apa. Ndiroleni ine ndikuwonetseni inu chinachake. Kodi mungandipatseko basi—mphindi zochepa chabe zowonjezera? Chabwino, chabwino.

<sup>389</sup> Tsopano taonani, tsopano ndiroleni ine ndinene chinachake. Tsopano, abale inu musunge izi pakati pa inueni. Mukuona? Tsopano, musunge izi pakati pa inueni. Ine ndikuyenera kukufikitsani inu powongoka pa izi chifukwa ndinu m'busa wanga. . . ndinu azibusa anga ndi zinthu, inu mwaona, ndipo ine—ine ndikuyenera kuchita ichi. Ndipo ndinu abale ndi ine tikugwira ntchito mu Uthenga uwu. Mukuona?

<sup>390</sup> Tsopano, kwa ine mwiniwanga, monga munthu, ine ndiri ngati inu ndipo woyipa kuposa inu. Ine—ine—ine. . . Ambiri a inu nonse munabwera ndi maziko a Chikristu ndi zinthu. “Ine ndi wamkulu wa ochimwa,” monga zinanenedwa nthawi yina, “pakati panu.” Wotsikitsitsa wa moyo, ine ndikuganiza, umene ukanakhoza kukhalidwa, monga wosakhulupirira ndi wokayikira, ine ndinali.

<sup>391</sup> Koma kuyambira ndiri mwana ndakhala ndikudziwa kuti Mulungu alipo, ndipo ndinkadziwa kuti panali chinachake chinachitika mmoyo wanga. Ndipo ndicho—icho ndi choposa funso lirilonse, m'bale wanga. Mukuona? Koma mudiroleni ine ndinene ichi, kuti kudzabwera—kudzabwera Uthenga, ndipo kudzabwera wa mthenga. Ine ndikukhulupirira kuti ngati ati adzakhale munthu iye—iye adzakhala winawake pambuyo pa ine. Mukuona? Izo zidzakhala. . . Koma Uthenga uwu umene

ine ndikulalikira ndi Uthenga woona wa tsiku lino, ndipo ndi Uthenga wotsiriza. Inu mukuona chimene ine ndikuchita, abale? Ine ndikukuyikani inu nonse pamalo omwewo amene ine ndiri, chifukwa inu muli mochuluka mu izo monga ine ndiri. Inu ndi atumiki a Uthenga womwewu.

<sup>392</sup> Taonani apa, ine ndiri ndi kuwonetsera. Ine—ine ndikuganiza kuti ndikhoza kupanga izo bwino mwa kuwonetsera. Ndiroleni ine ndingotseka pang’ono chitseko ichi kwa kanthawi. *Uyu* ndi Yesu, ndipo *uyo* ndi Yesu; chabwino, ine ndiyika *ichi* cha apa, Getsemane, ndi ichi *apa* ndi *apo*. Tsopano, inu simungathe... Ine sindinanene nkomwe izi pamaso pa mpingo kunja uko. Tsopano, kumbukirani, ndi mtundu wanji wa kuwala (nyenyezi) kunamutsogolera munthu amene ankafunafuna nzeru “*kuti ititsogolere ife ku Kuwala Kwanu kwangwiro*”?

<sup>393</sup> Tsopano ine ndiyima kaye apa miniti yokha ndi kukuuzani inu chinachake. Tiyeni tichigwedeze chinthucho kuchoka pa . . . chimene Willie wachita kumtunda uko, ndipo nkunena kuti ndi zolondola. Tiyeni tingonena kuti ndi izo ndi zoon. Ine sindinganene zimenezo, abale. Kumeneko ndi kudzikweza. Izo, ine sindingatero . . . Ngakhale ndikanakhulupirira izo, ine sindikananena izo. Mukuona? Winawake amanena zimenezo, amenewo ndi iwo.

<sup>394</sup> Koma, apa, chimodzimidzi monga ine ndinangofunsidwa kumene, ena a anyamata, ngati iwo angachitire umboni za zinthu zina zomwe zachitika. Ine sindimakonda kufika pa guwa ndi kuchitira umboni za chinachake chimene chachitika mu msonkhano. Mulole manejala kapena winawake azichita zimenezo, winawake azichita zimenezo. Ine sindimakonda kuchita zimenezo.

<sup>395</sup> [M’bale akuti, “Ngakhale iwo anabwera kwa Yohane ndipo anati, ‘Kodi inu ndi Khristu?’”—Mkonzi]. Eya, ndi zimenezo, chimene ine ndikuyesera kuti ndifikeko. [“Kodi inu ndi Mneneri ameneyo?”] Iye anakana izo. [“Sananene chimodzi, iye akuti, ‘Ine ndangokhala iye wofuula mchipululu.’”] “Liwu la iye wofuula m’chipululu.” Iye anadziyika yekha pa malo.

<sup>396</sup> [M’bale wina akuti, “Iwo anamufunsa iye ngati iye anali Mneneri ameneyo, iye anati ‘Ine sindiri.’”—Mkonzi]. Eya. Tsopano . . . Pakuti Mneneri anali Mmodzi uja amene Mose ankamukamba. Mwaona, ameneyo ndi Mneneri, mwaona. Mukuona? Koma iye ankadziwa yemwe iye anali, mwaona. Koma iye ananena, tsopano, izo . . . Iye anawauza iwo, mwaona, ndipo iye anati, “Ndine liwu la mmodzi . . .” Ameneyo anali iye. Iye—iye ananena chimene iye anali. Mukuona? Koma iye anali a . . .

<sup>397</sup> Pitirirani. [M’bale akuti, “Pamene Khristu anabwera pamenepo, akumutsatira Yohane, iwo anabwera kwa Iye, iwo anati, ‘Taphunzitsidwa kukhulupirira kuti Eliya adzabwera

Mesiya asanabwere.’ Iye anati, ‘Ngati inu mungalandire izo.’—Mkonzi]. Ameneyo anali iye. Uko nkulondola. Uko nkulondola. Ndipo Yohane anapitiriza kunena, “Ine si kanthu! Ine si kanthu! Ine siwoyenera kumasula nsapato Zake!”

<sup>398</sup> Koma bwanji pamene Yesu ananena za iye? Iye anati, “Inu munapita kukamuwona ndani?” Eya. Eya. “Kodi inu munapita kukawona bango likugwedezeke ndi mphepo? Kapena kodi inu munapita kukawona chiyani, munthu wina wovala zovala zabwino ndi zapamwamba ndi zinthu?” Anati, “Iwo ali mnyumba yachifumu. Koma kodi inu munapita kukamuwona mneneri? Ine ndikuti inde, ndipo woposa mneneri.” Iye anali woposa mneneri, iye anali mtumiki wa pangano. Icho ndi chimene iye anali. Iye anali woposa mneneri. Iye anati, “Sipanakhalepo mwamuna wobadwa ndi mkazi wamkulu monga iye kufikira pano.” Mukuona?

<sup>399</sup> Ndicho chimene icho chinali, mwaona, iye anali mtumiki wa pangano. Iye anali amene anamuwonetsera ndipo anati, “Uyu ndi Iye.” Aneneri ena onse ankayankhula za Iye, koma Yohane anati “Uyu *ndi* Iye.” Mukuona?

<sup>400</sup> Tsopano penyani. Tsopano zindikirani. Amuna anzeru ankatsatira nyenyezi. Ine ndizitengera izo mmbuyo mochuluka mwanjira yaying’ono, mwaona. Amuna anzeru ankatsatira nyenyezi, kumafunsa, “Ali kuti Iye wabadwa ali Mfumu ya Ayuda?” Inu munaimvapo nyimboyo. “Ife taiwona nyenyezi Yake kummawa ndipo tabwera kudzamlambira Iye.” Inu munaimvapo iyo, munawerenga izo mu Lemba. Chabwino.

<sup>401</sup> “Kutsogolera cha Kumadzulo, ikupitirirabe, tilondoleleni ife ku Kuwala Kwanu kwangwiro.” Mwaona, nyenyeziyo inkalondolera ku Kuwala kwangwiro, chifukwa nyenyezi inkangonyezimiritsa Kuwalako. Ndi pamene ife tinazipeza izi kunja kuno tsiku lina. Mukuona? Ndi angati anali pano Lamlungu kuti adzawone izo? Inu mwaona, ndangotsiriza kumene kulalikira za izo. Ulemelero wa Shekinah unanyezimira mu nyenyezi, ndipo nyenyezi imanyezimiritsa Iko. Apa panali Mngelo wa Ambuye atayima apa pa nsanja akunyezimiritsa Iko kumbuyo uko, kuchokera mu Ulemelero wa Shekinah. Ndendende basi chinthu chomwecho. Apo izo zinali kulondola ndendende. Akuyang’ana apa pa chenichenicho, akuyang’ana kunja uko ndipo Iko kukunyezimiritsidwa mmbali yomweyo monga choncho. Mukuona?

<sup>402</sup> Tsopano zindikirani izi, tsopano, nyenyezi imeneyo inatulukira kummawa. Nkulondola uko? Iyo inali nyenyezi yayikulu. Chabwino. Ndipo ndani amene anali nyenyezi yeniyeni ya padziko lapansi mu nthawi ya kudza kwa Yesu? Bwanji, Yohane. Iye anali amene anawatsogolera iwo ku Kuwala kwangwiro kuja. Nkulondola uko? Kumeneko kunali kummawa pa kuwonekera koyamba kwa Yesu. Ndipo, tsopano, ziripo

nyenyezi zambiri zazing'ono zomwe zimawoloka chopingasa mpaka izo zimafika ku nyenyezi ya kumadzulo.

<sup>403</sup> Ndipo nyenyezi ya kumadzulo imawala madzulo. Nyenyezi yam'mawa imawala m'mawa. Ndipo ziwiri zonsezo ndi nyenyezi zazikulu zofanana ndi nyenyezi zamtundu umodzi. Tsopano ziyikeni ziwiri ndi ziwiri pamodzi ndipo inu mupeza izo, mwaona. Mwaona, ndi inu pamenepo. Chotero izo siziri... Nyenyeziyo si Mesiya, koma iyo ikungonyezimiritsa Mesiya.

<sup>404</sup> Tsopano, nyenyeziyo simanyezimiritsa kuwala kwake komwe. Nyenyeziyo imanyezimiritsa kuwala kwa dzuwa. Nkulondola uko? [M'bale akuti, "Ayi."—Mkonzi]. Huh? ["Mu lingaliro. Mwezi umatero; nyenyezi zimanyezimiritsa kuwala kwake."] Eya. Eya, mwezi, eya, a-... Ndikutanthauza kuti mwezi umanyezimiritsa kuwala uku. Eya, Uh-hum. Tsopano, ngati—ngati nyenyezi ikunyezimiritsa kuwala kwake, ndiye kuwala kwake kumayenera kubwera kuchokera kwa... kuchokera kwa Mulungu, chifukwa ndi madzi owundana amtundu wina. Sichoncho izo? [M'baleyo akuti, "Dzuwa."] Huh? Dzuwa palokha, kuchokera ku dzuwa. ["Dzuwa liri kutali kwambiri kuposa dzuwa lathu."] Eya. Ndipo iwo... Timauzidwa kuti madzuwa amenewo amachokera ku dzuwa lalikulu. Dzuwa linaponya mizinga iyi ndipo ndi mizinga yaying'ono yoyaka ngati dzuwa. Chotero iwo ndi madzuwa aang'ono kwa ife. Nkulondola uko? Kuwala kwakung'ono. ["Ena ndi... ambiri a iwo ndi aakulu kuposa dzuwa lathu."] Ndikutanthauza kwa ife, kwa ife, mwaona. Ife tikukamba za ifeeni pantho. Chabwino.

<sup>405</sup> Tsopano, ngati iwo ali madzuwa kwa ife, kapena opereka kuwala, iwo ndi gawo la opereka wamkulu. Mukuona? Dzuwa lalikulu limatipatsa ife kuwala kwakukulu, kuwala kwangwiro. Madzuwa aang'ono, kapena nyenyezi zazing'ono, zomwe timatha kuziwona mmagulu, izo zikhoza kukhala kutali kupitirira—Dzuwa limene limawala, koma chimene izo zimanyezimiritsa kwa ife ndi kuwala kochepe. Koma izo zimangochitira umboni za kuwala. Nkulondola uko? Ndiye pamene dzuwa lalikulu likutuluka, madzuwa aang'ono amathima. Nkulondola uko? Iwo si—dzuwa kwa ife, iwo ndi onyezimira ngati dzuwa. Mukuona chimene ine ndikutanthauza?

<sup>406</sup> Tsopano, chachikulu pakati pa iwo (m'mawa) chimene chimalengeza kudza kwa dzuwa, kulowa kwa dzuwa ndi kudza kwa dzuwa, ndi nyenyezi ya mmawa ndi nyenyezi yamadzulo. Nkulondola uko? Nyenyezi ziwiri zazikulu kwambiri, nyenyezi ya kummawa ndi nyenyezi ya kumadzulo.

<sup>407</sup> Tsopano, tsopano inu mukuona pamene izo ziri? Eliya anali wamthenga kuti amuwone, wolengeza kudza kwa nyenyezi ya kummawa, ndipo ananedweratu kuti adzakhala wolengeza wa—nyenyezi ya kumadzulo, kapena kudza kwachiwiri kwa

tsiku latsopano tsiku ili litadutsa. Tsopano inu mukuona chimene icho chiri?

408 Kummawa, “Kudzakhala kuwala mu . . .” Mwaona, Dzuwa lisanalengezedwe ku dziko lapansi, nyenyezi yammawa imachitira umboni kuti “Dzuwa likubwera.” Nkulondola uko? Mwaona, izo zimabweretsa nyenyezi ya mmawa. Chabwino, ndiye nyenyezi ya mmawa ndi nyenyezi ya madzulo ndi mtundu womwewo wa nyenyezi, ndipo pali nyenyezi zazing’ono ponseponse. Kodi inu simukuwona chimene ine ndikutanthauza? Amithenga.

409 Chabwino, ndiye, Iye ankayenera kumawoneka ngati Alpha ndi Omega, Woyamba ndi Wotsiriza, mwala wa Yaspi ndi Sarde. Mukuona chimene ine ndikutanthauza? Tsopano, kudza kwa—kwa Khristu kukuyandikira pafupi, ndiye Uthenga umene Eliya ankayenera kuti alalikire mmasiku otsiriza, ngati pali kubwereza kwa mbiriyakale . . . Monga momwe nyenyezi ya m’wawa imalengeza kubwera kumeneko, nyenyezi yamadzulo imalengeza kudza kwa tsiku latsopano, tsiku lina. Uku ndi kubwera kwa dzuwa ndiye kumene kukulengeza a—kupita kwa—kwa dzuwa limene tinali nalo ndi kudza kwa dzuwa latsopano, mwaona, m’badwo watsopano, nthawi yatsopano yoti ibweremo.

410 Tsopano, mvetserani kwa: Ndiye, ngati Yohane anabweretsa uthenga wake ndi kudzalengeza kudza koyamba kwa Khristu, ndipo Eliya akudza mu tsiku lotsiriza, mneneri anati, “Kudzakhala Kuwala mu nthawi yakumadzulo.” Mwakuyankhula kwina, kudzakhala Kuwala mu nthawi yakumadzulo.

411 Kuwala kwakumadzulo, kuwala kwakumadzulo kwakukulu kumene ife tiri nako ndi nyenyezi yakumadzulo, kuwala kopambana kumene ife tiri nako. Chabwino, ndiye, iko kudzayenera kudzalengeza uthenga womwewo umene unali monga nyenyezi ina iyi. Iko kukulengeza dzuwa, kuyankhula za dzuwa.

412 Chabwino, tsopano ife tiri mu nthawi ya kumadzulo, Kuwala kwa kumadzulo kuli pano. M’badwo uwu watha. Mukuona chimene ine ndikutanthauza? Tsiku ili ladutsa, ndipo pakhalakulengeza kwa Tsiku lina likubwera.

413 Pakuti, mwaona, ndizo kwenikweni . . . Ngati winawake akanakhala kumadzulo ndi kuyang’ana mmbuyo ku nyenyezi imeneyo, kukanakhala kummawa. Ndiyeno, inu mwaona, “ife taiwona nyenyezi Yake kummawa,” koma iwo anali kwenikweni . . . iwo anali—iwo anali kummawa akuyang’ana cha kumadzulo kwa nyenyezi imeneyo. Nkulondola uko? Amuna anzeruwo anali chakumadzulo . . . chakummawa, akuyang’ana mmbuyo ku nyenyezi yakumadzulo. Mukuona chimene ine ndikutanthauza? Koma iyo inali nyenyezi yakummawa kwa amene anali kumadzulo.



414 Mwaona, monga ife tinganene. . . Ine nthawizonse ndimati, “Pansi ndi mmwamba.” Inu mumadziwa bwanji koma chimene chiri cholondola? Ife tikuyima mu Muyaya, chotero South Pole ikhoza kukhala mmwamba ndipo North Pole ikhoza kukhala pansi. Ife sitikudziwa. Mwaona, njira yopita mmwamba ndi pansi. Mukuona? Ndife. . . Ife tidzalisiya ili; likadzatha ili ife tidzapita mu Muyaya. Ndi kuwona, kulengeza kudza kwa Muyaya, tsiku losiyana, nthawi yosiyana, ndipo zonsezo pamodzi.

415 Tsopano ife tiri mu nthawi yakumadzulo. Ife tikukhulupirira zimenezo. Ife timakhulupirira kuti kudza kwa Ambuye kuli pafupi. Chabwino. Tsopano, ngati izo ziri chomwecho, ndiye pakuyenera kukhala Kuwala kwa kumadzulo. Ndipo Kuwala kwa kumadzulo, malingana ndi Malaki 4, kunkayenera ku “kudzabwezera mitima ya ana kwa atate,” kubwerera ku chiyambi.

416 Koma pamene iye anabwera nthawi yoyamba, iye ankabwezera mitima ya atate kwa ana. Ana anali iwo amene iye ankawasonkhanitsa momuzungulira iye. Iye anali woti adzawabweretse ana. . . mitima ya atate (okalamba, achikale achi orthodox) kubwerera ku kuwala uku kumene iye ankalengeza kuno.

417 Koma pamene iye akubwera kachiwiri, iye akuyenera kudzatembenuka kubwerera mmbuyo (kodi inu munazindikira, dziko lisanawonongedwe nkomwe, “tsiku lalikulu ndi lowopsya la Ambuye”) ndipo “adzabwezeretsa mitima ya ana kwa atate,” madzulo—nyenyezi yakumadzulo imene inali nyenyezi yammawa pa nthawi imeneyo. Amen.

418 Ine ndikuyembekeza—ine ndikuyembekeza kuti ndazimva izo molondola, mwaona. Nyenyezi yakumadzulo imene inali nyenyezi yammawa, chifukwa ndi nyenyezi yomwe yomweyo. Ife tiri kumadzulo, tikuyang’ana kummawa. Iwo anali kummawa, akuyang’ana kumadzulo. Imeneyo ndi ndendende nyenyezi yomwe yomweyo. Mukuona chimene ine ndikutanthauza? Zimatengera komwe inu muli, mwaona, kaya iyo ndi nyenyezi yakummawa kapena yakumadzulo. Inu mukuona chimene ine ndikutanthauza? Chabwino.

419 Tsopano, izo zimabwezeretsa. . . wina amabwezeretsa chikhulupiriro cha atate kwa ana; mu nthawi ino ndi “chikhulupiriro cha ana kubwerera kwa atate.” Inu mwazungulira, ndipo mukubwera mozungulira kachiwiri. Kodi inu simukuwona chimene mukutanthauza? Mukuona chimene ine ndikutanthauza? Iyo ndi nyenyezi yomweyi nthawi zonse. Chinthu chomwecho, Uthenga womwewo, chinthu chomwecho kubwerera kachiwiri. Iyo yadutsa.

420 Ndipo inu mumadziwa bwanji njira imene inu mukupita? Ine ndikukhulupirira ora lidzafika pamene

iwo ati adzapeze kwenikweni kuti dziko silimathamanga nkomwe. Ine ndikukhulupirira izo ndi mtima wanga wonse. Ine sindimakhulupirira...mochuluka bwanji momwe iwo amatsimikizira izo mwasayansi kapena china chirichonse. Iwo apanga zotsimikizira zasayansi zambiri zimene iwo ankayenera kuzibwezera mmbuyo. Mulungu anati dziko linayima...dzuwa. Ndikutanthauza kuti dzuwa linayima mmalo mwa dziko. Mwaona, dzuwa. Ine kwenikweni sindimakhulupirira dzuwa... Ine—ine—ine sindimakhulupirira kuti dzuwa limachita chimene iwo amati limachita. Ine ndikudziwa kuti mwezi umayenda, ndipo ndimakhulupirira kuti—dzuwa limayenda nalonso. Mukuona?

<sup>421</sup> Koma ena a iwo amati, “Iye anayang’ana pa umbuli wa Yoswa, mwaona, ndi” anati “Iye anayimitsa a...anati...” Chabwino, iye anati, “Iye anayimitsa dziko.”

<sup>422</sup> Ine ndinati, “Ndiye inu munandiuza ine, ‘Ngati a—ngati dziko likanayima konse, ilo likanangogwewera ngati nyenyezi yamlengalenga.’ Mukuona?” Ine ndinati, “Kenako, chinachitika ndi chiyani ndiye?”

<sup>423</sup> Ine ndimayankhula kwa Bambo Thiess kumusi uku, mphunzitsi wa Baibulo ku sekondare sukulu; inu mukudziwa amene iye anali, koma iye ananena izo. Ine ndinati, “Ine ndikukhulupirira izo zimene Baibulo linanena, kuti dziko linayima...” Ine ndinati, “Ine ndikutanthauza, ‘dzuwa linayima.’ Yoswa ananena kwa dzuwa: ‘Ima nji!’ ndipo ilo linayima pamenepo.”

<sup>424</sup> Iye anati, “Chabwino, Iye anangoyimitsa dziko, Iye anawona umbuli wa Yoswa.”

Ine ndinati, “Inu muzichita zomwezo mwa luntha lanu, ndiye.” Mukuona?

<sup>425</sup> [M’bale akuti, “Ndikukhulupirira kuti iwo akhoza kutsimikizira mwasayansi kuti ndi nthawi yayitali bwanji imene—dzuwa linayima.”—Mkonzi]. Inde, apo iwo...Ine ndazimvapo zimenezo, inenso. Inde, iwo amati...Ine ndinamumva wam’bwebwe kuno nthawi yina yapitayo akuyankhula pa izo, kuti iwo akanakhoza kutsimikizira izo. Ndipo pa nthawi yomweyo imene iwo...chinachake chinachitika mumlengalenga chimene iwo anakhoza kuchiwona kumene chinachake chinachitika Kumwamba ndipo chinatsegula Nyanja Yofiira pa nthawi imeneyo ndi chinthu. Iwo anatsimikizira zonsezo. Chabwino, mnyamata, ine ndikukuuzani inu, nyenyezi zochokera kutali kwinakwake zomwe zinachita chinachake chonga icho pa nthawi imeneyo. Komabe, izi ndi zozama kwambiri kwa ife.

<sup>426</sup> Chotero, tsopano, chifukwa chimene Uthenga uwu... Uthenga uwu ukuyenera kudzayang’anidwa motere, kutsimikizira kuti iwo uli. Tsopano, ife tikudziwa, abale,

kuti munthu sangakhale Mulungu. Munthu, komabe iye ndi mulungu, aliyense wa inu ndi mulungu. Inu munapangidwa kukhala mulungu, koma osati pamene inu muli mu moyo uno. Mukuona? Yesu anali munthu monga ife tiri, koma Mulungu anali mwa Iye. Chidzalo cha Mulungu chinali mwa Iye; ife tiri ndi Mzimu mwa muyeso.

<sup>427</sup> Koma pokhala kuti Kuwala uku kwabwera, ndipo ngati Iko kuli Kuwala koono kumene kuti kudzalengeze Uthenga umene Yohane M'batizi ankawutsogolera, monga Iye ananena kuti iye anachita pa mtsinje kumusi uko. . . Ndipo tangoyang'anani, izo zikanakhala bwanji—icho chikanakhala bwanji china? Tayang'anani pa ine, taonani, opanda ngakhale maphunziro a sukulu ya galamala. Pamene Iye anandiuza ine zinthu zimene zikanadzachitika, palibe chimodzi cha izo chimene chinalephera. Palibe chimodzi cha izo chimene chinayamba chalepherapo. Taonani zimene Iye wachita. Taonani, Iye ali ndi. . .

<sup>428</sup> Ndipo ine ndinawauza abale, mmbuyo zaka zapitazo, ine sindikudziwa amene akanakhala wamkulu kwambiri pakati pathu, koma ndinawauza iwo za zinthu izi, za kuwona Kuwala uku ndi mtundu wanji Iko kunali, ndi chirichonse. Tsopano chithunzi chikusonyeza kuti izo ndi zoono. Zinthu zosiyanasiyana zonsezi zikutsimikizira kukhala zoono. Ndi zoono zimenezo? Chabwino, ndiye, ngati izo ziri zoono. . . Ndipo uko ndiko Kuwalako.

<sup>429</sup> Tsopano, yambirani pafupifupi foro. . . [Malo opanda kanthu pa tepi—Mkonzi.] . . pamwamba pa ndime ya 35 apo, kapena ine ndikutanthauza. . . Tiyeni tiyambire pafupifupi ndime ya 14, m'bale. Watsegula iyo ndi ndani? Chabwino. Yambirani pafupifupi ndime ya 14 ya mutu wa 3 wa Luka Woyera pamene. [M'bale akuwerenga Luka 3:14-16.]

*[Ndipo asilikari chimodzimidzi anamufunsa iye, anati, Ndipo ife tichite chiyani? Ndipo iye anati kwa iwo, Musachite chiwawa kwa munthu, kapena kuyimba mlandu wina mwabodza; ndipo mukhale okhutira ndi malipiro anu.]*

*[Ndipo pamene anthu anali kuyembekezera, ndipo anthu onse anasinkhasinkha mmitima yawo za Yohane, ngati iye anali Khristu, kapena ayi;]*

*[Yohane anayankha, kunena kwa iwo onse, ine ndithudi ndikubatzani inu ndi madzi; koma wina wamphamvu kuposa ine akudza, ndipo zingwe za nsapato zake sindiyenera kuzimasula: iye adzakubatzani inu ndi Mzimu Woyera ndi moto:]*

<sup>430</sup> Chabwino. Icho chinali chiyani? Anthu anali pansu pa ziyembekezo zotero za Mesiya kuti awonekera, pamene iwo anawona utumiki wodzozedwa wawukulu uwo, wa munthu

wochokera mchipululu ndi kukhala ndi msonkhano wake ndi kubwerera ku chipululu, anthu ambiri, amene anali otsatira ake omwe, anati, “Iye ndi Mesiya.” Iwo ankayembekezera izo, mwaona.

<sup>431</sup> Ndiye ngati uwu uli Uthenga woona wa Mulungu ukutsogolera Kudza, kwa Yohane M’batizi, momwemonso... monga chinthu chomwecho, Uthenga wa Eliya, iwo ukuyenera kuganiziridwa mwanjira yomweyo. Mukuona? Kotero izo zikuyankha funso limenelo, ine ndikuganiza, ndendende. Mukuona? Izo zikuyenera kuganiziridwa mwanjira yomweyo. Mukuona?

<sup>432</sup> [M’bale akufunsa, “Kodi pali chirichonse chimene ife tiri ndi uundo wochita kuti tiyesere kumuthandiza aliyense amene anga—angatenge a—mu mkangano ngati umenewo? Kapena ife tingatani?”—Mkonzi]. Apo sipangakhale kanthu, palibe chimene inu mungachite. [“Malingaliro otayika... Kodi zimenezo zikhoza kukhala maganizo otayika?”] Chabwino, izo zingabwere ku malingaliro otayika ngati zingafike ku izi: ngati munthuyo, amene izo zimanenedwa, akanachitira umboni kuti iye anali Mesiya, ndiye ife tikudziwa kuti iye akanakhala khristu wabodza. Mukuona?

<sup>433</sup> Mwaona, bola ngati munthuyo mwiniwake akanati agwire malo ake, inu mwaona. Monga iwo anamuza Yohane, Yohane sana... Izo sizikunena kanthu pamenepo za iye akunena chirichonse za iwo. Iwo anali—iwo anali—anthuwo, a—Akhristu okondeka amene... kapena okhulupirira amene ankakhulupirira pa Yohane.

<sup>434</sup> Iwo anati, “Munthu uyu moona ndi mneneri wa Mulungu, palibe kukayika.” Iwo anati, “Kodi—kodi—kodi—kodi—kodi iwe si Mneneri ameneyo?”

Iye anati, “Ayi.”

<sup>435</sup> Iye anati, “Bwanji, kodi—kodi—kodi iwe si Mesiya?” Mwaona, iwo—iwo ankaganiza kuti iye analidi. Mukuona?

Iye anati, “Ayi.” Mukuona?

“Kodi—kodi—kodi si inu? Ndani—inu ndi ndani?”

Iye anati, “Ine ndi liwu la iye wofuula m’chipululu.”

<sup>436</sup> Ndipo kenako Baibulo linati, “Anthuwo ali pansu pa kuyembekezera.” Anali ndani ameneyo? Omvetsera ake, omvera ake, otsatira ake, abale ake. Mukuona? Tsopano, iwo sanafune kumupweteka iye, iwo sankayesera kuti amupweteke iye. Koma, onani, iwo—iwo ankaganiza kwenikweni mmitima yawo kuti iye anali Mesiya.

<sup>437</sup> Chabwino, tsopano, mbiriyakale imayenera kudziwewereza yokha pa chochitika chirichonse. Iye tikudziwa zimenezo. Ikuyenera kudziwewereza yokha.

438 Monga inu munatengera uko mu Mateyu 3, iyo inati, “Kuti chikakwaniritsidwe, chonedwa ndi mneneri, ‘Kuchokera ku Igupto ine ndamuyitana mwana wanga.’” Tsopano, izo sizinali. . . Izo zinkakamba za Yesu, Mwana; koma tsatirani zolozera; anali Yakobo, mwana, nayenso. Mukuona? Mukuona? Izo zonse ziri ndi tanthauzo lapawiri.

439 Chotero tsopano ngati izo. . . ngati—ngati chinthucho sichinawuke, ine ndinganenebe kuti icho chinali choti mtsogolomu chidzauka, chifukwa ine ndikudziwa kuti Uthenga uwu umachokera kwa Mulungu ndipo ndi kutsogolera kwa Khristu, ndipo ndi Mzimu ndi mphamvu ya Eliya chifukwa iwo ndi woti udzabwezeretsa mitima ya ana. Chirichonse ndendende chimatsimikizira zimenezo, kotero icho chikuyenera kupangidwa kukhala chinthu choterocho pansu pa anthu owona, kuti—ndizo mwamtheradi kukhulupirira ndi abale anu ndi abwenzi.

440 Tsopano, ine ndakhala. . . Ndiri ndi dokotala komwe kuno mtauni. Ndikhoza kukuuzani inu za dokotala. . . Sindikuuuzani inu kuti iye ndi ndani, mzanga amene anayika manja ake mondikumbatira ine, ndipo anati, “Billy, izo zingakhale zophweka kuti ndinene kwa iwe, ‘iwe ndi Mesiya wa tsiku lomaliza wa Mulungu.’” Mukuona?

Ine ndinati, “Doc, usachite zimenezo.”

441 Iye anati, “Chabwino, sindikumuwona aliyense padziko lapansi amene anayamba wakhlapo ndi chinthu ndi kunena zinthu ndi kuchita zinthu zomwe iwe umachita, Billy.” Izo zamuthandiza iye kwambiri, mwaona. Iye anati, “Ine ndimapita ku matchalitchi awa ndi kuwawona alaliki awa ndi zinthu,” iye anati, “ndiwe wosiyana ndi iwo ndipo ndikudziwa kuti iwe ulibe maphunziro.” Mukuona? “Ndipo ine ndikudziwa kuti iwe si wowerenga maganizo, chifukwa iwe. . . kuwerenga maganizo sikungachite zinthu zimenezo.” Mukuona?

Ndipo ine ndinati, “Izo nzoona, Doc.”

442 Palibe chifukwa choyankhula naye chifukwa iye sakudziwa nkomwe, simukanafika naye pa maziko oyambirira, mwaona, chifukwa iye samadziwa choti achite. Koma ndi zimenezo, mwaona.

443 Ine ndikumudziwa mkazi wachikuda amene amakhala kuntunda mu kanjira pafupi ndi ine, ndipo iye amagwira ntchito kwa mwamuna wina yemwe ine ndikumudziwa, ndipo mkazi wa mwamuna uyu anayimba, anati, “Mkazi ameneyo adzakupembedzani mwamtheradi ngati mulungu, chifukwa iye ankafa ndi khansa ndipo inu munayika manja pa mkazi ameneyo ndipo munati iye anali. . .” Mkazi uyu amene iye amamugwirira ntchito, mwamuna wake ndi dokotala wina uyu (osati dokotala amene ine ndimamukamba, dokotala wina) amasewera gofu ndi zinthu pamodzi, ndipo iye anali atamusiya iye. Ndipo uyo anali

wantchito wapakhomo wa mzake, ndipo anali atamulephera iye kuti afa, ndipo iye anachiritsidwa mwamtheradi. Ndipo adokotala sanathe ngakhale kupeza kotsalira kake, ka khansa. Ndipo, mwaona, iye akanati. . .

<sup>444</sup> Tsopano, iwo sakutanthauza izo mu kuwala kumene ine ndikuganiza kuti iwo amazinena izo kapena ife timazitengera izo mkati. Mukuona? Iwo amatanthauza kuti iwo—iwo. . . Iwo amatanthauza kuti amakhulupirira kuti Mulungu ali nafe, mwa ife, akugwira ntchito kudzera mwa ife; osati kuti munthu payekha ndi Mulungu, inu mwaona. Tsopano, iwo ankadziwa kuti Yohane anali munthu chabe.

<sup>445</sup> Ndi momwemonso Yesu anali munthu. Yesu anali munthu chabe, Iye anangobadwa mwa mkazi, ankayenera kufa. Nkulondola uko? Iye anali munthu, ankayenera azidya ndi kumwa, ndipo ankamva njala, ankalira, ndi kuchita ludzu, ndi chirichonse, monga munthu basi monga inu muliri, monga munthu monga ine ndiri. Koma Mzimu wa Mulungu unali mwa Iye mu chidzalo, wopanda muyeso. Iye anali wamphamvuzonse mu mphamvu.

<sup>446</sup> Pamene, Eliya anali gawo chabe la Mzimu umenewo; mwina wodzozedwa pang'ono pamwamba pa abale ake, koma iye anali gawo chabe la Mzimu. Koma anthu ankayembekezera Mesiya. Ndipo iwo anawona gawo ili pamwamba pa abale awo, iwo anati, "Oh, mai, uyu akuyenera kukhala Iye!"

<sup>447</sup> Koma pamene Iye anayamba kuwala, kuwala kwakung'ono kwa Yohane kunazima. Mukuona?

<sup>448</sup> Ndipo kuwala kwakung'ono uku kudzazima pamene Iye adzabwera, Khristu wamkulu wodzozedwa uja wa Kumwamba akubwera kuchokera kummawa kupita kumadzulo. Ndipo a. . . a. . . Mukuona? Koma Iye sadzakhala pa dziko lapansi tsopano, Mesiya sadzakhala pa dziko lapansi kufikira Zakachikwi zitayambika. Mukuona? Mukuona? Chifukwa Mpingo, "tidzakwatulidwa pamodzi kukakomana ndi Ambuye mu mlengalenga." Iye sadzabwera pa dziko lapansi. Iye akutengera Mkwatibwi Wake kutali.

<sup>449</sup> Iye akutenga makwerero, inu mukudziwa, monga. . . Kodi sewero lija linali chiyani, Leo, pamene bambo anayika makwerero pambali pa nyumbayo? Romeo ndi Juliet. Ndiko kulondola, anayika makwerero ndipo anamuba mkwatibwi wake.

<sup>450</sup> Tsopano Iye akungotsika kumene pa makwerero a Yakobo, ndipo akuti, "Psst, Wokondedwa, bwera kuno." Mwaona, ife tikupita kukakomana ndi Iye.

<sup>451</sup> [Mbale akufunsa, "Mbale Branham, kodi izi zingakhale zolondola ndiye ndi izo? Anthu awa anabwera kwa Yohane M'batizi ndipo ankafuna kumutcha iye Mesiya. Ndipo ine ndinakumvani inu nthawi ina mukunena kuti Myuda amaganiza

kuti Mesiya anali Mulungu.”—Mkonzi]. Mukuti chiyani? [“Ine ndikuti, anthu awa anabwera kwa Yohane M’batizi, kumaganiza kuti iye anali Mesiya, Khristu. Ine ndinakumvani inu mukunena nthawi ina kuti Mesiya adzakhala Mulungu, kwa Myuda.”] Inde, bwana. Uko nkulondola, “rabbi.”

<sup>452</sup> [M’bale akuti, “Chabwino, Yohane anawadzudzula iwo, kunena kuti iye ‘sanali,’ Khristu ameneyo anali nkudza.”—Mkonzi]. Uko nkulondola. [“Koma kodi si zoonza kuti ophunzirawo anamutcha Yesu ‘Ambuye’? Ndipo Yesu anavomereza zimenezo, akuti, ‘Inu mumanditcha Ine “Ambuye,” ndipo kotero ine ndiri.”] Eya. [“Mu—mu Yohane 13, pamene Iye anasamba. . . ? . . .”] Eya, Iye akanavomereza zimenezo. [“Monga kukhala Ambuye, inde, Iye anavomereza izo.”] Iye anavomereza zimenezo. [“Iye anavomereza zimenezo.”] Uh—huh. Koma, onani, Yesu pokhala *Ambuye*, pamene Iye anafunsidwa ngati Iye anali, Iye anati, “Inde, bwana. Ine ndi Ambuye wanu ndi Mbuye. Inu mwanditcha Ine icho, ndipo inu mwanena bwino, pakuti Ine ndiri chomwecho.” Koma. . . [“Koma sipanayambe pakhala pali munthu wina amene anga, amene. . .”] akhoza kunena zimenezo. Ayi.

<sup>453</sup> Monga ngati izo. . . Ngati wina anganene kuti ine ndinali mulungu, chabwino, ndiroleni ine ndikuuzeni inu mu Dzina la Ambuye Yesu kuti “Kumeneko ndi kulakwitsa!” Mukuona? Ndine wochimwa wopulumutsidwa mwa chisomo, ndi Uthenga *wochokera* kwa Mulungu. Mukuona? Mukuona?

**124. Kodi kapena kodi mpingo wamba ukuyenera uzisamalira ake omwe, ake—ake omwe (akeake) owathandizira asanayambe kusamalira zosowa zakunja mmadera ena? Komabe, iwo uta. . . wake. . . Iwo utakwaniritisa zosowa zake, izo ndi za Mwamalemba kuti mpingo uzithandizira pa ntchito ya umishonare pamene iwo uli ndi kuthekera?**

<sup>454</sup> Eya. Kulondola. Chikondi chimayambira kunyumba, inu mwaona. Ife—ife—ife timasamalira zosowa zathu zomwe kuno, chifukwa ife tikana. . . uwu ndi mpingo wa Mulungu, kapena konse, mpingo wanu wawung’ono, mpingo wa Mulungu. Tsopano, ngati inu simungathe ngakhale kuwalipira abusa anu, inu simungathe kupeza mabukhu a nyimbo ndi zinthu, inu simukuyenera kumatumiza izo kwina. Mukuona? Komano inu mukawulipira mpingo wanu, ndi chirichonse, ngongole zanu zonse ndi chirichonse, zitakonzedwa ndi zokonzeka ndi kumapitirira, ndiye muthandizeni m’bale winayo amene akusowa thandizo laling’ono kunjira uko, inu mwaona. Pezani pang’ono. . .

<sup>455</sup> Ine ndikukhulupirira, pamene. . . ngati mukupanga malipiro pa mpingo wanu ine ndingakhalenso ndi thumba laling’ono lokhazikitsidwa kwinakwake ku chopereka cha umishonare ngati anthu amamverera kuti akufuna kupereka ku umishonare.

Chifukwa anthu ambiri amapereka ku umishonare pamene iwo sapereka ku mipingo yakwawo ndi zinthu. Chotero ngati iwo sapereka ku umishonare, iwo amazigwiritsa ntchito pazinthu zina. Kotero ine ndinganene kuti mungokhala ndi kabokosi kakang’ono ka umishonare, ndipo ine ndi . . . Umo ndi momwe ife timayesera kuchita.

**125. Luka 1:17, chonde tafotokozani kubwera kwa Yohane mu “mzimu wa Eliya.”**

<sup>456</sup> Chabwino, ine ndikuganiza kuti tinangopeza Luka—Luka 1:17, uh-huh, akubwera mu “mzimu wa Eliya.”

<sup>457</sup> [M’bale akufunsa, “Kodi pamenepo ndi pamene okhulupirira kubadwanso mu thupi lina amapeza chiphunzitso chawo?”—Mkonzi]. Pepani? [“Kodi pamenepo ndi pamene anthu amene amakhulupirira kuti munthu amabadwanso mu thupi lina amayambira chiphunzitso chawo?”] Zikuyenera kuteru. [“Mwaona, iwo amakhulupirira kuti iye amabwereranso mu . . .”] Inde. [“. . . iye amabwereranso ndi thupi lina] Inde, onani, ndi zooni kuti mzimu sumafa. Uko nkulondola. Mulungu amatenga munthu Wake koma osati Mzimu Wake. [“Iwo amati, ‘Ngati iwe wakhala ukuchita bwino udzabwereranso mu—mwa munthu wina wabwino.’”] Eya. Eya. [“Ngati wakhala uli woyipa iwe ukhoza kudzabwerera mwa galu.”] Eya, iwo adzatero . . . Eya.

<sup>458</sup> Chabwino, tsopano, monga uko mu—mu—uko mu India, izo zinani mu gulu la amuna kumene ife tinakomana monga chonchi, ndipo iwo ama—iwo amangokolopa pansu; kuponda nyerere zazing’ono kapena chinachake, iyo imatha kukhala wachibale kapena chinachake. Mwaona, iwo sangachite zimenezo. Koma, inu mwaona, izo ndi—izo ndi zachikunja. Mukuona? Icho ndi chikunja. Izo ndi zooni.

**126. Paulo anati kwa . . . Paulo anati kuti “Zikhumbani moona mtima mphatso zabwino, ndipo komabe ndikuwonetsani inu njira yopambana kwambiri.” Chonde tafotokozani chimene “njira yopambana kwambiri” ili.**

<sup>459</sup> Chikondi, Akorinto Woyamba 13, mwaona. “Zikhumbani . . .” Pezani Woyamba . . . Tsopano pezani Akorinto Woyamba 13 pamenepo, m’bale. Akorinto Woyamba, mutu wa 13, ndipo tsopano mungowerenga ndime zitatu kapena zinayi zotsiriza za iyo. Akorinto Woyamba 13, zotsiriza . . . pafupifupi ndime zitatu zotsiriza za mutuwo—za mut- . . . [M’bale akuwelenga Akorinto Woyamba 13:11–13—Mkonzi].

*[Pamene ndinali mwana, ndinkalankhula ngati mwana, ndinkamvetsa ngati mwana, ndinkaganiza ngati mwana: koma pamene ndinakhala mwamuna, ndinasiya zinthu zachimwana.]*

*[Pakuti tsopano ife tikuwona kupyolera mu kalilole, mwamdima; koma pamenepo maso ndi maso: tsopano*



*ine ndikudziwa mwa gawo; koma ine ndidzaziwa ngakhale monga ine . . . inenso ndikudziwika.]*

*[Ndipo tsopano pali chikhulupiriro, chiyembekezo, chikondi, zitatu izi; koma chachikulu mwa izi ndi chikondi.]*

Uh-huh, chikondi, mukuona?

**127. Kodi m'bale azitsutsidwa chotani amene kufooka kwake ndi kwakuti amafuna atakhala ndi udindo mu tchalitchi wopanda kufunsidwa kuti atero?**

Oh, mai! Chabwino, muzipirira naye iye, ine ndikuganiza. Mukuona?

**Kodi M'bale azitsutsidwa chotani. . . (Iye sakuyenera azitsutsidwa!) . . . amene—amene kufooka kwake ndi kuti akhale ndi udindo mu tchalitchi popanda kufunsidwa kuti atero?**

<sup>460</sup> Mwachitsanzo, ngati iye amafuna ku—kukhala dikoni. Mukuona? Ndipo iye sanafunsidwe kuti atero, komabe iye akufuna kuti akhale dikoni mulimonse, mwaona. Chabwino, ngati munthu ali monga choncho, inu mukudziwa kuti pali chinachake chaching'ono, inu mukudziwa, chofooka penapake, mulimonse, ndipo koteru ndimangochita ndi iye mwachikondi.

<sup>461</sup> Ndipo, chifukwa, inu simufuna ku—kuchita chinthu chonga chimenecho pokhapokha ngati mukudziwa kwenikweni. Muziyika mwamuna wanu wofunikirayo amene mungathe mu bodi yanu, inu mwaona, monga choncho. M'bale, musamayike kalikonse mmenemo kamene . . . Muzimuyesa munthu ameneyo, choyamba. Dikoni amakhala ndi udindo wochulukuka kuposa umene m'busa amakhala nawo. Iye akuyenera kukhala wopanda banga, dikoni amatero. Mukuona?

**128. Pa msonkhano wa mgonero, munthu wina anabwera ku guwa kudzapemphera. M'bale Branham anali atayima kumbuyo kwa—zipangizo za mgonero pamene iwo ankatumikiridwa, iye anati iye “sakanawasiya iwo kuti azipemphera ndi munthuyo ali pa guwa.” Chonde tafotokozani.**

<sup>462</sup> Ine ndinatumiza wotheadizira, inu mwaona, M'bale Neville. Ine ndikukumbukira usiku umene izo zinachitika. Ine ndikuyenera kukhala ndi gome la mgonero limenelo, mwaona, ngakhale pamene . . . Yang'anani apa. Tsopano, ine ndiribe nthawi yoti ndilowe mu izi. Winawake wakhala apa amene anafunsa, ndithudi. Ichi ndi chimene icho chiri, m'bale. Pamene—pamene inu mulandira mgonero, icho ndi choyimira thupi la Yesu Khristu. Icho chikhoza kukhala . . . Chikuyenera kuyang'aniridwa nthawi zonse.

<sup>463</sup> Penyani, pamene Eliya ananena kwa—kwa Gehazi, “Tenga ndodo yanga” (iye anali atayidalitsa ndodo imeneyo), iye

anati, “pita panjira yako. Ndipo ngati wina akuyankhula, usamuyankhe. Ngati wina akupatsa moni, usambwezere moni. Zipita, ndipo ukayike ndodo iyo pa mwanayo.” Nkulondola uko? “Ukhale ndi ndodo imeneyo!” Mukuona? Ndipo icho ndi chimene ine ndinkachita.

<sup>464</sup> Tsopano, ngati pakanati pasakhale m’busa wothandizira pano, atayima pamenepo. . . Ndinali nditatsiriza kulalikira. Ine ndikukumbukira pamene izo zinali. Ndipo ine. . . ngati iwo. . . M’bale Neville akanapanda kuyima pano, kapena winawake kuti amuthandize munthu ameneyo pa guwa. . . Ine ndinali nditangomaliza kulalikira, kotero ine ndinali nditayima pa gome la mgonero. Ndipo pamene iwo anakonzekera kudya mgonero, ndipo ine ndinali kale mu—mu kupereka mgonero. M’bale Neville anali atangoyima pambali, ndipo ine ndinkapereka mgonero. Tsopano, M’bale Neville anali atayima pamenepo.

<sup>465</sup> Bwanji ngati iwo akanabwera ku guwa ndipo M’bale Neville anali akadali mu ulaliki wake, ndipo iye nkumalalikira? Ine ndikanapita ku guwa ndi munthuyo, ngati iye akanati atuluke mu msonkhano pamene iye amalalikira, kupita mmwamba ku guwa. Ndinakawona m’bale wanga ali. . .kuti anali ndi kudzodza kwa Mzimu. Iye anali akutumikira. Iye anali mtumiki mu mpingo. . . iye anali mu mzere wa ntchito, mtumiki mu mzere wa ntchito.

<sup>466</sup> Ndipo inu musamawalole iwo kuti aziyankhula ndi malirime, kumusokoneza, kapena mwanjira iliyonse, mtumiki mu mzere wa ntchito. Komabe, ngati Mzimu Woyera ukuyankhula kwa winawake ndipo iwo akuthamangira ku guwa kuti akapulumsidwe, mulole mtumikiyo apitirize ntchito yake; mulole m’busa, dikoni, wothandizira, ngati pali wothandizira kapena mtumiki wina aliyense, muloleni iye apite kwa munthu ameneyo mwamsanga kwenikweni. Ndipo musamuvutitse mtumikiyo pa ntchito yake. Mukuona?

<sup>467</sup> Ndipo ine ndinali nditayima kuseri kwa desiki mu mzere wa ntchito, ndikupereka mgonero. Ndipo wothandizira wanga, M’bale Neville, anali atayima pafupi ndi ine. Ndipo mwamuna anathamangira ku guwa, ine ndinati, “Pezani, pitani kwa iye, M’bale Neville.” Ndipo M’bale Neville anapita kwa iye. Ndicho chifukwa ine sindinapite.

<sup>468</sup> Tsopano, ngati pakanati pasakhale wothandizana naye pano, kapena palibe wina amene akanapita kwa mwamunayo, ine ndikanachokapo ndi kuyimitsa mgonero, ndi kupita panso ndi—ndi kuwona kuti moyo umenewo wapulumutsidwa. Inu mukuona? Koma pokhala kuti panali wina woti ndimutumize, izo zikanandichotsa ine pa mzere wa ntchito, inu mwaona, kumene ine ndimapereka mgonero.

**129. Ndi zonse ziti zimene munthu angachite. . . Ndi zonse ziti zimene munthu angachite ngati wogwira ntchito ndi anthu**

**pakuchita ndi munthu amene akufuna Mzimu Woyera, ndi kukhala Mwamalemba?**

469 Chabwino. Mungopitiriza kubwereza Mawu kwa iye, ndicho chinthu chabwino kwambiri choti muchite. Mawu ali ndi Kuwala. Mungonena, “M’bale, Yesu analonjeza Izo. Kumbukirani, ndi lonjezo Lake.”

470 Musamugwedeze iye, kumukankha iye, kapena kumusuntha iye mozungulira, kapena chinachake. Musayesere basi ku—ku...ayi, musayesere kupereka Izo kwa iye, chifukwa inu simungachite izo. Mukuona? Mukuona? Inu...Mulungu adzapereka Iwo kwa iye. Inu musingopitirira kubwereza malonjezowo. Mukuona? Pitirizani kuyima pamenepo mukubwereza lonjezolo. “Mulungu Kumwamba, ine ndikumupempherera m’bale wanga. Lonjezo lanu ndi loti Inu mudzamupatsa iye Mzimu Woyera.”

471 Ndiye ngati inu mukuyesera kumulimbikitsa iye...Iye akuti, “Oh, m’bale, m’busa, m’bale,” aliyense amene ali pafupi naye, “Ine—ine ndikufuna Mzimu Woyera.”

472 “M’bale, Ilo ndi lonjezo. Mulungu anapanga lonjezo. Kodi inu mukukhulupirira kuti Iye analonjeza? Tsopano, musati mukayikire Izo. Ngati inu mukukhulupirira lonjezo, Mzimu Woyera udzabwera kwa inu pa mphindi iliyonse tsopano. Khalani mukuziyembekezera Izo. Perekani chirichonse chimene muli nacho kwa Iye, ndi kuti, ‘Ambuye, ndayima pa lonjezo lanu.’”

473 Tsopano, pitirizani kubwereza. Tsopano, pangani lanu—lanu—lanu—phunziro lanu, mwaona, kumupangitsa iye kuti asiye...Pitirizani kubwereza. Nenani tsopano, “Inu mumuwuze Mulungu. Tsopano, kodi inu munalapa?”

“Inde.”

474 “Tsopano nenani, ‘Ambuye, Inu munati ngati ine ndilapa Inu mudzangondikhululukira ine. Inu munati ngati ndilapa ndi kubatizidwa mu Dzina la Yesu Khristu kuloza ku chikhululukiro cha machimo anga, ine ndidzalandira Mzimu Woyera. Tsopano, Ambuye, ine ndachita zimenezo. Ine ndachita zimenezo, Ambuye. Ine ndachita zimenezo. Ine ndikuyembekezera, Ambuye. Inu munalonjeza zimenezo.’”

475 Mwaona, imeneyo ndi njira yake, mungopitiriza kumulimbikitsa iye. Musungeni iye pa Mawu. Ngati Iwo uti ubwere Iwo udzabwera ndiye.

**130. Kodi mlaliki kapena Mkhristu aliyense amachita bwino amene sakhulupirira mu...Ayi: Kodi mlaliki kapena Mkhristu aliyense amachita bwino amene sakhulupirira mu chitetezo Chamuyaya?**

476 Tsopano, tiyeni tiwone. Ine ndikuganiza “...kuchita...” Taonani ngati inu mukuwerenga izo mofanana ndi ine.

Werengani izo. [M'bale akuwerenga funso, “Kodi mlaliki kapena Mkhristu aliyense akuchita bwino amene sakhulupirira chitetezo Chamuyaya?”—Mkonzi].

Ndimaganiza kuti ndinali nalo ilo molondola. Tsopano, chabwino, ine . . .

**Kodi mlaliki akuchita bwino amene sakhulupirira chitetezo Chamuyaya?**

<sup>477</sup> Ine ndikanakhulupirira kuti mlalikiyo anali kuchita . . . ngati iye samadziwa kalikonse za chitetezo Chamuyaya. Koma ngati iye anachidziwa icho ndi kudziwa icho kuti ndi Choonadi, ndiyeno nkusachilalikira Ichu, iye akuyenera kudzichitira manyazi yekha; ndiko kulondola, kapena Mkhristu aliyense. Tsopano, Mkhristu, tsopano, ine ndinganene kwa—kwa Mkristu yemwe samamvetsetsa izo kwambiri . . .

<sup>478</sup> [M'bale akufunsa, “Chimenecho si chiphunzitso chotseguka, kodi chiri, M'bale Branham, kuti chilalikiidwe kwa anthu amene sanayambepo . . .?”—Mkonzi]. Ayi, ayi, ayi. Tsopano, ndicho chimene ine ndinali kufikako. Inde. Mukuona? Mukuona?

<sup>479</sup> Tsopano, inu mukukumbukira zomwe ine ndinanena Lamlungu latha? Ngati inu muli mlaliki, dzipezereni guwa. Ngati inu simuli, khalani ndi ulaliki wanu. Mwaona, ndiyo njira yabwino yochitira izo, kukhala ulaliki wanu. Ngati muli mlaliki, tengani guwa, mwaona, ndipo kupita kukalalikira. Ngati inu simuli, mungokhalira ulaliki wanu, lolani moyo wanu ukhale guwa lanu. Mukuona? Ndikuganiza izo zimasamala zambiri, inu simutero? Mukuona? Mukuona? Chifukwa nthawi zambiri ife timapeza . . . Ndipo inu abale mumachita zimenezo mmipingo mwanu.

<sup>480</sup> Kumbukirani, anthu wamba nthawi zina amayesa kufotokoza zinthu ndi kuchita zinthu, ndi bwino kuwalangiza kuti asachite izo. Ndipo ngati wina akufuna kudziwa chinachake, aloleni iwo abwere kwa mmodzi wa a . . . amene wauzidwa kuti achite izo. Mukuona?

<sup>481</sup> Nenani, chabwino, tsopano, monga wina anganene, “Heyi, ine ndikuuzani . . . Iwo amandiuza ine, inu ku mpingo wanu mumakhulupirira mu chitetezero Chamuyaya.”

<sup>482</sup> Tsopano, inu kulibwino muyang'ane. Inu mwinamwake mudzalowa mu chisokonezeko chachikulu kuposa chimene inu munayamba mwakhalamo, inu mwaona, ndi kumupanga iye kukhala woyipa kuposa kale. Nenani, “Ine ndikuuzani inu chiyani, ngati inu mungabwere ndi kudzawafunsa abusa athu, mwaona. Inu—inu mupite mukalankhule nawo iwo, mwaona. Ife . . . Izo ndi zoono, ine ndikudziwa abusa athu amakhulupirira zimenezo. Ine ndimakhulupiriranso izo, koma sindingathe kuthandizira . . . Ine si mlaliki. Ine ndimangokhulupirira izo, ndizo zonse zomwe ine ndikudziwa. Ine ndimakhulupirira izo chifukwa ine ndinamumva iye akufotokoza izo kuchokera

mu Baibulo, kuti izo zinali mopanda mthunzi wa kukaikira kulikonse kwa ine.” Mukuona?

<sup>483</sup> Koma kulibwino kuwalola—kulibwino kuwalola anthu ayankhule kwa abusa za izo. Ndipo, abusa, khalani otsimikiza kuti iye akudziwa momwe angayankhire izo, nawonso. Kotero muwerenge izo mwabwino kwenikweni, chifukwa nthawi zambiri iwo amakumangilirani inu mu izo, inu mwaona. Chimene. . .

<sup>484</sup> [M’bale akuti, “M’bale Branham?”—Mkonzi.] Mundikhululukire ine. [“Ine ndi wokhudzika mu kudziwa pang’ono, koma ine—ine ndikudziwa mayitanidwe anga ndipo ndapanga kusankha kwanga kotsimikizika.”] Uh-huh. [“Inu mwangonena kuti ‘Ngati ndinu mlaliki, mukuyenera kukhala ndi guwa.’”] Inde, bwana. Uko nkulondola. [“Ine si mlaliki, ndine mvangeri.”] Inde bwana. [“Koma guwa la aliynse ndi langa.”] uko nkulondola. [“Koma pakali pano ndikugwira ntchito, ntchito yakuthupi. Si ntchito yovuta, koma ndikugwira ntchito, ndipo ndiliba guwa. Ndipo ine ndikukhulupirira kuti nthawi iyi ya ntchito imene ine ndirimo ili mu chifuniro cha Ambuye. Iye wandiiza ine kuti ndichite iyo, kupyolera mu Mawu ndi umboni wa Mzimu. Ndipo ine ndikukhulupirira, kenako, kuti maguwa adzakhala otseguka.”] Ndithudi, uko nkulondola. [“Ndi kulondola uko?”] Uko nkulondola, m’bale.

<sup>485</sup> M’bale, tsopano, ngati inu mungabwerere kuno ndi kukatenga buku lakale la mpingo, inu mukapeza kuti ine ndinachita ubusa mpingo uwu zaka seventini, ndipo ndinkalalikira tsiku lililonse, ndinkalalikira tsiku lililonse ndi kugwira ntchito tsiku lililonse. Mukuona? [M’bale akuti, “Ngati mukugwira ntchito, ndi chizindikiro chabwino kuti *mwayitanidwa*.”—Mkonzi.] Eya. Paulo anatero, sichoncho iye? Paulo ankamanga mahema. [“Ndikhoza kukhala wokhumudwa chifukwa, monga momwe inu munanenera, ngati ine ndiri mlaliki, ndikuyenera kukhala ndi guwa. Ine ndi. . .Ndikhoza kukhala wokhumudwa, koma ndikudziwa kuti Mulungu anandiyitana kuti ndipeze ntchito, kwa kanthawi.”] Ndithudi. Paulo anapita kukamanga mahema, sichoncho iye? Anagwira ntchito ndi manja ake kuti asachite. . .Ndizo ndendende. Ndithudi. [“Eya, oh, chabwino, ndi pamene ine ndinazipeza izo, kuchokera kwa Paulo.”] Hmm. Uko nkulondola. Mukuona? John Wesley anati, “Dziko lapansi ndi parish yanga.” Kotero guwa lanu likadali lotseguka, m’bale. Avangeri amapita ku dziko lonse lapansi. Si kulondola uko? “Pitani inu ku dziko lonse lapansi.” Kotero guwa lanu ndi dziko lonse lapansi. Inde, bwana.

Funso:

**131. Kodi ndi kulamula, k-u-l-a-m-u-l- . . . Kodi ndi kulamula kuti dikoni kapena trastii ayenera kukhala mu**

**chiphunzitso cha mpingo wawo?** Inde. Uko nkulondola. **Kodi ndizololedwa kwa iwo kuti awonjezere kapena kuchotsa ziphunzitsozo chifukwa cha maganizo awo kapena vumbulutso?** Ayi, bwana. Ayi.

<sup>486</sup> Dikoni kapena trastii akuyenera kugwirizana mwangwiro ndi a—ndi chiphunzitso cha mpingo wawo. Iwo akuyenera kukhala mwangwiro ndi kutanthauzira kwa Malemba a mpingo wawo, chifukwa, ngati iwo satero, iwo akumenyana ndi chinthu chomwecho. Iwo—iwo akudzipweteka okha. Mukuona? Inu mukulimbana . . .

<sup>487</sup> Ndi, kunena kwina, monga ngati—ngati—ngati ndingati ine ndimalikonda banja langa ndi kuyesera kuwadyetsa iwo poyizoni. Mwaona, chinthu chomwecho. Mwaona, inu simungachite izo, inu . . .

<sup>488</sup> A—a trastii kapena dikoni potenga udindo wawo, kapena waudindo aliyense wa mpingo amene amayimira gulu lina la mpingo, mwaona, amene amayimira mpingo.

<sup>489</sup> Chimenecho ndi chifukwa chimene ine ndinachoka mu mpingo wa Baptisti, mwaona, kwa nthawi yoyamba yomwe. Ine ndinali nditangokhala mmenemo pang’ono ndipo iwo—iwo anandipempha ine kuti ndidzodze alaliki aakazi. Chabwino, ine sindikanatha kwenikweni kukhala mmenemo. Ine ndinati, “Ine—ine ndikukana kuchita izo.”

<sup>490</sup> Ndipo abusa anandigwedeza ine. “Ichi ndi chiyani? Iwe ndi mkulu wa mpingo!”

<sup>491</sup> Ine ndinati, “Dokotala Davis, mwa ulemu wonse ku chikhulupiro cha Baptisti, ndi chirichonse chimene ine ndinadzodzedwerako, ine sindimadziwa kuti izo zinali mu chiphunzitso cha mpingo wa Baptisti kudzodza akazi. Ichochinali chinthu chimodzi chimene chinasiyidwa kwa iwo.”

Ndipo iye anati, “Chimenecho ndi chiphunzitso cha mpingo uwu.”

<sup>492</sup> Ine ndinati, “Bwana, kodi mungandikhulukire ine usikuuno, kapena mungandiyankhe mafunso ena?” Mukuona?

<sup>493</sup> Iye anati, “Ine ndiyankha mafunso ako.” Anati, “Ndi ntchito yako kukhala pamene?”

<sup>494</sup> Ine ndinati, “Ndi choncho, bwana. Uko nkulondola. Ine ndikuyenera kuyembekezera mu chirichonse chimene mpingo uwu umachita. Ine ndiri mu mzere wa ntchito, m’modzi wa akulu apa malowo.” Ndipo iye anati . . . Ine ndinati, “Kodi inu mungandifotokozere ine chifukwa chimene mu Akorinto Woyamba 14 kapena 15 apo, pamene Paulo anati, ‘Akazi anu akhale chete mmipingo, sikololedwa kwa iwo kuti aziyankhula.’”

<sup>495</sup> Ndipo iye anati, “Bwanji, ndithudi!” Iye anati, “Ngati . . . Ine ndikhoza kuyankha zimenezo.” Iye anati, “Inu mwaona, chimene icho chinali,” anati, “Paulo anati . . . Onse—akazi onse

anali atakhala kumbuyo mmakona, kumalongolola monga iwo amachitira nthawi zambiri. Iye anati, ‘Musamawalole iwo kuti azichita zimenezo.’ Mukuona?”

<sup>496</sup> Ndipo ine ndinati, “Ndiye fotokozani Timoteo Wachiwiri kwa ine, pamene Paulo anati, nayenso, mlembi yemweyo, mtumwi yemweyo, anati, ‘Ine sindikulola mkazi kuti aziphunzitsa kapena kutenga ulamuliro uliwonse, mwaona, koma ku—kukhala mu kumvera. Pakuti Adamu anayamba kupangidwa, ndipo kenako Eva, ndipo Adamu sananyengedwe, koma mkaziyo pokhala kuti ananyengedwa.’ Iye ndi wonyengedwa. Tsopano, sindikunena kuti iye akufuna kuchita chirichonse cholakwika, koma kwenikweni iye wanyengedwa mmenemo. Iye sakuyenera kukhala mphunzitsi.”

Iye anati, “Kodi limenelo ndi lingaliro lanu?”

<sup>497</sup> Ien ndinati, “Limenelo ndi lingaliro la Lemba ku njira yanga yowonera izo. Ndicho chimene Baibulo linanena.”

<sup>498</sup> Iye anati, “Mnyamata, iwe ukhoza kulandidwa layisensi yako chifukwa cha zimenezo.”

<sup>499</sup> Ine ndinati, “Ine ndingowapeputsa iwo vutolo. Ine ndingoyipereka iyo, Dokotala Davis.” Ine ndinati, “Osati kunyoza kulikonse kwa inu. . .” Ndipo iye sakanachita izo, ngakhale. Iye anzilola izo zipite, anzilola izo zipite monga choncho.

<sup>500</sup> Kenako iye anandiiza ine kuti adzapanga mtsutso wapoyera ndi ine pa izo. Ndipo ine ndinati, “Chabwino, nthawi iliyonse basi.” Koma iye—iye sanachite izo.

<sup>501</sup> Kotero ndiye a—kanthawi kena pang’ono, ndiye, pamene Ambuye anayankhula kwa ine, ndi zokhudza a—Mngelo wa Ambuye anabwera, ndiye—ndiye iye anangoziserewula Izo, inu mwaona. Ndipo kenako ine—ine ndinangomuza iye, ine ndinati, “Chabwino, Dokotala Davis, kulibwino kuti ndisiyane ndi ichi pakali pano, mwaona,” ine ndinati, “chifukwa icho chikhala cholemetsa. Ine ndangodzozedwa pang’ono, mulimonse, kotero icho chikhala cholemetsa kwa ine, kotero ine ndikhoza kungosiya izo pakali pano.”

<sup>502</sup> Kotero choncho ngati ine sindikhala mu mpingo wa Baptisti ndi kuphunzitsa chiphunzitso cha Baptisti ndi kutenga chikhulupiriro cha Baptisti. Ngati ine ndingachite izo—ngati ine ndingachite izo chifukwa chakuti iwo unali mpingo, ndiye ine ndikulakwitsa, mwaona, ine ndikubisa chinachake. Ndipo ngati ine—ngati ine—ngati ine ndiri woonamtima ndi inemwini, ine ndipita kwa anthu Achibaptisti (abusa anga kapena aliynse amene angafotokoze izo kwa ine) ndi kuwapempha iwo a—mawu a Moyo; ngati iye angandiwonetse ine molondola pamene izo ziri mu Lemba, ndi kukhutitsa kumverera kwanga, ndiye ine ndiziyankhula izo basi momwe iwo amayankhulira izo, mwaona, ndipo ine ndidzakhala wa Baptisti.

503 Chimenecho ndi chifukwa ine ndiri wodziimira pandekha. Chimenecho ndi chifukwa ine sindiri wa mabungwe, chifukwa ine sindimakhulupirira mu mabungwe. Ndipo ine ndimakhulupirira kuti izo si zamalemba, bungwe.

504 Choncho, ine sindikanakhala wa bungwe lililonse ndi kumverera olungama pochita zimenezo. Mukuona? Chotero, ine sindimawatenga anthu ndi kuwapanga iwo mamembala, ndi zina zotero monga choncho, chifukwa ine ndimakhulupirira ife *timabadwa* kuti tikhale mamembala, ife tinabadwira mu Mpingo wa Mulungu wamoyo. Mukuona?

505 Ife sitimachotsa mayina a anthu mu bukhu ndi kuwachotsa iwo, ndi chirichonse monga choncho, chifukwa ine ndimakhulupirira kuti izo siziri mwa zathu—ntchito zathu kuti tizichita zimenezo. Ine ndikukhulupirira kuti ndi Mulungu amene amachita kuchotsako. Mukuona? Koma ine ndimakhulupirira kuti mpingo, ngati pakanakhala m'bale amene amachita chinachake cholakwika . . .

506 Mwachitsanzo, ngati—ngati iwo anamugwira M'bale Neville, kapena M'bale Junior, kapena M'bale . . . m'bale wina pano, mmodzi wa madikoni kapena matrastii, kapena chinachake chimzake, akuchita chinachake cholakwika, Ine ndikukhulupirira chinthu choti muchite ndi chakuti mpingo usonkhane pamodzi ndi kumupempherera m'bale uyu. Ngati iye sakuwongokabe, mulole awiri apite ndi iye, apite kwa m'baleyo kuti akayanjanitsidwe. Ndipo ngati ndiye ngati iye salandira izo, ndiye mukanene izo pamaso pa mpingo. Ndiye ngati iwo salandira izo, imeneyo ndi nthawi ya mpingo wonse ndiye, mwaona, izo ndi za abusa, akulu, ndi china chirichonse kuti achite izo. Ine sindimakhulupirira kuti bodi ya madikoni iliyonse ili ndi ufulu womuponyera aliyense kunjwa kwa mpingo kapena bodi ya matrastii iliyonse kapena m'busa aliyense ali ndi ufulu wochita izo.

507 Ine ndikuganiza kuti ngati aliyense akanati achotsedwe, zikanakhala chifukwa cha makhalidwe oyipa, kapena chinachake chonga icho, kuti iye sanali munthu woyenerera, ngati mwamuna kubwera kuno kumayipitsa atsikana athu kapena—kapena kunyoza akazi athu, ndi zinthu monga izo, ndipo kumadzinenerabe kuti ndi mmodzi wa ife pano. Mukuona? Tsopano, ngati iye ali kunjwa kwinakwake akubwera mkati, bwanji, ife tikuyenera kuchita chinachake za izo, koma, pamene izo zifika kwa munthu woteroyo, munthu wamakhalidwe oyipa akuyesera kupanga chikondi kwa akazi athu kapena—kapena kunyoza ana athu aakazi kapena, inu mukudziwa, chinachake chimzake monga icho, kapena kuchita chinachake chopanda makhalidwe momuzungulira iye, kapena kuwatengera anyamata athu aang'ono kunjwa ndi kuwapanga iwo opotozedwa, kapena chinachake.



508 Zinthu zimenezo zikuyenera kuti zitengedwepo, ndipo kenako munthu ameneyo achotsedwe mu chiyanjano ndipo asaloledwe kutenga nawo mgonero, chifukwa ife sitikuyenera kuchita zimenezo. Ife sitiri. “Ngati wina adya mosayenera, ndi wolakwira Magazi ndi thupi la Ambuye,” pa munthu ameneyo.

509 Koma ndimakhulupirira monga momwe munthu angati, “Chabwino, tsopano, iye—iye ndi *ichi, icho*.” Mupemphereni iye. Kulondola.

510 Ine sindidzayiwala konse, mu Stockholm, Sweden, M’bale Lewi Pethrus, munthu wamkulu wa Mulungu. Ife tinali titakhala pa tebulo, maora ochepa okha tisanabwerere ku Amerika. Ife tinali ndi misonkhano yopambana kumeneko. Ndipo iye anati, Gordon Lindsay anati, “Ndani amene ali woyang’anira gulu lalikulu limeneli?” Mnyamata, ilo lagonjetsa Assemblies of God ndi mahandirede a mailosi, inu mwaona. Anati, “Woyang’anira ndi ndani?”

Ndipo Lewi Pethrus ndi ngati njonda, ndipo iye anati, “Yesu.”

Iye anati, “Atsogoleri anu ndi ndani?”

Iye anati, “Yesu.”

511 Iye anati, “Ine ndikudziwa kuti uko nkulondola,” anati, “ife timakhulupirira chinthu chomwecho za Assemblies of God yathu.” Iye anati, “Uko nkulondola.” “Koma,” anati, “tinene, mwachitsanzo, a—m’bale akachoka pamzere,” anati, “ndi ndani ali ndi chonena kuti amuchotsa iye?”

Anati, “Ife sitimamuchotsa iye.”

“Chabwino,” anati, “inu mumachita chiyani?”

512 Anati, “Ife timamupempherera iye.” Ine ndinaganiza kuti izo zinali zokoma kwambiri! Izi zinamveka ngati Chikhristu kwa ine, “Ife timamupempherera iye.” Palibe amene amamuchotsa iye, iwo amamupempherera iye.

513 Anati, “Chabwino, ndiye, nanga bwanji ngati abale ena atagwirizana,” iye anati, “ndipo ena a iwo sakufunanso kuyanjana naye? Kumubweretsa iye mkati, ngati ndi m’busa, inu mwaona, amene wayamba kukhala mwamuna wa madona pakati pa . . . Inu mukudziwa chimene ine ndikutanthauza, ndi zinthu monga choncho, ndipo ena a abusa sangakhale ndi iye mu mipingo yawo. Kodi inu nonse mumachita chiyani, kumuchotsa iye mu bungwe lanu?”

514 “Ayi.” Anati, “Timangomusiya yekha ndi kumamupempherera iye.” Anati, “Sitinatayepo mmodzi panobe. Iwo nthawizonse amabwerera, mwanjira yina.”

515 Iye anati, “Chabwino,” anati, “tsopano, bwanji ngati . . .” Anati, “Nanga bwanji ngati ena atanena kuti akumufuna iye ndipo ena sakumufuna iye? Tsopano, nanga bwanji zimenezo?”

516 Anati, “Chabwino, iwo amene akumufuna iye, amutenge iye; iwo amene sakumufuna iye, sakuyenera kutero.”

517 Kotero—kotero ine ndikuganiza iyo ndi njira yabwino yokhalira ndi izo, sichoncho inu, abale? Ndipo mwanjira imeneyo ife ndi “abale.”

518 Tsopano, abale, ine ndikuyembekeza kuti zinthu izi zapereka mtundu wina wa kuwonetsera kwakung’ono ku yankho kapena chinachake, kuti msonkhano wathu pano usikuuno wa—watipindulira ife chinachake. Ine ndikukonzekera kuti ndichoke tsopano kwa kanthawi, kupita ku misonkhano Kumadzulo. Ine modzichepetsa ndikukhumba mapemphero anu.

519 Ena a mayankho anga muno, mwinamwake ambiri a iwo, mwinamwake palibe limodzi la iwo, anali olondola. Ine sindikudziwa. Koma icho chikanakhala chopambana chimene ine ndikanakhoza kusonkhanitsa mwa njira yangayanga ya kuganiza, inu mwaona, kuti ndiyesere kuzifotokoza Izo. Mwinamwake otsiriza awa, makamaka, abwera mmenemo komalizira, ndinalibe nthawi yowayang’ana iwo. Ndipo ine basi sindina, iwo anali. . . Chimene ine ndikutanthauza, iwo anali Malemba amene ife timadutsamo nthawi iliyonse, tsiku ndi tsiku mu mpingo. Ine ndinaganiza kuti mwina chikanakhala chinthu china cholemetsa kwambiri chimene chingatipangitse ife kuti tifike pansu kuti tipite kwenikweni ku chinthu china chachikulu, koma izo zangokhala ngati mafunso a mipingo.

520 Ndine wokondwa kukuwonani mukugwiritsitsa monga choncho, palibe chisokonezo chirichonse, palibe kusakhutitsidwa kulikonse, palibe chisokonezo chirichonse. Palibe funso linatsutsa Iwo ndipo linati “Iwo ndiwolakwika, Iwo ndi olakwika, ife sitikhala ndi Iwo.” Iwo anali abale okha amene amafuna kudziwa chinachake choti chilimbitse kugwira kwawo, ndizo zonse. Kuti . . . kuzilimbitsa, kumanga—kumanga zidazo mothina pang’ono, kukokera mphako yina mmenemo. Ine ndikuyembekeza kuti ife tidzikomana nthawi zambiri monga chonchi, kukokera zida.

521 Ndipo inu muzikumbukira, abale, zida zanga zikufunika kukokedwa, nazonse. Kotero inu mundipempherere kwa Mulungu kuti Mulungu andithandize ine ndi kukoka zida zanga molimba pang’ono, kuti ine ndi. . . musakhale omasuka kwambiri ndi zinthu. Ndipo moyo umene ine ndimakhala ndi zinthu zimene ine ndimachita, mulole ine ndizichita izo ndi mzimu wochuluka wa kudzichepetsa, wofunitsitsa kwambiri kuti ndizichita izo. Ndipo Mulungu andipatse ine mtima woti ndichite izo kuposa momwe ine ndinkachitira kale. Ine ndikupempherera chinthu chomwecho kwa inu nonse. Mulungu akudalitseni inu.

522 Ine ndakusungani pano nthawi yayitali, ndipo pakali pano patsala maminiti faifi kuti ikwane leveni.

523 Ndipo tsopano, M'bale Neville, ine—ine ndikhoza... Tsopano, ine ndinapeza, ndi pafupifupi mailosi naini handiredede ndi chakuti okha kumeneko, ine sindinyamuka mpaka Lolemba mmawa. Koma ine ndikufuna kudzakhala kuno Lamlungu ku Sande sukulu, ine ndidzabwera ngati mlendo wanu kudzamvetsera kwa inu mukulalikira, inu mwaona, Lamlungu. Mukuona? Koma... Chabwino, m'bale, inde, m'bale. M'bale Neville, chifukwa chake ndi ichi, m'bale. Ine ndi... Ine ndimakukondani inu ndipo mwakhala woganizira kwambiri popereka guwa basi monga ngati... monga ine ndinali mkulu wampingo wamkulu kwa inu, kapena chinachake. Koma ine sindinayambe ndamvererapo mwanjira imeneyo, M'bale Neville. Ine ndimamverera kuti ndife abale.

524 M'bale Ruddell ndi M'bale Junie, ndi, oh, abale inu nonse ndi nonse a inu, ife ndi—ife ndi abale basi pamodzi, inu mwaona.

525 Koma chiyani... Chifukwa chake, ine ndangosasa mawu pang'ono tsopano, inu mwaona, ndipo ine ndiri ndi masabata sikisi olunjika a nkondo yosalekeza, inu mwaona. Ndipo ine—ine ndikungofuna kuti mwina ndiyambe ngati ine ndingathe, ndimagaganiza, ukatha msonkhano uwu usikuuno, izo zindipatsa ine Lachisanu ndi Loweruka ndi Lamlungu kuti ndipume, ine ndisanayambe misonkhano kunjira uko.

526 Ndipo M'bale Junie, mwamsanga ine ndikadzabwerera, nthawi yina ndikadzabwera, ine ndikuyenera kubwera kuno ndi kudzakuwonani inu kachiwiri, ndikufuna kudzabwera. Ine ndinadutsa mpingo wanu wawung'ono kunjira uko, dzulo, ine ndikukhulupirira. Mkazi wanga anati, "Ine ndikuganiza uwo..." Kodi iwo uli kunjira uko mmbali mwa njanji pafupi ndi Glenellen Park? Ndikufuna kudzabwera kumeneko ndi kuyankhula ndi anthu aku Sellersburg amenewo. Chabwino.

527 M'bale Ruddell, adalitse mtima wanu. Ndikufuna kudzabwera, inu muli ndi gulu labwino la anthu. Inu munakhala pamenepo usikuuno mukumvetsera basi monga inu munali mkulu wachikulire mukuzitengera izo mkati.

528 M'bale Beeler pamenepo, ndi mmodzi wa abale athu a uvangeri. Ine ndikuyembekeza nthawiyina ine ndikhoza kudzakumana ndi umodzi wa misonkhano yanu kwinakwake, m'bale, zikhoza kuchita chikoka china, kukhala ndi chinachake chonena kuti chikulimbikitseni inu. Ine nthawizonse ndakhala ndi mawu abwino kwa inu kwa aliyense, inu ndi kwa M'bale Stricker pano, ndi avangeri.

529 M'bale Collins pano, amene ine ndikukhulupirira tsiku lina adzakhala mtumiki wa nthawizonse mu ntchitoyi.

530 Mwamuna amene ali wolimba mtima, mwamuna wolimba mtima, mwamuna weniweni wachikhulupiriro, Mulungu akhale ndi inu nonse, ndi inu madikoni, inu matrastii, inu abale.

531 Ine ndikukhulupirira inu muli. . . M'bale pano, sindingathe kuliganizira dzina lake. Inu ndi. . . [M'bale Caldwell akuti, "M'bale Caldwell."—Mkonzi.] Caldwell. Ndinu basi. . . Ndinu mmodzi wa akulu kapena chinachake, sichoncho inu, kapena basi. . . ["Mtumiki."] Mtumiki. ["Ndine mtumiki. Ine ndinali wa Mpingo wa Mulungu, ine sindikanatha kumalalikira Uthenga wathunthu ndi kukhala ndi iwo. Ine sindikanatha kumalalikira ubatizo mu Dzina la Ambuye Yesu ndi kukhala ndi iwo. Ndinali ndi layisensi ya utumiki yapamwamba kwambiri imene iwo anayichotsa, koma ndinangowasiya iwo. Kuchokera pamene ine ndinakumvani inu mukulalikira Mauthenga aakulu awo, ine ndinawasiya iwo, kutuluka mu bungwe. Tsopano ndikufuna kukhala mmodzi wa inu."]

532 Zikomo inu, m'bale. Ife takulandirani inu ku chiyanjano chathu. Ndipo zathu—zoyeneriza zathu ndi za zakumwamba. Moyo wathu umapanga zoyeneriza zathu, inu mwaona. Zimenezo ndi zoyeneriza zathu. "Ngati Ine sindichita ntchito ku Atate Anga, ndiye musandikhulupirire Ine." Mukuona? Uko nkulondola. Ndizo zoyeneriza zathu. Ndipo monga wakale. . . Monga Howard Cadle anakonda kunena, "Ife tiribe lamulo koma Chikondi, tiribe bukhu koma Baibulo, ndipo—ndipo tiribe—tiribe kachikhulupiriro koma Khristu." Uko nkulondola. "Tiribe lamulo koma Chikondi, kachikhulupiriro koma Khristu, bukhu koma Baibulo."

533 Ndipo ife tiri—ife, M'bale Caldwell, ndife okondwa kukhala nanu. Inu munatuluka mu bungwe lalikulu. Anderson Church of God, ine ndikuganiza. [M'bale Caldwell akuti, "The Cleveland."—Mkonzi.] Kapena mpingo wa Cleveland, Pentecostal Church of God. ["Ndipo ine ndinali m'busa kunjira kuno ku. . . ? . . ."] Oh, inde. Oh, inde, ine ndakhala ndiri kumeneko. Ine ndikukhulupirira ine ndinali kunjira uko ndi M'bale Neville. . . kapena M'bale Wood, nthawi yina, ife tinapeza galu kapena galu wosakira kwa winawake amene ankapita ku tchalitchi chanu kunjira uko. Ndipo ine ndinayima pa masitepe kunjira uko ndi kumayankhula, ndipo iwo ankapamba za inu. Chabwino, ine ndikutsimikiza. . . ["Ku mpingo wanga."] Oh? ["Burns."] Ndiko kulondola, M'bale Burns. Ndiko kulondola [M'bale Caldwell akufotokoza chochitika.] Oh? Inde. Oh, Bertha, ndiko kulondola. Oh, izo ndizopambana.

534 M'bale Rook apo, iye ndi m'busa tsopano, kapena mvangeri, ine ndikukhulupirira. Ndi kulondola uko? Kapena kodi mukuchita ubusa? [M'bale Rook akuti, "Mvangeri chabe."—Mkonzi.] Mvangeri. Ine ndikufuna kuti ndikuchitireni ndemanga inu, M'bale Rook. Ndamva za ntchito yina yayikulu imene inu mukuwachitira Ambuye. Inu. . . Ine ndinamva kuti inu munapita ku Indianapolis kapena mumapita ku Indianapolis, ndipo munali ndi misonkhano ndipo munapindulira miyoyo kwa Khristu. Mulungu akhale nanu, M'bale Rook. Ndine wokondwa

ndithudi kukuwonani inu. Ine ndinakuwonani inu kunja kuno pa thirakitala yakale iyi kunja kuno, mukuthamanga mozungulira kuno, mukungothira feteleza bwalo lanu kunja uko. Chabwino, kukuwonani inu kunja mukuyesera kuwachitira Ambuye chinachake. Ndine wokondwa kuti Iye anakuyitanirani inu ku utumiki, nthawizonse muzimugwira Iye pamaso panu, m'bale. Mulungu akudalitseni inu. Musalekerere pa chirichonse; koma kuchite icho ndi mzimu wokoma kwambiri womwe inu mungathe kuchita nawo. Mulole wanu—mulole uthenga wanu nthawizonse ukhale wokometsedwa ndi kukoma kwa Mzimu Woyera.

535 Ndi M'bale Stricker... [M'bale akuti, "Ife tikufuna mapemphero a inu nonse. Ife ti—ife tikuyesera kuti tiyambitse mpingo ku North Vernon."—Mkonzi.] Oh, ine ndikuyembekeza inu mukhala nawo iwo. Ife tikupemphererani inu. ["Tikuchita bwino kwambiri, mpaka pano."] Uko nkulondola.

Billy, iwe uyamba liti kuchita ubusa?

536 Dokotala Goad ndi Dokotala Mercier pano, ine—ine—ine ndikuyembekezera... monga ife timatchulana wina ndi mzake zimenezo. Ndipo M'bale Goad wafika pa malo mpaka ine... iye kwenikweni akuyenera kukhala ndi udindo, iye amatha kuyika zipolopolo tsopano. Eya. Ndipo, M'bale Leo, ine ndikukhulupirira ife tikhoza kungomulola iye kuti apitirire ndi izo monga choncho, ndi kumutchula iye... mulole iye apitilize udindo wake wa—wa "Dokotala."

537 Chabwino, "Dokotala" Branham, kumbuyo uko, inu mungomusunga iye dokotala bwino kwenikweni, ndipo nyali zikuyaka mwabwino kwenikweni. Ndipo—ndipo ine ndikuuzani inu chiyani, nthawi iliyonse tikakhala ndi msonkhano wapadera ndimayankhula ndi bodi ndi kuwona ngati iwo sangakupatseni inu zowonjezera pang'ono pa zimenezo [M'bale Branham akuseka—Mkonzi.], chifukwa cha ntchito yapadera pamene inu mumayenera kuchita kusesa mochuluka ndi kunyamula mkati ndi kunja, ndipo izo zidzakusangalatsani inu.

538 Dokotala Wood. Ine ndamutchula iye "Dokotala," ndikuganiza kuti mukudabwa chifukwa chake. Ine sindikumutchula iye molakwika, iye amawaza nkhuhi zonse mu zidutswa, inu mukudziwa. Ambuye amameretsa mtengo wokongola, ndipo iye amawudula iwo ndi kumanga nyumba kuchokera mwa iwo. Ine sindinaziwonepo zoterozo, kotero ndikuyenera kumutchula ife "Dokotala."

539 M'bale Taylor, inu mukadali wokhulupirika pakhomo, kumupatsa munthu pokhala. Ine ndimaganiza za inu monga chonchi, "Ine kulibwino ndikhale chopondera pakhomo pa nyumba ya Ambuye kuposa kukhala mmahema ndi oyipa." Ndiko kulondola, bwana.

<sup>540</sup> M'bale Hickerson, inu mwangoyamba mu Njirayi, ndipo chokwera, mukubwera motsatira. Ine ndimayamikira kwanu . . . ine . . . Inu munayamba mu Njira, ndipo mukubwera motsatira, Ine ndithudi ndikuyamikira kuwona mtima kwanu ndi zonse zimene inu mukuwachitira Ambuye Yesu. Mulungu akudalitseni nthawizonse ndi kukupangani inu dikoni woona, m'bale, chimene ine ndikhulupirira inu muli, nyumba yanu yomvera ndi zinthu zonse monga inu mwakhala muli.

<sup>541</sup> M'bale Fred, inu simunakhale nafe motalika kwambiri, kubwera kuchokera ku Canada. Sitikumverera kuti ndinu waku Canada panonso, tikumverera kuti ndinu mwendamnjira ndi mlendo limodzi nafe, m'bale wathu, ngati trastii. Inu ndi M'bale Wood, ndi inu amene mumatumikira udindo wanu mwabwino ndi M'bale Roberson, ndi ena onse a iwo; M'bale Egan, iye sali pano usikuuno.

<sup>542</sup> Ndipo M'bale Roberson, inu mwakhala a—a thandizo lenileni kwa ine, M'bale Roberson pamodzi ndi ena, pa mlandu wa msonkho uwu umene unadutsa mu kufufuzidwa uku. 🐦

61-0112 Mafunso Ndi Mayankho  
Branham Tabernacle  
Jeffersonville, Indiana U.S.A.

CHICHEWA

©2025 VGR, ALL RIGHTS RESERVED

VOICE OF GOD RECORDINGS, MALAWI OFFICE  
P.O. BOX 51453, LIMBE, MALAWI

VOICE OF GOD RECORDINGS  
P.O. BOX 950, JEFFERSONVILLE, INDIANA 47131 U.S.A.  
[www.branham.org](http://www.branham.org)

## Chidziwitso kwa ofuna kusindikiza

Maufulu onse ndi osungidwa. Bukhu ili mukhoza ku printa kunyumba kwanu ngati mutafuna kuti mugwiritse ntchito inuyo kapena kuti mukawapatse ena, ulere, ngati chida chofalitsira Uthenga wa Yesu Khristu. Bukhu ili simungathe kuligulitsa, kulichulukitsa kuti akhalepo ambiri, kuikidwa pa intaneti, kukaliika pakuti ena azitengapo, kumasuliridwa mu zinenero zina, kapena kugwiritsidwa ntchito ngati njira yopezera ndalama popanda chilolezo chochita kulembedwa ndi a Voice Of God Recordings®.

Ngati mukufuna kuti mumve zambiri kapena ngati mukufuna zipangizo zina zimene tiri nazo, chonde mulembere ku:

VOICE OF GOD RECORDINGS, MALAWI OFFICE  
P.O. Box 51453, LIMBE, MALAWI

VOICE OF GOD RECORDINGS  
P.O. Box 950, JEFFERSONVILLE, INDIANA 47131 U.S.A.  
[www.branham.org](http://www.branham.org)